TWO PARTS OF
FAIZAN-E-SUNNAT,
V 3

# MAKHALIDWE ABWINO A KUYANKHULA



Machimo okwana 80 pa 100 aliense (80%) amachitika chifukwa cha lilime

Nfundo zenizeni za Sayyiduna Luqman Hakeem

Momwe mungayezere mawu anu musanayankhule

Nkhani 25 zopewera kuyankhula kopanda phindu


Shaykh-e-Tareeqat, Ameer-e-Ahl-e-Sunnat
Woyambitsa wa Dawat-e-Islami, Allamah Maulana Abu Bilal
MUHAMMAD ILYAS
ATTAR QADIRI RAZAVI



**Lamasuliridwa m'Chichewa ndi:**
Nthambi Yomasulira (Dawat-e-Islami)

## Mfundo zofunika Kukumbukira

Onetsani mfundo zosiyanasiyana powerenga bukuli paliponse pamene pali kufunikira. Lembani mutu ndikuyika nambala yatsamba m'magawo omwe ali pansipa. Maphunziro anu adzawonjezereka, إِنْ شَآءَاللّٰه.

| Mutu | Tsamba | Mutu | Tsamba |
|---|---|---|---|
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |

| Mutu | Tsamba | Mutu | Tsamba |
|---|---|---|---|
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |

(۱) گفتگو کے آداب

(۲) فضول باتوں سے بچنے کی فضیلت

(1) Guftugu kay aadab

(2) Fuzool Baaton say bachnay ki fazeelat

# (1) Miyambo ya pokambirana

# (2) Kupambana kopewa kuyankhula zopanda pake

*Magawo awiri a Faizan-e-Sunnat, buku 3*

Shaykh-e-Tareeqat, Ameer-e-Ahl-e-Sunnat,
Muyambitsi wa bungwe la Dawat-e-Islami, 'Allamah Maulana Abu Bilal

Muhammad Ilyas Attar
Qaadiri Razavi دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَه

Lamasuliridwa mu Chichewa ndi

Nthambi Yomasulira (Dawat-e-Islami)

Kumasulira n'chichewa kwa

(1) Guftugu kay aadab (2) Fuzool Baton say bachnay ki fazeelat

**MWAUMWINI ONSE NDI OTETEZEDWA**

© 2022 Maktaba-tul-Madinah

Palibe gawo lililonse la kusindikiza uku lomwe litha kutulutsidwa, kapena kutumizidwa, m'mawonekedwe aliwonse kapena mwanjira iliyonse, zamagetsi, zamakina, kujambula, kujambula mu mawu kapena mwanjira ina iliyonse, popanda chilolezo cholembedwa ndi Maktaba-tul-Madinah.

| | |
|---|---|
| **Kusindikizidwa koyamba:** | Safar-ul-Muzaffar, 1444 AH (September, 2022) |
| **Latanthauziridwa ndi:** | Nthambi Yomasulira **(Dawat-e-Islami)** |
| **Wosindikiza:** | **Maktaba-tul-Madinah** |
| **Kuchuluka:** | |

**Thandizo**

Chonde khalani omasuka kulumikizana nafe ngati mukufuna kuthandiza pa kusindikiza kwa buku lililonse la chipembedzo kapena kabuku pofuna kutumiza Sawab kwa achibale anu omwe anamwalira.

## Maktaba-tul-Madinah

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah – Mahallah Saudagran, Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

 Imelo: maktabaglobal@dawateislami.net – maktaba@dawateislami.net
**Foni:** +92-21-34921389-93

 **Webusayiti:** www.dawateislami.net



www.dawateislami.net

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الْمُرْسَلِيْنَ
اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ ؕ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ ؕ

# *Du'a Powerenga Buku*

Werengani Du'a iyi (pempho) musanawerenge buku lachipembedzo kapena musanayambe phunziro la chisilamu, mudzakumbukira china chilichonse mwaphunzira, اِنْ شَآءَاللّٰه:

اَللّٰهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَانْشُرْ
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْاِكْرَام

## Kumasulira

*O Allah عَزَّوَجَلَّ! Titsegulireni makomo a maphunziro ndi luntha, ndipo tichitireni chisoni! E inu omwe muli wolemekezeka kwambiri komanso waulemerero!*

*(Al-Mustatraf, buku. 1, tsamba. 40)*

**Chidziwitso:**

Mufunireni zabwino Mtumiki Omaliza صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَسَلَّم kamodzi musanayambe komanso kumapeto kwa Du'a.



www.dawateislami.net

# M’ndandanda wa zopezekamo


*Du’a Powerenga Buku* v

MIYAMBO YA POKAMBIRANA 1

Ubwino womufunira zabwino Nabi ﷺ 1

Kuletsa kukweza mawu pamene tikuyankhula 1

Kuyankhula motsitsa mawu ndi Sunnah 2

Okhulupirira milungu yambiri achiluya ankaona ngati kuyankhula mokweza mawu ndi chithu chonyaditsa 2

N’chifukwa chiyani bulu amalira? 2

Kuyetsemula mokweza ndi zonyansanso 2

Yang’anani ndi nkhope yanu molunjika alendo 3

Mwambo uyenera kukhala oti kukambirana kukhale komveka 4

Zoyankhula za Mtumiki Woyera ﷺ zinkakhala zofewa 4

Mtumiki Woyera ﷺ ankabwereza mfundo katatu 4

Kukambirana kwa Mustafa ﷺ 5

Nduna imene inkagwiritsa mawu ovuta (nthabwala) 5

Zithu ziwiri zimene zidzawalowetse ku moto anthu ambiri 6

Ndindani adzakakhale ku Paradiso? 6

Chitsimikizo cha Paradiso 6

80 peresenti ya machimo imapangidwa ndi lilime 7

Pempho la ziwalo zonse za thupi kwa lilime 7

I’tikaf ya Pagulu imakhala njira yozisinthira 8

Nyumba zowonekera mkati ku Paradiso 9

Zoyankhula zabwino ndi chopereka 9

Zimatanthauza chiyani akamati chopereka? 10

Itanirani ku zabwino mwachangu 10




www.dawateislami.net

Munthu wa makhalidwe abwino adzayandika ndi Mtumiki ﷺ 10
Makhalidwe abwino ndi atiwo? 10
Chithu choopsa kwambiri 11
Makutu ali ngati galasi ndipo zoyankhula zopanda pake zili ngati miyala 11
Lilime lilibe fupa komano limapangitsa mafupa kusweka 11
Kumutchula wina wake kuti bulu kapena nkhumba 12
Kumutchula Msilamu ndi dzina loyipa ndi tchimo 12
Angelo amatumiza themberero 13
Yankhulani zoona ngakhale ndi ana 13
Kutchulidwa kodalitsika kwa Sayyiduna Abdullah Bin Aamir 14
Tengani chuma ndi nyumba zonse ziwiri(Nkhani) 14
Momwe munthu osamvera makolo anasinthira? 15
Kuwakhazika ana mtima pansi ndi bodza 16
Tsatirani njira yosamala yowakhazikira mtima pansi 16
Ntchito za munthu amene amateteza lilime lake, zimakhalanso zotetezeka 17
Kusasangalala kwa Mtumiki Woyera ﷺ ndi munthu amene amanama pozitenga ngati nthabwala 17
Kugwera pansi pa Gahena 17
Anthu anthabwala ayenera kumvetsera 18
Lamulo la masewero anthabwala 18
Ntchito yokhudzana ndi dziko likubwera iyenera kupangidwa mwachangu 19
Kuyankhula kwabwino kumachita kuchokera kwa Mulungu ndipo.... 19
Tetezani mawu 20
Anthu ena alinso ndi malilime 20
Mulibe zabwino m'mawu amenewo 20
Pezani malipiro powayitana anthu ena mwaubwino 20
Kunena Labbaik poyankha kuyitana kwa munthu wina 20
Munthu amene amangopanga nthabwala amataya mbiri yabwino 21
Chifukwa chimodzi chimene chimayambitsa udani 22
Nthabwala zimayambitsa udani 22
Tanthauzo la machimo akuluakulu 22



www.dawateislami.net

Tanthauzo la kudzigomera 23
Ntchito zabwino za zaka 70 zinawonongeka 23
Mlandu waukulu kwambiri kuposa tchimo 24
Kufotokozera kofunikira kokhudzana ndi kudzigomera 24
Machiritso otsimikizirika a kudzigomera 25
Zithu 8 zoyambitsa kuzigomera komanso machiritso a kudzigomera 26
M'nyamata wochita zoyipa anayamba kusintha 27
Zoyankhula zinayi za Mtumiki Woyera ﷺ zokhudza mawu onyansa 28
Lilime loyipa ndi matenda oopsa 29
M'maonekedwe a galu 29
Tanthauzo la mawu onyansa 29
Mfundo za Madani 8 zokhudzana ndi kuyankhula bwino 30
Zinthu 15 zaphindu m'dziko komanso dziko limene likubwera 32
Malangizo 50 opatsa chidwi 33
Miyambi 19 ya chiarabu(ndi kumasulira m'Chichewa) yokhudzana ndi lilime mogwirizana ndi zilembo 19 za بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ 38
Miyambi 11 ya Urdu (ndi matanthauzo a Chichewa) 39
Kulapa kwa zizolowezi zauchimo kunaperekedwa 40
Kuyitanira ku chiwongoko(mwachidule) 42

KUPAMBANA KOPEWA KUYANKHULA ZOPANDA PAKE 43
Kuwerenga Salat(kumufunira zabwino Mtumiki) mochuluka zimaonetsa kuti muli phindu 43
Allah Wamphamvu zonse amadana ndi zokambirana zopanda pake: 44
Ndemanga ya ndime yodalitsika 45
Chilimbikitso kuti tipewe zinthu zopanda pake: 45
Chipulumutso ndi chiyani? 46
Kufunikira koteteza lilime komanso phindu lake ndi zoyipa zake: 46
Thireyi ya tende (Nkhani): 47
Kuti anthu angakugululeni mano anu: 47
Chilango chapadera pa funso limodzi lopanda pake (Nkhani): 47



www.dawateislami.net

Palibe angakwanitse kupirira pa chilango cha ku Gahena: 48
Ntchito zolemera: 48
Kukongola kwa munthu ndi chiyani? 48
Malangizo a Mtumiki Woyera ﷺ: 49
Dua ya Mustafa: 49
Chizindikiro chakuti chifundo cha Allah Wamphamvu zonse chachoka: 49
Munthu amene amangoyankhula zopanda pake amakhala ndi machimo ambiri: 49
Kutchulidwa kolemekezeka kwa Sayyiduna Abdullah Ibn Abi Awfa: 50
Dua kwa munthu wopereka Zakah: 50
Kukumana kwa Imam Abu Hanifah ndi sahaba wa Mtumiki: 51
Kuyankhula kopanda pake ndi chiyani? 51
Ngati mu kukhala chete mulibemo kulingalira za dziko likubwera, ndiye kuti kumeneko ndi kunyalanyaza: 52
Kunyalanyaza ndi chiyani? 52
Ndikuopa kupezeka kwa kunyalanyaza pa inu: 53
M'malo mwake, ndikulira chifukwa cha mapemphero osiyidwa: 53
Adzalowa ku Gahena akulira: 54
Munthu woyera anapereka nkhani yabwino ku maloto: 55
Mitundu iwiri ya mayankhulidwe komanso kukhala chete: 57
Satana amamugonjetsa munthu amene samateteza lilime lake: 58
Chida chachikulu cha Satana: 58
Siddiq-e-Akbar amkayika mwala mkamwa mwake: 59
Kukhala chete kwa zaka 40 (Nkhani): 59
Tabi'i woyera amene analemba mikambirano komanso ndikuyiwunikira: 59
Momwe tingawunikire mkambirano: 60
Kuwunikira ntchito: 61
Dandaulo kwa Allah Wamphamvu zonse lokhudzana ndi kuthwa kwa lilime: 61
Musatilole ife kutuluka pa lilime: 61
Lilime liyenera kukhala m'ndende: 62
Kukhazikika pa kupembedza kumabwera chifukwa choteteza lilime: 62



www.dawateislami.net

| | |
|---|---|
| Kudzikakamiza kunena zopanda pake (Nkhani): | 62 |
| Nditha kupirira kusala kudya kwa nyengo yotentha kwambiri koma... | 63 |
| Lilime ndiloyenera kwambiri chitetezo: | 63 |
| Chifukwa chimodzi choyambitsa kusowa kwa chakudya: | 64 |
| Allah Wamphamvu zonse amamva zinthu zonse: | 64 |
| Bwanji munakakhala kuti muzilipira ndalama chifukwa choyankhula zopanda pake? | 64 |
| Angelo amalemba china chilichonse: | 64 |
| Nkhani yokhudzana ndi mkambirano opanda pake | 65 |
| Mfundo za Madani 7 za Farooqi | |
| Kuyankha mlandu wa mkambirano opanda pake kudzakhala kotalika kwambiri | 67 |
| Khalani kutali ndi zoyankhula zopanda pake kuti mupewe mavuto | 67 |
| Malangizo kwa munthu amene amayankhula zonyansa | 68 |
| Dawat-e-Islami inandipanga ine kukhala munthu wopemphera Salah | 68 |
| Lilime lili ngati mkango, wokonzeka kuyendayenda | 69 |
| Chilombo | 70 |
| Kuteteza chuma ndi kosavuta, koma kuteteza lilime... | 70 |
| Zizindikiro 6 za wodzipereka | 71 |
| Zizindikiro 6 za umbuli | 71 |
| Zoyipa zinayi za zokambirana zopanda pake | 72 |
| Phunzirani kukhala chete | 73 |
| Kupembedza kumayamba ndi kukhala chete | 74 |
| Kukhala chete ndi kiyi wa kupembedza | 74 |
| Malangizo asanu abwino kwambiri | 74 |
| Mahadith anayi okhudza ubwino okhala chete | 75 |
| Zabwino kuposa kupembedza kwa zaka 60 | 76 |
| Yankhulani zokhudza chinthu chabwino kapena khalani chete | 76 |
| Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amkakhala chete nthawi yayitali | 76 |
| Kalanga! Anthu ambiri anachokapo atamva kuwerengedwa ku Quran | 77 |
| Chikondi chomvetsera kuwerengedwa kwa Quran | 77 |
| Ubwino omvetsera ndime imodzi yoyera | 77 |




www.dawateislami.net

Kuvutika zaka 20 mu kuwerenga Quran 78
Ngati mukufuna Paradiso, musayankhule kungopatula zabwino 78
Kulapa kwenikweni kuchokera ku machimo 79
Kukhala chete ndi gwero la chitetezo cha Chikhulupiliro 80
Chinsinsi chokhala woyikidwiratu ku Paradaiso(Nkhani) 81
Sahabi aliyense wa Mtumiki anayikidwiratu kuti akalowa ku Paradaiso 82
Masahabah onse anayikidwiratu kuti akalowa ku Paradaiso 82
Kudya kwambiri ndi chifukwanso chimodzi choyambitsa choyankhula kwambiri 84
Aliyense amene amadya opanda chilakolako ndi munthu wokonda kuyankhula 84
Mawu oyipa amacheka kwambiri kuposa lupanga 84
Sungani lilime kukhala lomangidwa 84
Mawu osayenera pakamwa sangakhalenso oyenera kulikonse 85
Aliyense angawulule nkhani za m'banja ndi munthu wotsika mtengo 85
Nthawi zina mawu amatuluka pakamwa omwe… 86
Iye adzachepetsa kuyankhula mkambirano opanda pake 86
Kutelereka kwa lilime ndi koopsa kwambiri kuposa kutelereka kwa phazi 86
Ndani amadziwa nthawi ya kuyankhidwa? 87
Mavuto pa malo okwana asanu pa Tsiku la Chiweruzo kwa munthu amene amayankhula zopanda pake 87
Kukhala chete kuli ndi ubwino 7 88
Chinyamata ndi nthawi ya misala; pewani zoyipa zake 88
Kukhala chete kuli ndi ubwino 9 89
Tetezani lilime ngati golide ndi siliva 89
Kukhala chete ndi golide 89
Munthu wanzeru ndindani? 90
Kuyankhula pang'ono, ntchito yambiri 90
Kuzitalikitsa kuchokera ku kuyankhula zopanda pake m'mausiku a zaka 40 90
Ngakhale liwu lotukwana litha kukakulowetsa ku Gahena 91
Abwenzi oyipa anandiwononga ine 91
Malangizo kuti upewe mfundo zosafunikira mu mkambirano 93



www.dawateislami.net

Ngati munthu akuchita mkambirano wa m'dziko lapansi, pangani ma Zikr a Allah Wamphamvu zonse 94
Pamene chisamaliro chachifundo chachotsedwa 94
Kusowekera makhalidwe abwino komanso kumvetsetsa Deen 95
Woyankhulitsa nthawi zambiri amanong'oneza bondo 95
Kunong'oneza bondo chifukwa siunayankhule ndi bwino kuposa kunong'oneza bondo utayankhula 96
Munthu woyankhulitsa kwambiri amachititsidwa manyazi 96
Aliyense amene amaganizira kaye asanayankhule amazitalikitsa kuchokera ku mkambirano opanda pake 96
Wodwala khansa anachira 97
Palibe matenda osachiritsika 98
Machiritso auzimu a khansa 98
Munthu wopusa samadziwika ngati atakhala chete 98
Nanga bwanji dzuwa litapanda kulowa mpaka pakati pa usiku? (Nkhani) 99
Ndimalakalaka ndikanakhala wosayankhula 99
Ndimalakalaka iye akanakhala wosayankhula 100
Momwe nyumba ingakhalire ya mtendere! 100
Nkhani yodziwika ya pa tsamba la mchezo 100
Njira yothetsera mikangano pakati mkazi ndi apongozi 101
Kumuona Mtumiki Woyera ﷺ chifukwa cha m'dalitso okhala chete 101
Zoyipa za lilime ndi zazikulu 102
Umar Bin Abdul Aziz anagwetsa misonzi 102
Kufotokozera kwa nkhani 103
Tsatirani njira zosiyanasiyana zoyankhulira kuti mulimbikitse 104
Kuyankhula kwambiri, zolakwika zambiri 105
Kamba wapaulendo ayenera kukhala wokwanira ulendo 105
Udindo wa kukhala chete popanga malo wolimbikitsa-Sunnah pa khomo 106
Zoyipa za kufunsa mafunso opanda pake 107
Nzeru za Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه 108
Kukhala chete ndi nzeru(Nkhani) 108
Ndi mkambirano uti umene umatchedwa opanda pake? 109



www.dawateislami.net

Uthenga okhudzana ndi Sayyiduna Luqman Hakeem 109
Luqman Hakeem anali ndani? 110
Sayyiduna Luqman ndi m'modzi mwa atsogoleri aku Paradaiso 110
Matanthauzo anayi a nzeru 111
Sayyiduna Luqman anali Dokotala 111
Kuyipa kokhala m'chimbudzi nthawi yayitali 111
Ngati lilime ndi mtima zitakhala zoyipa, kenako... 112
Zitsanzo za mafunso opanda pake 112
Ndi zovuta kwa munthu woyankhulitsa kwambiri kupewa kukokomeza 114
Udindo wa kukhala chete popanga malo kukhala achipembedzo m'dera 114
Chida cha Madani cha ntchito za chipembedzo 115
Munthu wopusa amayankhula opanda kuganizira 115
Samalirani lilime, chilichonse chidzakhala bwino 116
Ganizirani musanayankhule 116
Njira yolingalira musanayankhule 116
Njira yokhalira chete 117
Palinso kuyankha mlandu pa kuyankhula zopanda pake pogwiritsa ntchito chinenero cha manja 118
Phindu lolingalira kaye usanayankhule 119
Mkambirano opanda pake wa uchigawenga 120
Mtima wa munthu woyankhulitsa umakhala wouma 120
Sayyiduna Imam Malik amkamunyengelera munthu amene amakonda kupanga miseche 120
Munthu wophwanya malamulo anasanduka kukhala wodekha 121
Machiritso 7 a machimo 122
Ntchito iliyonse yabwino imene ndiyovuta kuyichita imakhala ndi malipiro ochuluka 123
Pewani mkambirano opanda pake 124
Iye sadzanong'oneza bondo ku Paradaiso 125
Nsonga ya cholembera 125
Kudzala mtengo ku Paradaiso 126
Ubwino omufunira zabwino Mtumiki Womaliza ﷺ 126



www.dawateislami.net

Phindu la pa dziko kapena la muyaya la mkambirano 127

Chitsimikizo chowerengera mawu oti ‘سُبۡحٰنَ اللّٰه’ kapena kuwapanga iwo kuwerengedwa 127

Zabwino kuposa zaka zokwana 60 za kupembedza 128

Kufunikira kwa nthawi ya mtengo wapatali 129

Chifukwa chachikulu choyambitsa kunyozeka 129

Nthawi ili ngati lupanga 129

Kuwerenga mu Sakrat 129

Nthawi imene Faizan-e-Sunnat yalowa m’nyumba 130

Nkhani 25 za kupewa mkambirano opanda pake 132

1. Osayankhula motero mwakuti mudzafunika kupepesa nthawi ina 132

Kufotokozera kwa magawo awiri a Hadith 132

2. Wokondedwa bambo! N’chifukwa chiyani simuyankhula? 133

3. Njira yopezera kumuopa Allah Wamphamvu zonse 133

4. Malangizo kwa lilime ali chiyimire pa Phiri la Safa 134

5. Tsoka kwa inu! 134

6. Ndimakonda kukhala chete kuposa m’mene ndimakondera kuyankhula 135

7. Amuna atatu ochita zabwino Allah Wamphamvu zonse amene anayenda pa madzi ndipo anayandama 136

Mtengo ku Paradaiso –Chitetezo kuchokera ku zoyipa 136

8. Ngati china chake chayikidwa mkamwa 137

Ndikulakalaka panakakhala chitseko cha chitsulo 137

9. Kulamulira lilime lake 138

Allah Wamphamvu zonse ndi yemwe amapereka chipambano 138

10. Ophunzira anayi, zoyankhula zinayi 138

11. Mafumu anayi, mikambirano inayi 139

12. Iye sanaseke kwa zaka 40 140

Ubwino omuopa Allah Wamphamvu zonse 140

Hadith Yolemekezeka yowonetsa kuti kumuopa Allah Wamphamvu zonse kumaonjezera chakudya komanso zaka 141

Kumuopa Allah Wamphamvu zonse kumatanthauza chiyani? 141

13. Anthu amene amayankhula kenako ndikukhala chete 141



www.dawateislami.net

14. Lingaliro la kukhala chete cholinga chofuna kubisa zimene waluza 142
Kusangalala pa kuluza kwa Msilamu 142
15. Kukhala chete ndi chizolowezi cha anthu anzeru 143
Kunena lamulo lolakwika 143
Zitsanzo zitatu za anthu amene anali opatulika popereka mayankho 144
16. Ndi chithu chanzeru kusasokoneza mkambirano wa munthu wina 144
Aliyense angasokoneze popanda chifukwa ndi wopanda nzeru 145
17. Kukhala chete ndi kofunikira pa chinsinsi 145
Kutumiza mauthenga a WhatsApp kwa anthu ena 145
Zoyankhula ziwiri za Mtumiki Woyera zokhudza kusunga chinsinsi cha munthu wina 146
18. Ngati mtendere ukufunidwa, kukhala chete ndikofunikira 147
Chinyengo chachikulu 147
19. Nzeru zimabwera bwanji? 148
20. N'chifukwa chiyani simukuyankha? 148
Uku ndikulingalira usanayankhule 148
21. Munthu wosayankhula wanzeru ndi opambana kuposa munthu woyankhulitsa amene ali mbuli 149
Tetezani anthu kuchokera ku zoyipa zanu 150
Ubwino oteteza anthu kuchokera ku zoyipa 150
Ntchito zitatu zomwe zimatsogolera ku Paradaiso 151
22. Chopereka chokwana dirham imodzi kuchotsa mawu opanda pake ena aliwonse 151
Kulimbikira kwa zaka 20 mopitirira 152
Vesi ya mu Qur'an yokhudzana ndi kulimbikira 152
Nkhani yabwino kwa anthu onse amene amalimbikira mu njira ya Allah Wamphamvu zonse 153
Wophunzira-wopelewera mu nzeru anakhala Imam wolemekezeka (Nkhani) 153
Mfumu ndi nyerere (nkhani) 154
Mphaka anachita bwino 154
23. Mukuyenera kunyadira pa kukhala kwanu chete 155
Kukhala chete kuli ndi ubwino 155



www.dawateislami.net

24. Mbalame inalira ndipo inaphedwa 156
25. Kunena kuti 'Ndine okhumudwa kwambiri' 156
Momwe zimakhalira kunena kuti 'kutentha thupi kwambiri'? 157



www.dawateislami.net

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الْمُرْسَلِيْنَ
اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ ؕ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ ؕ

# MIYAMBO YA POKAMBIRANA

O Mbuye wa Mustafa, aliyense angawerenge kapena kumvetsera buku la masamba 42 la '*Miyambo ya pokambirana*', aphunzire kuyankhula mogwirizana ndi Sunnah ndipo akhululukidwe mopanda kuyimbidwa mlandu!

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

## Ubwino omufunira zabwino Nabi ﷺ

Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Ndithudi, munthu amene adzakhale pafupi ndi ine pa Tsiku la Chiweruzo ndi amene amandifunira zabwino mochuluka." *(Tirmizi, buku. 2, tsamba. 27, Hadith: 484)*

E omukonda Rasool! Mopanda chikayiko, munthu atha kumafuna kuyankhula nthawi iliyonse komano kumbukirani kukhala chete ndikopambana kuposa ngakhale mawu ololedwa opanda pake.

## Kuletsa kukweza mawu pamene tikuyankhula

Allah Wamphamvu zonse wayankhula mu gawo 21, Surah Luqman, ndime 19:

وَاغْضُضْ مِنْ صَوْتِكَ ؕ اِنَّ اَنْكَرَ الْاَصْوَاتِ لَصَوْتُ الْحَمِيْرِ ﴿۱۹﴾

*Ndipo tsitsani mawu anu; ndithudi, mawu oyipitsitsa kuchokera m'mawu ena ndi kulira kwa bulu.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 21, Surah Luqman, ndime 19)*



www.dawateislami.net

## Kuyankhula motsitsa mawu ndi Sunnah

'Allamah Mufti Syed Muhammad Naeem-ud-Deen Muradabadi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba mu ndemanga ya ndime yolemekezekayi kuti: "Kupanga phokoso komanso kukweza mawu ndikosakondedwa komanso kosayenera, ndipo mulibemo ubwino m'menemu. Kulira kwa bulu, ngakhale kumakhala kokwera mawu, ndi kosakondedwa komanso koyipa. Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amkakonda kuyankhula motsitsa mawu ndipo iye samkakonda kuyankhula mosakhala bwino." *(Khazain Al-'Irfan, tsamba. 762)*

## Okhulupirira milungu yambiri achiluya ankaona ngati kuyankhula mokweza mawu ndi chithu chonyaditsa

'Allamah Ismail Haqqi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba kuti: "Pamene anthu akuyankhulana, mawu oyipitsitsa komanso osakhala bwino mwa iwo ndi munthu amene amayankhula mokweza ngati bulu. Okhulupirira milungu yambiri achiluya ankaona ngati kuyankhula mokweza mawu ndi chithu chonyaditsa. Mu ndime imeneyi, m'chitidwe wawo wodzikweza unatsutsidwa." *(Mwachidule kuchokera mu Ruh al-Bayan, buku. 7, tsamba. 87)*

## N'chifukwa chiyani bulu amalira?

Kulira kwa bulu kukufotokozedwa, choncho, nkhani yodziwitsa yabweretsedwa yokhudza zimenezi. Chifukwa chake, Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Pamene mwamva kulira kwa tambala, pemphani kwa Allah Wamphamvu zonse chifundo chake chifukwa amakhala waona angelo. Ndipo pamene mwamva kulira kwa bulu, sakanisakani chitetezo mwa Allah Wamphamvu zonse kuchokera kwa Satana chifukwa amakhala waona Satana." *(Bukhari, buku. 2, tsamba. 405, Hadith: 3303)*



www.dawateislami.net

Mwachitsanzo, nenani zotsatirazi: اَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْم

*(Tayseer Sharh Jami' Sagheer, buku. 1, tsamba. 107)*

## Kuyetsemula mokweza ndi zonyansanso

Sayyiduna 'Allamah Ismail Haqqi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analembanso zokhudzana ndi ndime yolemekezeka yatchulidwa m'mwambamu: "Kuchokera ku zimenezi, nkhani yoyetsemulanso ndi yowonekeratu kuti kuyetsemula mokweza mawu ndi zonyansa. Ndi chifukwa chake lamulo ndiloti munthu ayenera kuyesetsa kuyetsemula motsitsa mawu momwe angathere." *(Ruh Al-Bayan, buku. 7, tsamba. 88, mwachidule)*

Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Kuyetsemula mokweza ndi kochokera kwa Satana." *('Amal al-Yaum wa al-Laylah, tsamba. 119, Hadith: 265)*

Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amkadana ndi kuyetsemula mokweza mu Mzikiti. *(Shu'ab Al-Iman, buku. 7, tsamba. 32, Hadith: 9356)*

Sayyiduna 'Allamah Abdul Rauf Munawi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena zokhudzana ndi Hadith iyi: "Tanthauzo ndilakuti kuyetsemula mokweza mawu mu Mzikiti ndikonyansa kwambiri ndipo ndikonyansa pang'ono panja pa Mzikiti." *(Faiz Al-Qadeer, buku. 5, tsamba. 311, Hadith: 7156)*

## Yang'anani ndi nkhope yanu molunjika alendo

Allah Wamphamvu zonse wayankhula mu gawo 21, Surah Luqman, ndime nambala 18:

وَلَا تُصَعِّرْ خَدَّكَ لِلنَّاسِ

*Ndipo musalipange tsaya lanu kukhala lokhota(mwamwano) pamene mukuyankhula ndi aliyense.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 21, Surah Luqman, ndime 18)*



www.dawateislami.net

Sayyiduna ‘Allamah Syed Naeem-ud-Deen Muradabadi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba mu ndemanga ya ndime yodalitsikayi: “Musatengere njira ya munthu wodzikweza amene amati, pamene anthu akuyankhula, amatembenuza nkhope zawo kuchokera kwa iwo kwinaku akumawatenga iwo (amene akuyankhulana nawo) ngati apansi kwambiri; muchitireni aliyense zabwino, kaya akhale osauka kaya ndi olemera, ndipo pakhale kudzichepetsa.” *(Khazain Al-Irfan, tsamba. 761)*

Sayyiduna ‘Allamah Ismail Haqqi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba mu *Tafseer Ruh al-Bayan*: “Yang’anani ndi khope yanu yonse pa anthu pa nthawi ya malonje, kuyankhula komanso mkumano modzichepetsa; musatembenuze khope yanu kuchokera kwa iwo kapena kuphimba mbali iliyonse ya khope. Ndi chizolowezi cha anthu odzikweza kuti iwo amawayang’ana anthu monyoza ndipo amawayang’ana osauka ndi osowa mwamkwiyo. Zoona zake, onse olemera ndi osauka ayenera kukhala ayenera kukhala ofanana kwa inu powapangira zabwino.” *(Ruh Al-Bayan, buku. 7, tsamba. 84)*

## Mwambo uyenera kukhala oti kukambirana kukhale komveka

Tiyenera kupewa kufuula mokweza mawu, chifukwa Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanayankhuleko motero. Pa nthawi ya kuyankhula kwake kolemekezeka, mawu ake samkakhala okwera kwambiri kapena otsika kwambiri kuti munthu wina amkalephera kumva ayi.

## Zoyankhula za Mtumiki Woyera ﷺ zimkakhala zofewa

Umm-ul-Mu’mineen (mayi wa anthu onse okhulupirira) Sayyidatuna Aishah Siddiqah رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهَا ananena kuti Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amkayankhula momveka bwino; womvera aliyense amkamvetsetsa. *(Abu Dawood, buku. 4, tsamba. 343, Hadith: 4839)*



www.dawateislami.net

## Mtumiki Woyera ﷺ amkabwereza mfundo katatu

Kapolo wa Mtumiki Wolemekezeka, Sayyiduna Anas رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anafotokoza kuti: “Pamene Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali kunena chithu china chake, iye amkachibwereza katatu ndicholinga chakuti chimveka.” *(Bukhari, buku. 1, tsamba. 52, Hadith: 95)*

**Kufotokoza kwa Hadith:** Zafotokozedwa mu is *Mir'aat* kuti: “Zikutanthauza kuti, panthawi imene akunena malamulo, iye amkabwereza lamulo lililonse katatu ndicholinga malamulo akhazikike m'mitu mwa anthu. (Pamenepa), sizikutanthauza kuti (kubwereza kwa) mfundo iliyonse (katatu).” *(Mir'aat, buku. 1, tsamba. 194)*

## Kukambirana kwa Mustafa ﷺ

Zafotokozedwa mu *Sirat-ul-Jinan*, buku 7, tsamba 502: “Zikukambidwa m'mabuku a Seerah kuti Mtumiki wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم samkayankhula mwachangu, m'malo mwake, iye amkayankhula mopumira, ndipo zoyankhula zake zimkakhala zomveka bwino komanso zosiyana kwambiri moti omvera amkamvetsetsa komanso kuloweza, ndipo ngati pali mfundo yofunikira, iye nthawi zina amkabwereza mfundo imeneyo katatu ndicholinga chakuti omvera akhazikitse m'mitu mwawo. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم samkayankhula mosafunikira;m'malo mwake, iye nthawi zambiri amkakhala chete. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapatsidwa chozizwitsa chokhala “*Jami' Kalimaat*”, mukunena kwina. iye amkawapanga mawu aatali kukhala aafupi.

## Nduna imene imkagwiritsa mawu ovuta (nthabwala)

Pamene mukuyankhula, mawu ayenera kukhala osavuta komanso omveka bwino. Ngati mukugwiritsa mawu ovuta, zitha kutheka kuti munthu atha kungotengeka ndi luso lanu la chinenero, komano iye sangamve zimene mukufuna munene. Yesani kumvetsetsa mfundo yangayi kudzera mu



www.dawateislami.net

nthabwala yopekayi: "Tsiku lina, nduna ya zaulimi komanso ulimi wothirira anapita kukayendera mudzi wina. Nthumwi za alimi zinabwera kudzakumana nayo. Anthu amenewo anatumiza mlimi m'modzi kuti akapemphe chilolezo kuchokera kwa nduna. Nduna inayang'ana m'mwamba ndipo inafunsa kuti: '*Tumhari Kisht-e-Zaar per Imsal Taqatur-e-Amtar Huwa Ya Nahi?*' (Kodi mvula inagwa m'munda mwako chaka chino kapena ayi?) Pamene mlimi wosaphunzira anamva mawu amenewa, iye nthawi yomweyo anatuluka ndipo ananena kwa anzake kuti: 'Nduna yolemekezeka ikuwerenga Quran.'"

E omukonda Rasool, zinakakhala kuti nduna sinagwiritse chiyankhulo chovuta, mlimi sakanasokonezeka, ngakhale iye samkawerenga Quran; zinangokhala kuti mfundo inakambidwa mopititira muyeso. Tanthauzo la mawu anduna ndilakuti: Kodi mvula inagwa m'munda mwanu chaka chino kapena ayi? Choncho, pamene mukukambirana ndi ndi munthu wina wake kapena kupereka ulaliki ndi kuyankhula kulikonse kapena kulemba nkhani komanso buku ndi zina zambiri, yesetsani kugwiritsa ntchito mawu amene angamvetsetsedwe ndi omvera komanso owerenga.

## Zithu ziwiri zimene zidzawalowetse ku moto anthu ambiri

Okondedwa abale achisilamu, ndi zofunikira kwambiri kulisamalira lilime. Pali anthu ambiri amene adzalowe ku Gahena chifukwa cha malilime awo basi. Sayyiduna Abu Hurairah رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anafotokoza kuti Mtumiki Woyera صَلَّی اللہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anafunsidwa kuti, "Ndi ntchito iti yomwe idzawalowetse anthu ambiri ku Paradaiso?" Iye صَلَّی اللہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anayankha kuti, "Kumuopa Mulngu ndi makhalidwe abwino." Ndipo iye anafunsidwanso kuti, "Ndi chiyani chomwe chidzawalowetse anthu ambiri ku Gahena?" Iye anati, "Zinthu ziwiri: pakamwa ndi maliseche." *(Ibn-e-Majah, buku. 4, tsamba. 489, Hadith: 4246)*



www.dawateislami.net

## Ndindani adzakakhale ku Paradiso?

Sayyiduna Abu Hurairah رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ anafotokoza kuti Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: “Aliyense yemwe Allah Wamphamvu zonse wamuteteza kuchokera ku zoyipa za zithu zimene zili pakati pa nsagwada ndi miyendo (pakamwa ndi maliseche), adzalowa ku Paradiso.” *(Tirmizi, buku. 4, tsamba. 184, Hadith: 2417)*

## Chitsimikizo cha Paradiso

Aliyense angateteze pakamwa pake komanso maliseche ake, mukunena kwina, iye samazigwiritsa ntchito mosemphana ndi Shari’ah, munthu ameneyo wayikidwiratu kuti akalowa ku Paradiso.Pakuti, sahaba wa Mtumiki, Sayyiduna Sahl Ibn Sa’d رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ anafotokoza kuti Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: “Aliyense anganditsimikizire ine za zinthu zopezeka pakati pa nsagwada zake ndi miyendo yake (pakamwa ndi maliseche), Ndikumpatsa iye chitsimikizo cha Paradiso.” *(Bukhari, buku. 4, tsamba. 240, Hadith: 6474)*

Zikutanthauza kuti pali lonjezo la Paradiso chifukwa choteteza pakamwa ndi maliseche kuchokera ku zithu zoletsedwa ndi Shari’ah.

## 80 peresenti ya machimo imapangidwa ndi lilime

Zithu za pakati pa nsagwada ziwiri ndi lilime ndi mkhama ndi zina zambiri, ndipo zithu za pakati pa miyendo iwiri ndi maliseche, mukunena kwina, munthu ayenera kuteteza lilime lake kuchokera ku bodza, miseche komanso kuyankhula zithu zosaloledwa, iye ayenera kuteteza pakamwa pakamwa pake kuchokera ku chakudya cha Haraam ndipo iye sayenera kuwasiya maliseche ake kuyandikira chiwelewele. Ndi zachidzikiwikire kuti Msilamu ameneyo adzakhala ochita zabwino. Kumbukirani kuti pafupifupi 80 peresenti (ambiri) mwa machimo amapangidwa ndi lilime. Munthu, amene amateteze lilime lake, samaba, samachita umbava kapena



www.dawateislami.net

kupha. Munthu amapalamula mlandu pokhapokha pamene wakhonzekera kunama, kuti ndidzakana ngati nditagwidwa. Kunama ndi gwero la machimo onse. Kumbukirani kuti chitsimikizo chimenechi chochokera kwa Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi cha anthu onse mpakana kufikira Tsiku la Chiweruzo, ndipo chitsimikizo chochokera kwa Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi chitsimikizo chochokera kwa Ambuye Wamphamvu zonse. *(Mir`aat, buku. 6, tsamba. 447, ndi kusinthidwa pang'ono)*

## Pempho la ziwalo zonse za thupi kwa lilime

Sahaba wa Mtumiki, Sayyiduna Abu Saeed Khudri رَضِیَ اللّٰہُ عَنْهُ anafotokoza kuti Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Pamene munthu wadzuka mam'mawa, ziwalo zake za thupi zimagwada ndipo zimanena kwa lilime kuti, 'Muope Allah Wamphamvu zonse zokhudzana ndi ife chifukwa tili limodzi ndi iwe. Ngati iweyo ungakhale owongoka, nafenso tidzakala owongoka, ndipo ngati utapindika, nafenso tidzakhala opindika.'" *(Tirmizi, buku. 4, tsamba. 183, Hadith: 2415)*

## I'tikaf ya Pagulu imakhala njira yozisinthira

Okondedwa abale achisilamu, ngati tikugwiritsa ntchito lilime moyenera, phindu lonse lopezeka kuchokera ku lilime zidzakololedwa ndi ziwalo zonse za pathupi, ndipo ngati silikugwira moyenera; ngati litatukwana munthu wina ndi zina zambiri, ndiye kaya lilime lapwetekedwa nawo kapena ayi, ziwalo zina zonse za pathupi zidzamenyedwa. Kuti mukhale ndi malingaliro okhala osamala lilime, nthawi zonse ziyikeni mu zochitika zachipembedzo za Dawat-e-Islami. Ngati Allah Wamphamvu zonse wakupatsani kuthekera, ndiyeno pangani nawo I'tikaf ndi omukonda Rasool amene ali gawo la Dawat-e-Islami m'mwezi wa Ramadan-ul-Mubarak. سُبْحٰنَ اللّٰه! Madalitso aakulu bwanji omwe ali mu I'tikaf! Ndikuuzeni chozizwitsa cha Madani: Malingana ndi tsatanetsatane amene

anaperekedwa ndi m'bale wa Chisilamu ochokera dera lotchedwa Mandi Bahauddin (Punjab), asanalowe mu zochitika za chipembedzo za Dawat-e-Islami, Allah aletse, iye amkatenga makhwala osokoneza bongo. Iye amkakonda kuledzera ndi mowa komanso chamba mpakana iye anayamba kuba komanso umbava ndi cholinga chakuti akagule makhwala osokoneza bongo, pachifukwa chimenechi achibale ndi anansi akenso anayamba kukhala ndi nkhawa. Ulendo wake osinthika unayamba motere, m'mwezi wodalitsika wa Ramadan, iye anali ndi mwayi opanga nawo Sunnah I'tikaf ndi omukonda Rasool a Dawat-e-Islami. Iye anapezanso abwenzi abwino mu nthawi ya I'tikaf ndipo anapitirizanso kuwerenga buku la, '*Faizan-e-Sunnat*',. Patadutsa nthawi, iye anapeza mwayi otenga nawo mbali pa mkumano wa pasabata umene unachitika pa Madani Markaz Faizan-e-Madinah ya Dawat-e-Islami ku Mandi Bahauddin, pomwe, anaona gulu la omukonda Rasool atavala zovala za Chisilamu, mtima wake unayamba kusintha. Patatha sabata imodzi, iye anafikanso pa mkumano wa pasabata mu nthawi yokonzedwa ndipo anayamba kumvera ulaliki. Ulaliki unali ndi zotsatira zimene zinapangitsa dziko lake lonse kusinthiratu, ndipo iye anabwerera ku nyumba atamaliza kulapa machimo ake. Sikuti anangoyamba kupemphera mapemphero asanu a Fard pafupipafupi ayi komanso anasunga ndebvu zotalika ngati chibakera ndipo anayambanso kuvala motsatira ndi Sunnah. Kudzera mu chifundo cha Allah Wamphamvu zonse, iye anapezanso mwayi wofalitsa kuyitanira ku zabwino poyenda m'Madani Qafilah a Dawat-e-Islami pamodzi ndi anthu omukonda Rasool.

*اِنْ شَآءَاللّٰہ Bhai sudhar jao gay*

*Madani mahol mayn kar lo tum i'tikaf*

*Marz-e-'Isyan say chutkara tum pao gay*

*Madani mahol mayn kar lo tum i'tikaf*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 644)*



www.dawateislami.net

## Nyumba zowonekera mkati ku Paradiso

Khalifah wachinayi wa Asilamu, Sayyiduna Maula Ali, Mkango wa Ambuye رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ anafotokoza kuti Mtumiki Wolemekezeka صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati: "Kuli nyumba zapamwamba ku a Paradiso zimene panja pake ndipowonekera kuchokera mkati ndipo mkati mwake ndimowonekera kuchokera panja." Munthu wochokera kumudzi anafunsa mwaulemu kuti: "Ya Rasoolallah صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم, nyumba zimenezi zidzakhala zandani?" Iye صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anayankha kuti: "Munthu amene amayankhula mwaubwino, amadyetsa chakudya anthu ena, nthawi zonse amasala kudya komanso kupemphera mkati mwausiku pamene anthu ena akugona." *(Tirmizi, buku. 3, tsamba. 396, Hadith: 1991)*

## Zoyankhula zabwino ndi chopereka

Kuyankhula zokhudza china chake chabwino ndizopambana kuposa kungokhala chete ndipo kukhala chete ndikopambana kuposa kuyankhula zopanda pake; pamene kuyankhula zoyipa ndithudi ndi koyipa. Sayyiduna Abu Hurairah رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ anafotokoza kuti Mtumiki Wolemekezeka صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati: "Kuyankhula zabwino ndi kupereka chopereka ." *(Bukhari, buku. 2, tsamba. 306, Hadith: 2989)*

## Zimatanthauza chiyani akamati chopereka?

Pamenepa, chopereka zikutanthauza kupeza malipiro a chopereka. Mtumiki Woyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati: "China chilichonse chabwino ndi chopereka." *(Bukhari, buku. 4, tsamba. 105, Hadith: 6021)*

**Kufotokozera kwa Hadith:** Zikutanthauza kuti, chopereka sichimachitika kungopatula kudzera mu chuma, (ngakhale) ntchito iliyonse yabwino komanso yochepa imene yachitika ndi chitsimikizo chabwino, malipiro a



www.dawateislami.net

chopereka amapezedwa pamenepa, kwambiri kotero kuyankhula mawu abwino ndi ofewa kwa m'bale wachisilamu ndi choperekanso.

*(Mir`aat, buku. 3, tsamba. 95)*

## Itanirani ku zabwino mwachangu

Munthu sayenera kusiya chithu chaphindu chimene iye akudziwa kuti anthu amene atenga nawo mbali adzafuna mkumano wina pa chithu chimenechi, (Mwachidule, iye ayenera kufotokoza mfundo yonse mwachangu ndipo sayenera kunena kuti afotokozabe zonse nthawi ina.) chifukwa (kwa munthu ofotokoza komanso amene amawafotokozera chithucho,) palibe chitsimikizo chokhala ndi moyo mpaka kufikira mkumano wina. *(Islah-e-A'maal, tsamb. 360; Al-Hadiqah al-Nadiyyah, buku. 1, tsamba. 95)*

## Munthu wa makhalidwe abwino adzayandika ndi Mtumiki ﷺ

Sahaba wa Mtumiki, Sayyiduna Jabir رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anafotokoza kuti Mtumiki Wolemekezeka صَلَّی اللہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati: "Mopanda chikayiko, kuchokera mwainu, okondedwa kwambiri komanso oyandikira kwa ine pa Tsiku la Chiweruzo adzakhala amene ali ndi makhalidwe abwino pakati panu. Ndipo kuchokera mwainu, munthu osakondedwa komanso otalikana ndi ine pa Tsiku la Chiweruzo adzakhala amene ali ndi makhalidwe oyipa, amene amayankhula kwambiri, ndi amwano komanso amayankhula mopitirira malire ndi kukamwa kwawo. *(Shu'ab Al-Iman, buku. 6, tsamba. 334, Hadith: 7989)*

## Makhalidwe abwino ndi atiwo?

Sayyiduna Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ anafotokoza mu kufokozera kwa Hadith yolemekezekayi: "Chifukwa munthu wa makhalidwe-abwino nthawi zonse amapanga ntchito zabwino. Iye samapanga machimo



www.dawateislami.net

nthawi zambiri. Chilungamo (kukhulupirika, kukhala wokhulupirika, kunena zoona), kukwaniritsa malonjezo komanso kuchita zinthu moyenera zikuphatikizidwa m'makhalidwe abwino. Ndipo anthu amakhalidwe oyipa nthawi zambiri amakhala anthu ochimwa. Makhalidwe oyipa pawokha ndi oyipa komanso njira ya ntchito zambiri zoyipa. Kunama, kuononga (chikhulupiriro), kuphwanya lonjezo komanso kupanga chinyengo mu zichitochito zonsezi ndi nthambi za makhalidwe oyipa." *(Mir`aat Al-Manajih, buku. 6, tsamba. 436, mwachidule)*

## Chithu choopsa kwambiri

O anthu omukonda Rasool, kuteteza lilime ndi zofunikira kwambiri chifukwa zisokonezo ndi zoyipa zimachokera ku lilime. Sahaba wa Mtumiki, Sayyiduna Sufyan Bin Abdullah رَضِیَ اللّٰہُ عَنْهُ anafotokoza kuti tsiku lina ndinayankhula mozichepetsa pa maso pa Mtumiki Wolemekezeka صَلَّی اللہُ عَلَیْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuti: "Ya Rasoolallah صَلَّی اللہُ عَلَیْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, ndichiyani chimene mungachitchule kuti chinthu choopsa kwambiri komanso choyipa kwa ine?" Mtumiki Wolemekezeka صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anagwira lilime lake lodalitsika ndipo anati: "Ichi." *(Tirmizi, buku. 4, tsamba. 184, Hadith: 2418)*

## Makutu ali ngati galasi ndipo zoyankhula zopanda pake zili ngati miyala

'Allamah Abdul Wahhab Sha'rani رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَیْه ananena kuti: "Ndinawamva Shaykh Afzal-ud-Deen رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَیْه akunena kuti makutu ali ngati galasi ndipo zoyankhula zopanda pake zili ngati miyala. Pamene miyala yaponyedwa pa galasili, galasi lidzasweka." *(Al-Minan Al-Kubra, tsamba. 547)*

## Lilime lilibe fupa komano limapangitsa mafupa kusweka

Zikunenedwa kuti: Lilime lilibe fupa komano limapangitsa mafupa kusweka. Lilime si lupanga komano limakhetsa mwazi. Ndi mfundo



www.dawateislami.net

yabwino kwambiri imene wina wanena: Pa zithu zimene zomwe anthu amamenyera nkhondo ndikuyikidwa m'manda, akhoza kukhululuka komanso kuyiwala ndikumakhala moyo wabwino m'dziko.

## Kumutchula wina wake kuti bulu kapena nkhumba

Tabi'i woyera, Sayyiduna Ibrahim Nakha'i رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Ngati munthu wamutchula munthu wina kuti bulu kapena nkhumba, woyitana adzafunsidwa pa Tsiku la Chiweruzo kuti: 'Tandiuze, ndinamulenga iye ngati bulu? Tandiuze, ndinamulenga iye ngati nkhumba?'" *(Ihya al-Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 494; Ihya al-Uloom, buku. 3, tsamba. 200)*

## Kumutchula Msilamu ndi dzina loyipa ndi tchimo

E omukonda Rasool, ndizoletsedwa kumutchula kapena kumuyitana Msilamu ndi dzina loyipa, chifukwa ndi lamulo la Quran. Allah Wamphamvu zonse wanena mu gawo 26, Surah al-Hujuraat, ndime 11:

وَلَا تَنَابَزُوْا بِالْاَلْقَابِ ؕ

*Ndipo musapatsane wina ndi mzake mayina oyipa.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 26, Surah Al-Hujuraat, Ndime 11)*

Tikuphunzira kuti kupereka dzina loyipa kwa Msilamu ndi zoletsedwa. Othirira ndemanga olemekezeka anafotokoza ndime imeneyi m'mawu osiyanasiyana. Awiri mwa iwo abweretsedwa m'musimu kuchokera mu *Sirat-ul-Jinan*, buku 9, kuyambira tsamba 431 mpakana tsamba 432:

1. Ophunzira ena a Chisilamu anati: Kupereka mayina oyipa kwa Msilamu zikutanthauza kumutchula Msilamu kuti galu kapena bulu kapenanso nkhumba.



www.dawateislami.net

2. Ophunzira ena a Chisilamu anati zikutanthauza mayina amene amagwiritsidwa ntchito pomutukwana Msilamu ndipo iye amanyansidwa nawo, [koma mayina oyamikira amene ali owonadi, sioletsedwa, monga dzina lina la (khalifah oyamba wa Asilamu) Sayyiduna Abu Bakr رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ linali 'Ateeq', (khalifah wachiwiri) Sayyiduna Umar رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ linali 'Farooq', (khalifah wachitatu) Sayyiduna Usman Ghani رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ linali 'Zun-Noorain', (khalifah wachitatu) Sayyiduna Ali رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ linali 'Abu Turab' komanso (sahaba wa Mtumiki) Sayyiduna Khalid رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ linali 'Saifullah'] ndipo mayina amene anakhaladi ngati mayina enieni ndipo mwini wake opatsidwa sanyansidwa nawo, sioletsedwanso, monga, (Muhaddiseen wodziwika bwino) A'mash (osaona-bwino bwino) komanso A'raj (olumala mwendo umodzi),ndi ena ambiri.

*(Khazin, buku. 4, tsamba. 170)*

## Angelo amatumiza themberero

Mtumiki Wokondedwa komanso Omaliza wa Allah Wamphamvu zonse, Muhammad Arabi صَلَّی اللهُ عَلَیْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Munthu amene amamutchula Msilamu ndi mawu (dzina loyipa) kusiya dzina lake lenileni, angelo amamutemberera ." *(Jami' Saghir, tsamba. 525, Hadith: 8666)*

**Kufotokozera kwa Hadith:** Sayyiduna 'Allamah Abdul Rauf Munawi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه (anamwalira mu 1031 Hijri) anati: "('Angelo angelo amamutemberera iye' zikutanthauza kuti) kwa munthu amene amamuyitanira Msilamu ndi dzina loyipa, angelo amapempha kuti asapatsidwe ulemerero ndi kupambana kwa anthu ochita zabwino. Kupatula zimenezi, kumutchula munthu wina wake ndi mawu kusiya dzina lake zitha kutanthauza dzina limene amanyansidwa nalo kapena mbiri imene amanyansidwa nayo. Komabe, ngati muthu wamuyitana iye ndi mawu amene samanyansidwa nawo, ndiyeno palibe chovuta, mwachitsanzo, kumuyitana wina wake kuti, 'E Abdullah!' (E



www.dawateislami.net

mchimwene!), ndi ena ambiri. M'malo mwa dzina lake lenileni. *(Chidule chochokera mu: Fayz al-Qadeer, buku. 6, tsamba. 163, pansi pa Hadith: 8666)*

## Yankhulani zoona ngakhale ndi ana

Sahaba wa Mtumiki, Sayyiduna Abdullah Ibn Aamir رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anafotokoza (pamene amkafotokoza nkhani ya umwana wake wodalitsika) kuti tsiku lina, Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali nawo m'nyumba mwathu pamene amayi anga ananena kwa ine kwinaku akundiyitana kuti ndipite kwa iwo, "Tabwera kuno. Ndikupatsa china chake." Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anawafunsa (mayi anga), "Ndi chiyani chimene mukufuna mumpatse?" Iwo anayankha modzichepetsa kuti, "Ndimpatsa tende" Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Munakapanda kumupatsa chilichonse, bodza limodzi linakalembedwa mu buku lanu." *(Abu Dawood, buku. 4, tsamba. 387, Hadith: 4991)*

## Kutchulidwa kodalitsika kwa Sayyiduna Abdullah Bin Aamir رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ

Tiyeni timve mbiri ya sahaba wa Mtumiki amene anafotokoza nkhani imeneyi, Sayyiduna Abdullah Bin Aamir رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ. Dzina lake lodalitsika ndi Abdullah Ibn Aamir Bin Kuraiz. Iye ndi wa mtundu wachi Quraishi. Iye ndi msuweni ochokera mbali ya mayi wa khalifah wachitatu wa Asilamu, Sayyiduna Usman Ghani رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ. Pambuyo pa kubadwa kwake, iye anabweretsedwa pa maso pa Mtumiki Wolemekeza صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم; iye anauzira mpweya pa iye. Mu nthawi ya ulamuliro wa Sayyiduna Usman Ghani رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ, iye anakhalabe bwanamkubwa wa Basra komanso Khorasan. Sayyiduna Ameer Mu'awiyah رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anamuyikanso iye pa udindo omwewu. Iye ndi amene anapangitsa ngalande ya Basra



www.dawateislami.net

kukumbidwa. Iye anali wowolowa manja. Iye anamwalira mu chaka cha 57 kapena 58 Hijri. *(Al-Isabah li Ibn-e-Hajar, buku. 5, tsamba. 14 mpaka 15)*

## Tengani chuma ndi nyumba zonse ziwiri (Nkhani)

Sahaba wa Mtumiki, Sayyiduna Abdullah Bin Aamir رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anagula nyumba imene inali mu msika ndi ndalama zokwana 70 kapena 80 dirham kuchokera kwa Tabi'i woyera, Sayyiduna Khalid Bin Uqbah رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ. Pamene kunada, iye anamva nawu a banja la Sayyiduna Khalid رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ likulira, choncho iye anawafunsa achibale ake omwe kuti, 'Ndi chifukwa chiyani mukulira?' Iwo anayankha kuti, 'Chifukwa chakuti nyumba yagulitsidwa.' Choncho, (chidwi chake cha kuwolowa manja chinabwera ndipo) iye ananena kwa kapolo wake kuti, 'E kapolo, pita ndipo ukanene kwa Sayyiduna Khalid Bin Uqbah رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ kuti: Tengani nyumba komanso ndalama zimene tinagwirizana pa nyumbayo.'

*(Shu'ab Al-Iman, buku. 7, tsamba. 438, mawu nambala: 10887)*

Allah Wamphamvu zonse amuchitire chisoni komanso atikhululukire ife opanda kuyankha mlandu kudzera mu ubwino wake!

اٰمِیْن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِیّٖن صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم

صَلُّوا عَلَی الْحَبِیب! صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Momwe munthu osamvera makolo anasinthira?

Kuti muchulukitse chikondi cha masahaba komanso Ahl-e-Bayt عَلَیْہِمُ الرِّضْوَان, khalani ndi malingaliro opewa kuyipitsa mayina a Asilamu komanso khalani ndi chilakolako chokhala ndi chizolowezi choyankhula zowonadi nthawi zonse angakhale ndi ana, yendani ndi Madani Qafilah a Dawat-e-Islami. Mvetserani chozizwitsa cha Madani cha m'nyamata amene anali



www.dawateislami.net

osamvera makolo komano anasintha kudzera m'madalitso a zichitochito za chipembedzo za Dawat-e-Islami. Mudzakondwera: M'nyamata okhala m'dera lotchedwa Jhang, Punjab poyamba anali munthu wosapemphera-Salah ndipo anali osamvera makolo ake. Motero, iye analinso akuphwanya maufulu a Allah Wamphamvu zonse komanso aanthu. Tsiku lina, m'bale amene amkatenga nawo mbali pa zichitochito za chipembedzo za Dawat-e-Islami, anabwera kuti akumane ndi bambo ake pa shopu yawo. Pa nthawiyi, iye anali atakhalanso pomwepo. M'bale wa Chisilamu anamuyitanira iye kuti akapezeke nawo pa mkumano wa pasabata wolimbikitsa-Sunnah wa Dawat-e-Islami ndipo anavomera komasno anatenga nawo mbali pa mkumano wa chipembedzo pa tsiku Lachinayi. Iye anapeza mtendere wauzimu pa mkumanopa moti pambuyo pa zimenezi, chinakhala chizolowezi chake chomapezeka nawo pa mkumano wa chipembedzo Lachinayi lililonse. Sizimenezi zokha, komanso kudzera mu ubwino khama la m'bale wa Chisilamu uja, iye analinso ndi mwayi oyenda nawo mu Madani Qafilah kwa masiku atatu ndikuphunzira komanso kutsatira Sunnah. Mu nthawi ya Madani Qafilah, anthu omukonda Rasool anamulimbikitsa iye kuti akachite nawo maphunziro a kanthawi kochepa. Pamene iye anabwerera kuchokera ku Madani Qafilah, iye anavomereza zokhudzana ndi kusamvera makolo ake. Iye anagwada pa mapazi a makolo ake ndipo anapepesa kwa iwo. Iwo anaonetsa chikondi ndipo anamukhulukira. Pambuyo pa zimenezi, iye ananena kwa makolo ake kuti: Moyo ndi waufupi kwambiri; palibe amene amadziwa tsiku limene ungathe. Ndikufuna ndikapeze maphunziro a chipembedzo m'moyo wanga. Ponena zimenezi, iye anawanyengelera makolo ake kuti amulole akatenge nawo gawo pa maphunziro, ndipo atalandira chilolezo, iye anatenga katundu wake ali osangalala ndipo anatenga nawo gawo pa maphunziro kumene anaphunzira zinthu zochuluka kwambiri. Njira ya moyo wake inasintha mpakana moti munthu amene samkamvera makolo m'mbuyomo, tsopano anayamba kuwapyopyona mapazi awo asanachoke pa khomo. Kenako, iye anatenga nawonso gawo pa maphunziro a Fard Uloom. Pamene amkapita chitsogolo ndikuchita bwino, iye



www.dawateislami.net

anapatsidwanso udindo wa Nigran wa Halqah Mushawarat mu kakhazikitsidwe ka bungwe la Dawat-e-Islami. Allah Wamphamvu zonse amupatse iye ndi ife kukhazikika mu zochitika za chipembedzo za Dawat-e-Islami!

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

*Allah Karam aysa karay tujh pay jahan mayn*

*Aye Dawat-e-Islami tayri dhoom machi ho*

## Kuwakhazika ana mtima pansi ndi bodza

Tabi'i woyera mtima, Sayyiduna Imam Mujahid رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Zokambiranazo zimalembedwa (m'buku la ntchito) kwakuti pamene munthu wanena kwa mwana wake pomutonthoza kuti: Ndidzakugulira chinthu chotere (ngakhale alibe cholinga chogula), amalembedwa kuti ndi wabodza." *(Ihya Al-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 350; Ihya Al-'Uloom, buku. 3, tsamba. 142)*

## Tsatirani njira yosamala yowakhazikira mtima pansi

Kalanga! Masiku ano mabodza amanenedwa mochuluka pofuna kutonthoza ana; mwachitsanzo, amanenedwa ngakhale palibe chitsimikizo kuti: Tidzakugulirani zidole, mizende, matofi ndi mabisiketi a mtundu wakuti-wakuti, tidzakuphikirani chakudya cha mtundu wakuti-wakuti, ndipo tidzakupititsani kukacheza kumalo akuti-akuti, ndi zina zotero. Allah Wamphamvu zonse, Wachowonadi, atithandize ife nthawi zonse kunena zoona kudzera mu kupambana kwa Wokondedwa Wake woona صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم!

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم



www.dawateislami.net

## Ntchito za munthu amene amateteza lilime lake, zimakhalanso zotetezedwa

Sayyiduna Yunus Ibn Ubaid رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Munthu amene amagwiritsa ntchito lilime lake mosamala, ndimamuona akuchita zabwino." *(Al-Samt ma'a Mawsu'ah li Al-Imam Ibn-e-Abi Al-Dunya, buku. 7, tsamba. 63, mawu nambala: 60)*

Okondedwa abale achisilamu, aliyense amene amagwiritsa ntchito lilime lake ngati lumo mosaganiza, ndiye kuti bodza, miseche ndi zina zonse zimachokera kwa iye. Zimakhalanso zovuta kuti munthu amene amayankhula mopitirira muyeso kupewa nthabwala, ndipo palinso mbali ya bodza mu nthabwala. Kumbukirani kuti kunama sikololedwa ngakhale zitakhala nthabwala.

## Kusasangalala kwa Mtumiki Woyera ﷺ ndi munthu amene amanama pozitenga ngati nthabwala

Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Chiwonongeko chili kwa munthu amene amayankhula ndi kumanama kuti anthu aseke. Chiwonongeko chili kwa iye. Chiwonongeko chili kwa iye." *(Tirmizi, buku. 4, tsamba. 142, Hadith: 2322)*

## Kugwera pansi pa Gahena

Mtumiki Omaliza صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Munthu amayankhula ndipo amangochita zimenezo kuti anthu aziseka. Chifukwa cha zimenezi, amagwera pansi penipeni pa Gahena pamene mtunda wake ndi woposa wa kumwamba ndi dziko lapansi. Ndipo kulakwa kumene kumachitika chifukwa cha lilime n'koposa kwambiri kulakwa kumene kumachitika chifukwa cha phazi." *(Shu'ab Al-Iman, buku. 4, tsamba. 213, Hadith: 4832)*



www.dawateislami.net

Sayyiduna 'Allamah Abdul Rauf Munawi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba kuti Imam Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Pamenepa, mfundo yowapanga anthu ena kuseka ikunenedwa mfundo yomwe ili ndi chinthu cha miseche komanso chokhumudwitsa Msilamu (kapena machimo ena); apo ayi, chenjezo ili silikutsutsana ndi nthabwala chabe." *(Fayz Al-Qadeer, buku. 2, tsamba. 425, pansi pa Hadith: 1984)*

## Anthu anthabwala ayenera kumvetsera

Zafotokozedwa mu *Mir'aat*, buku 6, tsamba 463: "Anthu opanga nthabwala a masiku ano, ndi ena otero amene amapeza zofunika pa moyo pochepetsa anthu ndipo malipiro kudzera mu kuwaseketsa anthu, ayenera kuphunzirapo kuchokera m'mawu odalitsikawa." Pansi pa gawo ili la Hadith, 'Kulakwa kumene kumachitika chifukwa cha lilime', zafotokozedwa kuti: "Kutetereka kwa lilime kuli koopsa kuposa kuterereka kwa phazi, chifukwa thupi limavulala phazi likaterereka koma lilime likaterereka, mtima, moyo ndi chikhulupiriro zimavulala. Ndikuterereka kwa lilime kumene kumayambitsa kuphana ndi kukhetsa magazi. Ndkuterereka kwa lilime kumene kumapangitsa munthu kukhala wosakhulupirira. Iblees (Satana) akulangidwabe chifukwa cha kuterereka kwa lilime lake."

## Lamulo pa masewero a nthabwala

Chionetsero cha masewera a nthabwala sichololedwa nkomwe, chifukwa m'menemo mumakhala kunyoza anthu ena kapena anthu owonera amalimbikitsidwa kunyoza anthu ena ndipo zimapweteka mitima ya anthu ambiri. Chimodzimodzinso, kugwiritsa ntchito mawu osonyeza zinthu zonyansa kumapezekanso momweno. Miseche ya anthu apadera kapena kunyoza zizolowezi zawo kumapezekanso kawirikawi. Maonekedwe a anthu opezekapo ndi omwe palibe amanyozedwa, ndipo kuwonjezera pa miseche, nkhani yowanena anthu ena imapitirirabe



www.dawateislami.net

kuchitika. Nthawi zambiri, kusakhulupilira kumachitikanso, Mulungu aletse. Mwachidule, ndikovuta kwambiri kuti chionetsero cha masewero a nthabwala kutichikhale chopanda zinthu zonsezi. Choncho, chionetsero choterechi chidzapatsidwa lamulo chakuti sicholoedwa. Kuchita, kukonza, kuonera, kuwaonetsa ena pulogalamu yotereyi, kulandira ndi kupereka malipiro pa izi, kumvetsera ndi kuwamvetseretsa anthu ena mawu ake ndi kuonera mavidiyo ake, ndi kuifalitsa kuti anthu azionera ndi kuimvetsera, ndi zina zotero ndi Haraam ndipo ndi ntchito zomwe zimatsogolera ku Gahena.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب !        صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Ntchito yokhudzana ndi dziko likubwera iyenera kupangidwa mwachangu

Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Ndi bwino kuchita ntchito iliwonse modekha kungopatula ntchito zokhudzana ndi dziko likubwera ziyenera kuchitidwa mwachangu." *(Abu Dawood, buku. 4, tsamba. 335, Hadith: 481)*

**Kufotokozera Hadith:** Zikutanthauza kuti, ndi bwino kuchedwetsa ntchito yokhudzana ndi dziko lapansi, chifukwa n'zotheka kuti ntchitoyo ndi yolakwika ndipo pamene ikuchedwa, kulakwika kwake kukhoza kudziwika ndipo tingayipewe ntchitoyo, koma ntchito yokhudzana ndi dziko limene likubwera ndi yabwino basi; muyenera kuyigwira mukangopeza mpata, chifukwa poyichedwetsa, mwayiwo ukhoza kutayika. Zimaoneka kwambiri kuti anthu ena akapeza mpata (wokapanga Hajj), samakapanga (panthawiyo). Kenako samatha kukuyipanga pambuyo pake. Allah Wamphamvu zonse wayankhula kuti, "فَاسْتَبِقُوا الْخَيْرٰتِ" *(Kumasulira: Yesetsani kuwaposa anthu ena pa ntchito zabwino.)* *(Gawo 2, Al-Baqarah: 148)*. Satana amamuchedwetsa munthu

kuchita ntchito yabwino ndipo pamapeto pake amamulepheretsa kuchita ntchitoyo. *(Mir`aat Al-Manajih, buku. 6, tsamba. 627, mwachidule)*

## Kuyankhula bwino kumachokera kwa Mulungu ndipo…

Sayyiduna Imam Abu Hamid Muhammad Ibn Muhammad Ibn Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Kuyankhula kwa lilime kumakhudza ziwalo zonse za thupi. Pamene munthu wayankhula zinthu zina zake zabwino, zimakhala chifukwa cha kupereka kumene Mulungu wapereka ndipo ngati wayankhula zoyipa, zimakhala manyazi komanso kunyozeka." *(Minhaj Al-Aabideen (Urdu), tsamba. 142; Minhaj Al-Abideen, tsamba. 65)*

## Tetezani mawu

Munthu wina ananena kuti: "Tetezani maganizo chifukwa amasanduka kukhala mawu. Tetezani mawu chifukwa amasanduka kukhala ntchito. Tetezani ntchito chifukwa zimasintha kukhala khalidwe. Tetezani khalidwe chifukwa limasanduka kukhala umunthu wanu."

## Anthu ena alinso ndi malirime

Musayipitse lilime lanu ndi zonyansa za zolakwika za anthu ena chifukwa inunso muli ndi zolakwika zanu ndipo enanso ali ndi malilime.

## Mulibe zabwino amenewo

Khalifah woyamba wa Asilamu, Sayyiduna Siddiq-e-Akbar رَضِیَ اللّٰہُ عَنْهُ anati: "Mulibe zabwino m'mawu amenewo amene cholinga chake si kukondweretsa Allah Wamphamvu zonse." *(Hilyat Al-Awliya, buku. 1, tsamba. 71, mawu nambala: 82)*

## Pezani malipiro powayitana anthu ena mwaubwino

Kumuyitana munthu ndi mawu akuti 'inu' kapena kufuna chidwi chake motere si makhalidwe abwino. Ngati mukumudziwa dzina lake kapena Kunyah yake, ndi bwino kumuyitana ndi zimenezo chifukwa ndi Sunnah. Ngati simukumudziwa dzina lake, itanani mwaulemu komanso ndi mawu ofanana ndi chikhalidwe cha deralo. Nthawi zonse Msilamu akayitanidwa, kachitidwe koyenera kukhala kabwino kwambiri ndi cholinga chofuna kupeza mphotho yosangalatsa mtima wake, komanso dzina lonse liyenera kutchulidwa. Komanso, malinga ndi nthawi yoyenera, mawu akuti, 'm'bale' kapena 'bambo' ayeneranso kuwonjezeredwa. Ngati wachita Hajj, mawu akuti, 'Haji' ayeneranso kuphatikizidwa.

## Kunena Labbaik poyankha kuyitana kwa munthu wina

Ndi bwino kuti woyitanidwa ayankhe ndi "لَبَّيْك" (ndilipano). Komabe, zinthu ziyenera kuwunikiridwa kuti mwina pakunena kwanu "لَبَّيْك", munthu winayo akhoza kusokonezedwa. Mwa chisomo cha Allah Wamphamvu zonse, mu chikhalidwe chachipembedzo cha Dawat-e-Islami, wina akayitanidwa, "لَبَّيْك" amagwiritsidwa ntchito poyankha nthawi zina, amena amamveka mokondweretsa m'makutu ndipo amatha kubweretsa chisangalalo mumtima mwa Msilamu. Bambo wolemekezeka a A'la Hazrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, 'Allamah Naqi Ali Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba kuti: "Aliyense akamuyitana Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, iye amkayankha ndi "لَبَّيْك" (ndilipano)." *(Suroor Al-Quloob, tsamba. 182)*



www.dawateislami.net

Pakuyitana kwa Mtumiki Omaliza wa Allah, Sayyiduna Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, masahaba odalitsika رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُم kuyankha ndi Labbaik kwafotokozedwa m'mahadith opatulika. Kupatula zimenezi, umboni wake ukupezekanso mu ntchito ya Allah Wamphamvu zonse. Choncho, nthawi zonse pamene munthu wina akufuna chidwi cha mtsogoleri wamkulu wa mamiliyoni achi Hanbali, Sayyiduna Imam Ahmad Ibn Hanbal رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه kupita kwa iye mwini pofuna kudziwa lamulo, nthawi zambiri ankanena "لَبَّيْك". *(Manaqib İmam Ahmed bin Hanbal Al-Juozi, tsamba. 298)*

Zanenedwanso m'buku lodziwika bwino lomwe lili ndi madua omwe amapezeka mu Sunnah lotchedwa, 'Hisn-e-Haseen': "Pamene wina wake wakuyitanani, yankhani ndi "لَبَّيْك"." *(Hisn-e-Haseen, tsamba. 104)*

O Allah Wamphamvu Zonse, tipatseni kuthekera ife kowayitana Asilamu ndi mayina abwino ndikupeza mphoto yokondweretsa mitima yawo!

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

## Munthu amene amangopanga nthabwala amataya mbiri yabwino

Khalifah wachiwiri wa Asilamu, Sayyiduna Umar Farooq A'zam رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anati: "Munthu, amene nthabwala, amataya mbiri yabwino." *(Ihya Al-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 389; Ihya al-'Uloom, buku. 3, tsamba. 158)*

## Chifukwa chimodzi chimene chimayambitsa udani

Sayyiduna Umar Ibn Abdul Aziz رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Musapange nthabwala ndi kusekana wina ndi mnzake, chifukwa mukamachita zimenezi (kwinaku mukuseka), chidani chimalowa mumtima." *(Seerat Ibn-e-Abdul Hakam, tsamba. 114)*



www.dawateislami.net

## Nthabwala zimayambitsa udani

Sayyiduna Imam Muhammad Ibn Muhammad Ibn Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Zanenedwa kuti chilichonse chili ndi mbeu ndipo mbeu ya chidani ndi kuchita nthabwala. Ndipo zimanenedwanso kuti kuchita nthabwala kumaba nzeru komanso kumapangitsa abwenzi kugawikana."

*(Ihya Al-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 392; Ihya Al-'Uloom, buku. 3, tsamba. 159)*

O Allah Wokondedwa komanso Wamphamvu zonse, titetezeni ife kuti tisamanyoze anthu ndikupanga nthabwala zopweteketsa mtima, ndipo mutipatse chidwi cholemekeza Asilamu.

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

## Tanthauzo la machimo akuluakulu

Mu *Sirat-ul-Jinan*, buku 9, pa tsamba 567, zafotokozedwa mu ndemanga ya gawo lotsatirali la vesi 32, gawo 27, Surah al-Najm:

اَلَّذِيْنَ يَجْتَنِبُوْنَ كَبٰٓـئِرَ الْاِثْمِ وَ الْفَوَاحِشَ

*Anthu amene amapewa machimo akuluakulu komanso zinthu zoyipa,*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 27, Surah Al-Najm, vesi 32)*

Tchimo ndi ntchito imene wochita wake akuyenera kulangidwa, kapena mukhoza kunena kuti kuchita ntchito yosaloledwa kumatchedwa tchimo. Mulimonse momwe zingakhalire, pali mitundu iwiri ya machimo: 1) ang'onoang'ono 2) akuluakulu. Tchimo lalikulu ndi limene limati likachitidwa Hadd imaperekedwa m'dziko (kutanthauza kuti chilango chimaperekedwa molingana ndi lamulo la Shari'ah), mwachitsanzo, kupha, chigololo ndi kuba ndi zina zotero, kapena pali chenjezo la chilango pa ilo ku Dziko likubwera, mwachitsanzo, miseche, kunena zonyoza anthu ena, kudzigomera ndi kudzionetsera ndi zina zotero. Ndipo Fawahish (zonyansa) kuphatikizapo mawu aliwonse onyansa,



www.dawateislami.net

kuchita ndi machimo onse ang'onoang'ono ndi akuluakulu. Komabe, pamenepa (kutanthauza kuti mu gawo ili la vesi), Fawahish (zonyansa) zimatanthauza machimo akuluakulu amene zoyipa zake ndi chisokonezo chake ndi chachikulu kwambiri, mwachitsanzo, kuchita chigololo, kupha ndi kuba ndi zina zotero. *(Khazin, buku. 4 tsamba. 196-197; Mudarik, tsamba. 1181; Abu Sa'ud buku. 5 tsamba. 648)*

## Tanthauzo la kudzigomera

Odzipereka a Rasool, mu ndemanga yomwe yatchulidwa pamwambayi, kudzigomera kwatchulidwanso pakufotokozera machimo. Kudzigomera kumatchedwa *'Ujub'* mu Chiarabu. M'buku la masamba 352 la Maktaba-tul-Madinah, *'Batini Bimariyon ki Ma'lumaat',* tanthauzo lotsatira la Ujub ndiko kuti kudzigomera kwalembedwa pa masamba 36 ndi 37: "Kudzichemelera za kupambana kwa munthu (mwachitsanzo, m'maphunziro, ntchito zabwino kapena chuma) kwa munthu mwiniyo ndipo opanda kuopa kuti zimenezi zidzatha. Zili ngati kuti munthu wodzigomera amayiwala kupereka mtendere woperekedwa kwa Wopereka weniweni wa m'dalitso (amene ndi Allah Wamphamvu zonse). (Zikutanthauza kuti, poganizira za m'dalitso opatsidwa, mwachitsanzo, thanzi kapena kukongola ndi chisomo kapena chuma kapena nzeru kapena mawu abwino kapena udindo, ndi zina zotero, kuti ndikupambana kwa munthu chabe ndikuyiwala kuti zonsezi ndi mphatso ya Allah Wamphamvu zonse yekha ndipo nthawi iliyonse Allah Wamphamvu zonse akafuna, akhoza kutenganso kupambana kopatsidwa kapena ubwino umene unaperekedwawo.)

*(Batini Beemariyon ki Ma'lumat, tsamba. 36-38; İhya al-'Uloom, buku. 3, tsamba. 404)*

## Ntchito zabwino za zaka 70 zimawononongeka

Kudzigomera kumawononga kwambiri zabwino; monga momwe

Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anafotokozera kuti: "Ujub (kudzigomera) kumawononga ntchito zabwino za zaka zokwana 70."

*(Jami'-us-Sagheer, tsamba. 127, Hadith 2074)*

## Mlandu waukulu kwambiri kuposa tchimo

Pewani kuipa kwa kudzigomera kukuchenjezedwa, Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Ngakhale mutapanda kupanga tchimo, koma kwa inu, ndikuwopera mlandu waukulu kuposa tchimo, ndipo ndi Ujub (kudzigomera)." *(Shu'ab-ul-Iman buku. 5 tsamba. 453, Hadith 7255)*

Mu mawu odalitsikawa, iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananena kuti kudzigomera ndi tchimo lalikulu kwambiri. *(Ihya-ul-'Uloom buku. 3 tsamba. 453)*

Ndipo ndikofunika kuti Msilamu apewe machimo onse oonekera ndi obisika. Allah Wamphamvu zonse wanena mu Qur'an Yopatulika, gawo 8, Surah al-An'aam, vesi nambala 120:

وَذَرُوْا ظَاهِرَ الْاِثْمِ وَبَاطِنَهٗ ؕ

*Ndipo siyani machimo owonekera ndi obisika;*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 8, Surah Al-An'am, vesi 20)*

## Kufotokozera kofunikira kokhudzana ndi kudzigomera

Sayyiduna Imam Abu Hamid Muhammad Ibn Muhammad Ibn Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba kuti: "Aliyense amene amadziona kuti ndi wopambana kudzera m'maphunziro, ntchito komanso chuma, iye amakhala ndi zinthu ziwiri:

1. Chimodzi mwa izo ndi chakuti iye amaopa kuluza kupambana kumeneko ndipo amaopa kuti kusintha kwina kudzapezeka pa ubwino umenewo kapena kudzatheratu . Choncho, munthu



www.dawateislami.net

wotere si wodzigomera.

2. Chinthu chachiwiri ndi chakuti saopa kuchepa kapena kuchiluza kwake, koma amakhutira ndi kusangalala ndi chakuti Allah Wamphamvu zonse wamupatsa m'dalitso umenewu ndipo si mwa mphamvu zake ayi. Kumenekunso si kudzigomera. Ndipo kwa iye, kulinso chinthu chachitatu, chomwe ndi kudzigomera, ndipo ndichakuti: iye samaopa kuluza kapena kuchepa kwa kupambana kumeneko, koma amakhutira ndi kusangalala ndi kupambanako, ndipo chifukwa cha chisangalalo chimenecho ndi chakuti kupambana kumeneku ndi chisomo, madalitso ndi chipambano. Sasangalala chifukwa chakuti ichi ndi choperekedwa ndi chisomo cha Allah Wamphamvu zonse, komano chifukwa cha chisangalalo chake (cha munthu wodzigomera) ndi chakuti amakuona kupambana kumeneku ngati ubwino wake komanso kupambana kwake kokha. Samakuona ngati koperekedwa komanso m'dalitso wa Allah Wamphamvu zonse.” *(İhya-ul-‘Uloom, buku. 3 tsamba. 454)*

## Mankhwala otsimikizirika ochizira kudzigomera

Imam Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: “Ngakhale kuti anali odziletsa ndi ochita zabwino, Masahaba odalitsika رَضِىَ اللهُ عَنْهُم amkalakalaka kuti anakakhala mchenga, mankhusu kapena mbalame. Nanga, munthu wanzeru angamazigomere bwanji pa ntchito zake kapena kudzitama pa zokhudza ntchito zake, ndipo angakhale bwanji wosaopa Nafs yake? Awa ndi machiritso a kudzigomera amene amapangitsa maganizo a kudzigomera kutheratu. Pamene munthu ali ndi vuto la kudzigomera ayenera kuchiritsa molingana ndi njira imeneyi, choncho kudzigomera kwadzaza mu mtima mwake, pa nthawiyo, mantha oluza m'dalitso amamulepheretsa kudzitamandira. Ndipotu, pamene akuona osakhulupirira ndi ochita zolakwa kuti popanda tchimo lililonse,

sanapatsidwe chuma cha Chikhulupiriro ndi kumvera Allah Wamphamvu zonse, choncho amawopa ndi kuganiza kuti Wamphamvu zonse amene samasamala za kulanda wina popanda cholakwa chilichonse kapena kupatsa wina popanda mkhalapakati, ndiye Iye angathenso kutenga m'dalitso umene wapereka. Ambiri mwa okhulupirira, atatembenukira ku chipembedzo china, ndipo omvera malamulo (Asilamu ochita zabwino) pambuyo pokhala ophwanya malamulo, anakhala ndi mathero oyipa. Pamene munthu akuganiza motere, ndiye kuti kudzigomera sikudzakhalanso mwa iye.” *(İhya-ul-‘Ulom (Urdu), buku. 3, tsamba. 1106; İhya-ul-‘Uloom, buku. 3, tsamba. 458)*

*Hubb-e-Jah-o-Khud Pasandi Ki Mita Day Adatayn*

*Ya Ilahi, Bagh-e-Jannat Ki ‘Ata Kar Rahatayn*

اٰمِیْن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِیّٖن صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم

## Zinthu 8 zoyambitsa kudzigomera komanso machiritso ake

Imam Abu Hamid Muhammad Ibn Muhammad Ibn Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza zinthu 8 zotsatirazi zoyambitsa kudzigomera komanso machirritso ake mu *Ihya al-Uloom*:

1. Choyambitsa choyamba: Kudzigomera chifukwa cha kukongola kwa thupi. Machiritso ake ndiakuti munthuyo aganizire za zonyansa zake zamkati ndi kuganizira za chiyambi chake ndi mapeto ake (anali dontho losayera pachiyambi ndipo adzakhala mtembo wowola pamapeto pake).

2. Choyambitsa chachiwiri: Kudzigomera chifukwa cha mphamvu ndi kulimba kwa thupi. Machiritso ake ndiakuti munthuyo aganizire kuti Allah Wamphamvu zonse angatengenso



www.dawateislami.net

mphamvuyi pongomupatsa vuto laling'ono (mwachitsanzo, matenda, ngozi, ndi zina zotero).

3. Choyambitsa chachitatu: Kudzigomera chifukwa cha nzeru zake. Machiritso ake ndiakuti munthuyo aganizire kuti madalitso amenewa akhoza kutengedwa chifukwa cha matenda kapena ngozi iliyonse.

4. Choyambitsa chachinayi: Kudzigomera chifukwa chokhala ochokera ku banja lolemekezeka. Machiritso ake ndiakuti munthuyo aganizire momwe angafikire pamene pali makolo akepo opanda kupanga ntchito zabwino ngati momwe iwo anapangira ntchito zabwino.

5. Choyambitsa chachisanu: Kudzitamandira chifukwa cha chithandizo cha wopondereza komanso kusapereka kufunikira kwa kuyanjana ndi anthu achipembedzo komanso anthu ophunzira bwino. Machiritso ake ndiakuti munthuyo ayenera kuyang'ana chiwonongeko cha anthu oponderezawo pa Tsiku Lomaliza ndikuganizira kuti oponderezawo akuyenera mkwiyo wa Allah Wamphamvu zonse.

6. Choyambitsa chachisanu ndi chimodzi: Kudzitamandira chifukwa cha antchito ake. Machiritso ake ndiakuti munthuyo ayenera kuona kufooka kwake ndi kukhazikitsa m'maganizo mwake kuti anthu onse ndi akapolo odzichepetsa a Allah Wamphamvu zonse.

7. Choyambitsa chachisanu ndi chiwiri: Kudzitamandira chifukwa cha chuma ndi kulemera. Machiritso ake ndiakuti munthuyo ayenera kuyang'ana mavuto a chuma ndi kulemera, ufulu wake ndi masautso amene amabwera chifukwa cha izo.



www.dawateislami.net

8. Choyambitsa chachisanu ndi chitatu: Kudzitamandira chifukwa cha maganizo olakwika', machiritso ake ndiakuti munthuyo asadalire kulondola kwa maganizo ake (ayenera kuganizira kuti maganizo ake akhoza kukhala olakwika).

*(Batini Beemariyon ki Ma'lumat, tsamba. 38-43;*

*Ihya`-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 1107-1119 mwachidule)*

## M'nyamata wochita zoyipa anayamba kusintha

Inu omukonda Rasool, kuti mudziwe zambiri za kudzigomera ndi zoyipa zina, thetsani chizolowezi chochita machimo ndikuwonjezera chilakolako chochita zabwino, nthawi zonse khalani m'malo a zochitikachitika za chipembedzo a bungwe la Dawat-e-Islami. Mu bungwe lachipembedzo la Dawat-e-Islami, anthu oipa amasintha. Ndingokuuzani chodabwitsa cha Madani pankhani iyi: Mnyamata wina wokhala ku Lahore, Punjab anali wokonda kwambiri masewera. Kuyambira m'mawa mpaka madzulo, chinthu chokhacho chomwe amachita chinali kusewera masewera. Abambo ake, omwe analinso Imam wa Mzikiti, amamulangiza kwambiri koma sanasiye. Kukonda masewera kunawonjezeka kwambiri moti anayambanso, Allah aletse, kutchova njuga. Kuwonjezera pa bwalo lamasewera, chinali chizolowezi chake chokonda kuyendayenda m'misewu ndi m'misika ndi abwenzi mpaka pakati pa usiku komanso kuchezera malo ogwiritsira ntchito intaneti. Analibe chizolowezi choyankhula zoona, chifukwa chake, akafika kunyumba mochedwa usiku, ankanamanso chifukwa chimene wachedwera. Kusintha komwe kunachitika m'moyo wake kunali kwakuti abambo ake anafotokoza zokhudzana ndi khalidwe lakeli kwa m'bale wina wachisilamu amene amatenga nawo gawo mu zochitika za chipembedzo za bungwe la Dawat-e-Islami ndipo anamupempha kuti amusinthe. Chifukwa cha khama la m'bale wachisilamuyo, atapita ku msonkhano wolimbikitsa Sunnah kawiri kapena katatu, anapita ku Madani Qafilah kwa masiku atatu kukaphunzira ndi kuphunzitsa Sunnah. M'gulu la anthu okonda Rasool,



www.dawateislami.net

anaphunziramo ma Sunnah omwe kale samkawadziwa. Atabwerera kuchokera ku Madani Qafilah, anatsimikiza mu mtima kukhala moyo wake m'deralo ngati munthu wamakhalidwe abwino komanso wochita zabwino. Mwachifundo cha Allah Wamphamvu zonse, analowa nawo m'malo a zichitochito za chipembedzo a Dawat-e-Islami.

*Rab kay dar per jhukayn, iltija`ayn karayn*

*Bab-e-Rahmat khulay, qafilay mayn chalo*

*(Wasa`il-e-Bakhshish, tsamba. 671)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Zoyankhula zinayi za Mtumiki Woyera ﷺ zokhudza mawu onyansa

Amene amayankhula mawu onyansandi munthu wopanda manyazi (wopanda ulemu komanso wopanda mantha) ndipo kuluza kwake kwakukulu ndi kwakuti Allah Wamphamvu zonse ndi Mtumiki Wake Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم samakonda munthu woteroyo, ndipo malo ake okhala munthu wopanga zonyansa ndi Gahena. Mvetserani zoyankhula zinayi za Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم pa nkhani imeneyi ndipo mutengepo phunziro:

1. Mawu onyansa ndi nthambi ya makhalidwe oyipa ndipo makhalidwe oyipa amatsogolera ku Gahena. *(Tirmizi, buku. 3, tsamba. 406, Hadith 2016)*

2. Ntchito zoyipa ndi zoyankhula zoyipa (zonyansa) zilibe gawo m Chisilamu. *(Masnad Ahmad Bin Hanbel, buku. 7, tsamba. 431, Hadith 20997)*

3. Mayankhulidwe onyansa ndi kuyankhula zoyipa sizimakondedwa ndi Allah Wamphamvu zonse. *(Muslim, tsamba. 920, Hadith 5659)*

4. Zikanakhala kuti mawu onyansa ali m'maonekedwe ngati a munthu, akanakhala m'maonekedwa a munthu woyipa. *(Al-Samt Ibn-e-Abi Al-Dunya ma' Mausu'ah, buku. 7, tsamba. 206, Hadith: 331)*

## Lilime loyipa ndi matenda oopsa

Tabi'i woyera mtima, Sayyiduna Ahnaf Ibn Qais رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه Ananena kwa anthu kuti, "Kodi ndikuuzeni za matenda oopsa kwambiri?" Anthu anati, 'Inde.' Iye anati, 'Makhalidwe oyipa ndi lilime loyipa ndi matenda oopsa kwambiri.'" *(Adab Al-Dunya wal-deen, tsamba. 383)*

O Mbuye wa Mustafa, kudzera m'makhalidwe abwino a khalifah wachitatu wa Asilamu, Sayyiduna Usman Ghani رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ, tetezeni ife kuchokera zoyankhula zoyipa komanso ntchito zoyipa.

اٰمِیْن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِیّٖن صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم

## M'maonekedwe a galu

Sayyiduna Ibrahim Ibn Maisarah رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Zimanenedwa kuti munthu amene amayankhula zinthu zonyansa adzabwera pa Tsiku la Chiweruzo m'maonekedwe a galu." *(Al-Samt li Ibn-e-Abi Al-Dunya ma'a Mausu'ah, buku. 7, tsamba. 205, mawu nambala: 329)*

## Tanthauzo la mawu onyansa

Ndi amwayi otani abale ndi alongo achisilamu amene amagwiritsa ntchito malilime awo pokhapokha pa kukamba mawu abwino ndikufalitsa kuyitanira anthu mochuluka ku chilungamo. Kalanga! Masiku ano, sipangakhale misonkhano ya anthu yopanda mawu onyansa, kotero kuti ngakhale anthu owonekera mu zovala zachipembedzo nthawi zambiri sangathe kuzipewa. Mwina, anthu ambiri samadziwa ngakhale kuti mawu



www.dawateislami.net

onyansa ndi chiyani. Choncho, mvetserani tanthauzo lotsatira la mawu onyansa: “اَلتَّعۡبِيۡرُ عَنِ الۡاُمُوۡرِ الۡمُسۡتَقۡبَحَةِ بِالۡعِبَارَاتِ الصَّرِيۡحَةِ” kufotokoza zinthu zochititsa manyazi ndi ntchito m’mawu omveka bwino. *(Ihya-ul-‘Uloom, buku. 3, tsamba. 151)* Choncho, achinyamata amene amayankhula zinthu zonyansa ndi cholinga chokwaniritsa ‘chilakolako chawo ’, m’malo mwake, amakhutira ndi kuzimvera, amene amayankhula mawu achipongwe, kuchita zizindikiro zopanda manyazi, kusangalala ndi zizindikiro zonyansazi komanso amene amaonera mafilimu ndi masewero kuti apeze chisangalalo chonyansa (monga mwachizolowezi, zodzaza ndi zonyansa), ayenera kuwerenga nkhani yochititsa chisoniyi mobwerezabwereza ndi kunjenjemera ndi mantha a Ambuye Wamphamvu zonse. Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: “Paradaiso ndiyoletsedwa kwa munthu amene amagwiritsa ntchito zonyansa (mawu kapena ntchito zosayenera)).” *(Al-Samt, buku. 7, tsamba. 204, Hadith, 325)*

Anthu amene amaganizira kwambiri za manong'onong'o a satana onyansa okhudza akazi omwe sali a Mahram kapena anyamata okongola opanda ndevu, amadzilowetsa okha m'maganizo ochititsa manyazi ndipo, Allah aletse, omwe amasangalala poganizira 'zichitochito zoyipa', ayenera kutenga uphungu kuchokera m'nkhani yomwe tafotokoza m'mwambayi. *(Siraj-e-Munir Sharah Jami’ah-us-Sagheer, buku. 3 tsamba. 84)*

*Aa’ayn na mujh ko waswasay aur ganday khayalat*

*Allah nikal ja`ye har ik dil say buri baat*

صَلُّوا عَلَى الۡحَبِيۡب !　　صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد



www.dawateislami.net

## Mfundo 8 za Madani zokhudzana ndi kuyankhula bwino

1. Ndi Sunnah kuyankhula ukumwetulira komanso ndi nkhope yosangalala.

2. Poyankhula, khalani ofewa kwa ana ndi ulemu kwa akulu. Ngati Allah Wamphamvu zonse afuna, mudzalemekezedwa ndi onse awiri.

3. Si Sunnah kuyankhula mokuwa.

4. Sikoyenera kuomberana m'manja pamene mukuyankhula, chifukwa zimatsutsana ndi machitidwe a anthu olemekezeka ndi otukuka. (Sirat-ul-Jinan, buku. 7, tsamba 502 – 503)

5. Pamene mukuyankhulana, kukanda mphuno mobwerezabwereza pamaso pa ena, kuyika chala m'mphuno kapena m'makutu, kulavula, kuchotsa dothi pa thupi, ndi kukhudza kapena kukanda ziwalo zobisika sizabwino. Zinthu izi siziyenera kuchitidwa mosafunikira ngakhale pa malo obisika.

6. Pamene munthu winayo akuyankhula, tiyenera kupewa kuyang'ana uku ndi uku ndikumvetsera modekha kwinaku tikupereka chidwi chathu chonse kwa iye. Tisayankhulenso mkatikati moyankhula, chifukwa kumusokoneza wina kumatsutsana ndi makhalidwe abwino. Mtumiki Wokondedwa komanso Omaliza wa Allah Wamphamvu zonse Sayyiduna Muhammad صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم samkasokoneza aliyense. Komabe, ngati munthu wina watsala pang'ono kudutsa malire, amkamuletsa kapena kuchoka pamalopo. *(Shama`il Tirmizi, tsamba. 200 mwachidule)*

7. Musamamutsanzire munthu amene amalephera kuyankhula kapena amene sayankhula bwino akakhala palibepo, chifukwa kutero ndikuchita miseche, ndipo kumutengera pamaso pake chimakhalanso chifukwa chimene chomukhumudwitsira.



www.dawateislami.net

8. Kuyankhula mopitirira muyeso ndi kuseka mokweza pamene mukuyankhula kumapangitsa kuti ulemu ndi mantha zichepe.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Zinthu 15 zaphindu m'dziko lapansi komanso dziko limene likubwera

1. Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafunsidwa kuti, "Munafika bwanji pa ulemerero umenewu?" Iye anayankha kuti, "Poyankhula zoona, kukwaniritsa chikhulupiriro ndikusiya zinthu zopanda pake.." *(Hilyat Al-Awliya`, buku. 6, tsamba. 358, Hadith, 8925; Allah Walon ki Baatayn, buku. 6, tsamba.462)*

2. Imam Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Chinthu chimene chimanenedwa (kwa wina ndi cholinga chomukonza) pamaso pa anthu, chimatengedwa ngati chitonzo ndi kunyozetsa, koma chonenedwa (pofuna kumusintha munthu wina) kwa iye yekha chimatengedwa ngati chikondi ndi uphungu." *(Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 2, tsamba. 659)*

3. Zinthu zinayi zimabweretsa zinthu zinayi: 1) Kukhala chete kumabweretsa chitetezo 2) Kuchita zabwino kumabweretsa ulemu 3) Kupereka kumabweretsa utsogoleri ndipo 4) Kuyamika kumabweretsa kuchulukitsidwa kwa madalitso. *(Deen-o-Dunya ki Anokhi Baatayn, buku. 1, tsamba. 84)*

4. Zoyankhula za munthu zimasonyeza ubwino wake komanso zimayimira nzeru zake. Choncho, yankhulani zochepa komanso zabwino zokhazokha. (Izi zikutanthauza kuti, nzeru za munthu zimadziwika ndi mmene amayankhulira. Choncho, ayenera



www.dawateislami.net

kuyankhula pang'ono kuti chophimba chikhalepobe, chifukwa popitiriza kuyankhula kwambiri, kupusa kwake kungaonekere.)

5. Munthu amadziwika kudzera mu zokambirana zake ndipo amatchuka ndi zochita zake. Choncho, nenani zolondola (ndipo chitani zinthu zabwino zokha).

6. Aliyense amene amazidziwa yekha, amasunga lilime lake, samachita zinthu zopanda pake ndipo sanyoza m'bale wake wachisilamu, amakhala wotetezeka mpaka kalekale ndipo kawirikawiri samanyozeka.

7. Khalani chete ndipo nenani zoona chifukwa kukhala chete ndi chitetezo ndipo kunena zoona kumabweretsa ulemu.

8. Amene amayankhula kwambiri, anthu anzeru amamupewa ndi kumuthawa.

9. Amene amayankhula zoona pazokambirana zake, makhalidwe ake abwino amachulukira.

10. Kukhala chete kobweretsa chitetezo ndi kwabwino kuposa kuyankhula kobweretsa kunyozeka.

11. Munthu amene amayankhula mawu osayenera amamva zinthu zosasangalatsa.

12. Bala la lilime ndi lovuta kwambiri kuposa bala la lupanga.

13. Kukhala chete pa mawu achipongwe ndi opweteka a munthu wosazindikira ndi yankho labwino kwambiri kwa iye ndipo kumayambitsa ululu waukulu kwa munthu wosazindikirayo.

14. Lilime ndi lupanga lakuthwa lomwe kuukira kwake sikungatheke kupewa, ndipo kuyankhula ndi muvi womwe watulutsidwa womwe



www.dawateislami.net

sungatheke kubwezeretsedwa. *(Deen-o-Dunya ki Anokhi Baatayn, buku. 1, tsamba. 85-88, ndi zosintha zochepa)*

15. Musauze aliyense chinsinsi chanu, chifukwa chinthu chomwe sichingabisidwe ndi milomo iwiri sichingakhale chobisika malo ena aliwonse.

## Malangizo 50 opatsa chidwi

Mfundozi zatengedwa kuchokera pa masamba ochezera a pa Intaneti, ndi zina zotero, ndipo zafotokozedwa ndi kusintha pang'ono.)

1. Ulusi wautali ndi lilime nthawi zambiri zimakodwa. Nchifukwa chake, muyenera kusunga ulusiwo utapindidwa ndipo lilime libwenzedwe m'mbuyo.

2. Matenda a shuga amabwera chifukwa chodya zotsekemera, osati chifukwa choyankhula mokoma.

3. Pamene mpeni, chikwanje, muvi ndi lupanga zinakhala pansi kumaganiza za chomwe chimapweteka kwambiri, panthawiyo, mawu anali atakhala kumbuyo akumwetulira (kutanthauza kuti mabala a mawu ndi akuya kwambiri).

4. Pa zinthu zimene anthu amamenyana ndi kumakwiriridwa pansi pa milu ya mchenga, akhoza kuponyapo mchenga pang'ono (kukhululukira ndi kuiwala) n'kukhala ndi moyo wabwino padziko lapansi.

5. Kupha sikuchitika ndi mpeni wokha komanso ndi mawu. Si chipolopolo chokha chimene chimapha, komanso khalidwe (loyipa) limabweretsa imfa. Ndithudi, chipolopolo ndi mpeni zimathetsa ubale ndi dziko, koma kubaya kwa mawu ndi kumenya kwa khalidwe kumakhala chingwe pakhosi ndipo sizilola munthu kukhala ndi moyo kapena kufa.



www.dawateislami.net

6. Yankhulani pokhapokha ngati mawu anu ali opindulitsa komanso okongola kuposa kukhala chete kwanu.
7. Mbalame ya mtundu wa chinkwe imayankhula mawu okoma ngakhale itadya tsabola, pamene munthu nthawi zambiri amayankhula mawu owawa ngakhale atadya zotsekemera.
8. Ngakhale poizoni wa munthu amene amayankhula mawu okoma amagulitsidwa, pamene ngakhale uchi wa munthu amene amayankhula mawu owawa sugulitsidwa.
9. Monga momwe mumasankhira zipatso zokoma pogula zipatso, momwemonso, sankhani mawu okoma poyankhula.
10. Monga momwe mabowo ang'onoang'ono m'chipinda chotsekedwa amaonetsera kutuluka kwa dzuwa, momwemonso, zinthu zazing'ono zimaonetsa khalidwe la munthu.
11. Mosakayikira, mawu alinso ndi kufunika kwake, koma nthawi zina, chikoka cha kamvekedwe chimakhala chachikulu kwambiri.
12. Nthawi zonse yankhulani mawu okoma, chifukwa ngati mutayenera kuwatenga kubwerera kwa inu nthawi ina, simudzawapeza owawa.
13. Mayankho a mafunso ena saperekedwa ndi lilime koma ndi nthawi, ndipo mayankho operekedwa ndi nthawi ndi osatsutsika.
14. Amanena kuti, 'Ubalewo unatha chifukwa cha kachinthu kakang'ono ngakhale kuti nthawi zina, kuseli kwa 'kakang'ono kalikonseko', kumakhala zinthu zina zambiri ndipo kakang'ono kalikonseko ndi malire omalizira a kupirira.
15. Munthu amabisika kumbuyo kwa lilime lake; ngati mukufuna kumudziwa bwino, mulole kuti ayankhule.
16. Mawu alibe mano koma amaluma ndipo akaluma, bala lake silichira mophweka.



www.dawateislami.net

17. Nthawi zina, anthu amayankhula chinthu chotentha mu kamvekedwe kofewa kotero kuti moyo wonse umadutsa kuti kutentha kwa mawu amenewo kuzizire (kutanthauza kuti kuwayiwala).
18. Pamene nzeru zachepa, lilime limatalika.
19. Pamene makina achita dzimbiri, zitsulo zimayamba kupanga phokoso ndipo pamene nzeru zachita dzimbiri, lilime limayamba kuyankhula mawu opanda pake.
20. Ganizirani bwino musanayankhule, chifukwa mawu anu angathenso kuswa mtima wa munthu kwambiri.
21. Mfundo imamveka ndikukhazikika mumtima kudzera m'mawu oyankhulidwa mokoma chifukwa nthawi zina matsenga amakhala ochepa m'mawu ndipo amakhala ambiri m'kamvekedwe.
22. Aliyense amadziwa kuyankhula koma nzeru za wina zimayankhula ndipo makhalidwe a wina amayankhulanso.
23. Kukambirana ndi ntchito yomwe kudzera m'menemo munthu amatha kulowa mumtima mwa munthu kapena kuchoka mumtima mwa munthu.
24. Mawu ochepa okoma, mawu ochokera pansi pa mtima komanso mawu a ulemu angatsitsimutse mtima wa munthu.
25. Mawu odzikuza komanso oopsa nthawi zina amakhala okwanira kupha munthu pang'onopang'ono.

26-27 Sonkhanitsani uchi wa dziko lonse koma mawu amodzi okoma ochokera pa lilime ndi okoma kwambiri kuposa (uchi wa dziko lonsewo), ndipo sonkhanitsani poizoni wa dziko lonse koma mawu amodzi owawa ochokera pa lilime ndi owawa kwambiri kuposa (poizoni yenseyo).



www.dawateislami.net

28. Kuteteza lilime lanu kuchokera ku mawu owawa ndi chipambano chachikulu.

29. Dziko lonse lingagonjetsedwe kudzera mu chikondi ndi mawu ofewa.

30. Ngakhale lilime ndi laling'ono kukula kwake koma anthu ochepa kwambiri amatha kulilamulira.

31. Pongoteteza lilime lanu, mutha kupewa zovuta zambiri.

32. Ngati mukufuna kusintha munthu, chitani mokoma chifukwa mawu okoma amayambitsa chilakolako chosinthika, pamene mawu olimba amachititsa kuuma mtima.

33. Yankho la zinthu zina ndi kukhala chete chokha, ndipo kukhala chete ndi yankho labwino kwambiri.

34. Mbalame zimagwidwa chifukwa cha mapazi awo ndipo anthu amagwidwa, chifukwa cha malilime awo.

35. Khalani ofewa pokambirana; kamvekedwe kali ndi chikoka chachikulu kuposa mawu.

36. Ngati supuni yadetsedwa, imatha kuyeretsedwa ndi madzi pang'ono koma ngati lilime lili lodetsedwa, ngakhale madzi a nyanja zisanu ndi ziwiri sangayeretse.

37. Ngati wina wayika poizoni m'chakudya, mankhwala ake ndi otheka, koma ngati wina wayika poizoni m'khutu, kulichiza kwake kumakhala kovuta kwambiri.

38. Lipangeni lilime lanu kukhala ndi chizolowezi chonena Salam kwa Asilamu. Kudzera mu izi, abwenzi amachulukirachulukira ndipo adani amachepa.



www.dawateislami.net

39. Lilime la mwana nthawi zambiri limawulula chinsinsi cha khalidwe labwino kapena loyipa la munthu.

40. Nthawi zonse kusamala kuyenera kukhalapo ngakhale pa zinthu zazing'ono chifukwa munthu samangogwa pa mapiri pokha ayi komanso pa miyala.

41. Kuganiza molakwika ndi kuyankhula mosakhala bwino ndi zolakwa ziwiri zomwe zingasandutse kupambana konse kwa munthu kukhala kuluza.

42. Chikondi chachikulu chimabwera chifukwa chosamalira zinthu zazing'ono.

43. Sungani lilime lanu, ngati Allah Wamphamvu zonse akufuna, mudzapeza ulemu; apo ayi, konzekerani kukhala onyozeka.

44. M'malo mokweza mawu anu, kwezani umboni wanu. Maluwa amaphuka chifukwa cha mvula osati chifukwa cha kubangula kwa mitambo.

45. Kunama kamodzi kungabweretse funso pa kunena kwanu zoona mpaka kalekale.

46. Munthu wanzeru sayankhula mpaka aliyense atakhala chete.

47. Musataye chilimbitso pambuyo pakumva mawu odzudzula. Phokoso limapangidwa ndi owonerera, osati osewera.

48. Ngati simungathe kusangalatsa munthu mwa pomupatsa ndalama, ndiye kuti musangalatseni poyankhula mawu ochepa okoma.

49. Nthawi zonse muziapangira anthu zabwino. Ngati Allah Wamphamvu zonse akufuna, ulemu wanu udzakhala wosatha m'mitima.



www.dawateislami.net

50. Mundiuze zolakwa zanga ndekha ndi cholinga choti ndizikonze; Ine ndilibe nthambi ina iliyonse.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب!    صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Miyambi 19 ya chiarabu (ndi kumasulira m'Chichewa) yokhudzana ndi lilime mogwirizana ndi zilembo 19 za بِسْمِ اللهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم

1. "خَيْرُ الْكَلَامِ مَا قَلَّ وَدَلَّ" (Mawu abwino kwambiri ndi amene amakhala afupi komanso otsimikizika.).
2. "عَيْبُ الْكَلَامِ تَطْوِيْلُهٗ" (Kutalikitsa zokambirana (mosafunikira) ndi cholakwika cha zoyankhula).
3. "بَلَاءُ الْاِنْسَانِ مِنَ اللِّسَانِ" (Munthu amakumana ndi mayesero chifukwa cha lilime).
4. "لِسَانُكَ دَاءٌ مَا لَهٗ دَوَاءٌ" (Kugwiritsa ntchito lilime lanu molakwika ndi matenda omwe alibe mankhwala).
5. "لَاتُكْثِرْ كَلَامَكَ فَيَقِلَّ مَقَامُكَ" (Osayankhula kwambiri, apo ayi, mbiri yako yabwino idzatsika).
6. "حِفْظُ اللِّسَانِ سَلَامَةُ الْاِنْسَانِ" (Chitetezo cha munthu chili pakuteteza lilime).
7. "يَمُوْتُ الْفَتٰى مِنْ عَثْرَةٍ بِلِسَانِهٖ وَلَيْسَ يَمُوْتُ مِنْ عَثْرَةِ الرِّجْلِ" (Mnyamata amafa chifukwa cha kutereka kwa lilime lake, osati chifukwa cha kutereka kwa phazi lake).
8. "خَيْرُ الْخِلَالِ حِفْظُ اللِّسَانِ" (Kuteteza lilime ndiye chizoloŵezi chabwino kwambiri).



www.dawateislami.net

9. "صَدْرُكَ اَوْسَعُ لِسِرِّكَ" (Chifuwa chako ndi malo otakasuka a chinsinsi chako, choncho, usaululire wina aliyense zofooka zako).

10. "مَا اَصْغَرَ اللِّسَانَ وَمَا اَكْثَرَ نَفْعَهٗ وَضَرَرَهٗ" (Lilime ndi laling'ono motani komano phindu ndi kuluza kwake ndikwakukulu!)

11. "جُرْحُ اللِّسَانِ اَنْكٰى مِنْ جُرْحِ السِّهَامِ" (Chilonda cha lilime chimapweteka kwambiri kuposa chilonda cha muvi).

12. "مَنْ حَفِظَ لِسَانَهٗ نَجَا مِنَ الشَّرِّ كُلِّهٖ" (Amene amateteza lilime lake, amapeza chipulumutso ku zoyipa zonse).

13. "لَا تَتْرُكْ لِسَانَكَ يَقْطَعُ عُنُقَكَ" (Musalole lilime lanu kuyendayenda momasuka kotero kuti mpakana kukupangitsani inu kudulidwa mutu).

14. "مَنْ كَثُرَ كَلَامُهٗ قَلَّ فِعْلُهٗ" (Aliyense amene amayankhula kwambiri, ntchito yake imachepa).

15. "مَنْ كَثُرَ كَلَامُهٗ كَثُرَ مَلَامُهٗ" (Munthu amene amayankhula kwambiri, amanyozekanso kwambiri).

16. "مَنْ عَذُبَ لِسَانُهٗ كَثُرَ اِخْوَانُهٗ" (Munthu amene ali ndi lilime lokoma, amakhala ndi abwenzi ambiri).

17. "اَللِّسَانُ مِفْتَاحُ الْخَيْرِ وَالشَّرِّ" (Lilime ndi chinsinsi cha zabwino ndi zoyipa).

18. "اَلْحَرْبُ اَوَّلُهَا كَلَامٌ" (Nkhondo imayambika chifukwa cha lilime).

19. "لِيْنُ الْكَلَامِ قَيْدُ الْقُلُوْبِ" (Mawu ofewa amaba mitima).

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب ! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد



www.dawateislami.net

## Miyambo[1] 11 ya Urdu (ndi matanthauzo a Chichewa)

1. **Zaban badalnay say gali badalna bayhtar hay** (Ndi bwino kuluza chinachake kusiyana ndi kulephera kukwaniritsa lonjezo).
2. **Zaban par sar dayna** (Kuyika moyo wako pa chiswe pofuna kukwaniritsa lumbiro).
3. **Zaban say phool jharna** (Kuyankhula mawu okoma kwambiri).
4. **Zaban qaynchi ki tarah chalna** (Kuyankhula mofulumira kwambiri).
5. **Zaban ko lagam dau** (Ganizirani musanayankhule).
6. **Zaban hilanay say kaam nikalta hay** (Ntchito imachitika poyankhula ndi kumvetsera kokha basi. Cholinga chimak waniritsidwa kudzera mu kuyanjanitsa).
7. **Pehlay tolo ba'd mayn bolo** (Ganizirani kaye; ngati mfundo yake ili yoyenera kuyankhula, ndiye kuti muyankhule, apo ayi, khalani chete).
8. **Ayk chup so sukh** (kukhala chete ndi chitonthozo chachikulu).
9. **Ayk chup so ko haraye** (Ndi munthu okhala chete yekha amene amapambana).
10. **Jo baat dau honton mayn nahin samati woh kahin bhi nahin samati** (Pambuyo pomuuza chinsinsi munthu wina, kukhala ndi chiyembekezo choti anthu ena sadzadziwa n'kopanda pake).
11. **Zaban mayn khujli hona** (kufunitsitsa kukangana).

---

[1] Liwu kapena mawu amene anthu okhala m'dzikolo amene ndi mbadwa anawayikira tanthauzo linalake ogwirizana kapena osagwirizana ndi tanthauzo lenileni.



www.dawateislami.net

## Kulapa ku zizolowezi zoyipa kunaperekedwa

O omukonda Mtumiki, mosakaikira, kuyankhula ndi ntchitonso; ngati kuli mogwirizana ndi chifuniro cha Allah Wamphamvu zonse, ndiye kuti kumapezetsa mphotho, ngati kuli koyipa, ndiye kuti pali chilango, ndipo ngati kuli kopanda pake, ndiye kuti pali chiwerengero cha tsiku lachimaliziro. Kuti muwonjezere maphuziro anu pa nkhani zimenezi komanso chidwi chofuna kuzitsatira, ndi bwino kuyenda ndima Madani Qafilah a Dawat-e-Islami kuti muphunzire ndi kuphunzitsa Sunnah. Nayi nkhani yochititsa chidwi ya Madani: Mnyamata wina wokhala ku Karachi, m'dera lotchedwa Lines, anali kukhala moyo wochimwa asanalowe mu chikhalidwe cha zichitochito za chipembedzo cha Dawat-e-Islami. Zinali ngati kuti gawo la moyo wake kunali kunama, kusamvera makolo ake, kukwiya pa nkhani zazing'ono, kuvala mphete ndi zibangili zoletsedwa komanso kulekerera chikhadabo cha chala chaching'ono kukula kwambiri. Panalibe kusintha ngakhale anthu amkamulangiza. Potsirizira pake, chifukwa cha khama la abale achisilamu, anapeza mwayi woyenda mu Madani Qafilah kwa masiku atatu ya Dawat-e-Islami kuti akaphunzire ndi kuphunzitsa Sunnah. Madani Qafilah imeneyi inabweretsa madalitso akuti anatembenuka mtima kuchoka ku chizolowezi choyipa choyankhula bodza ndipo chikhadabo chake chachitali kwambiri chimene samkachidula ngakhale kuti ndizoletsedwa kuchisunga, anachidula ali mu Madani Qafilah momwemo. Komanso, analapa kuchoka ku zizolowezi zake zoyipa ndipo anapanga chitsimikizo chabwino kuti adzapepesa kwa makolo ake ndikuwakondweretsa, adzalamulira mkwiyo wake, adzatenga nawo mbali mu zochitika zachipembedzo za Dawat-e-Islami ndipo adzayitanira ena kuti achite zomwezo.



www.dawateislami.net

O omukonda Mtumiki, mwamva mu nkhani yochititsa chidwi ya Madani iyi kuti m'bale wachisilamu wachinyamatayo anali kuvala mphete ndi zibangili zoletsedwa. Pankhani imeneyi, zikunenedwa mu buku la Maktaba-tul-Madinah, '*Rafiq al-Haramayn*', patsamba 82: "Nthawi zonse pamene abale achisilamu avala mphete, azivala mphete imodzi yokha ya siliva yolemera osakwana 4.5 Masha (magalamu okwana 4.374); asavale yoposera imodzi, ndipo mu mphete imeneyo, pakhale mwala umodzi wokha. Pasakhale miyala yoposera umodzi ndipo asavale yopanda mwala. Palibe malire a kulemera kwa mwala. Chibangili chopangidwa ndi siliva kapena chitsulo china chilichonse (ngakhale ngati chili chochokera ku Madinah Al-Munawarrah) kapena mphete yopangidwa ndi chitsulo chilichonse (monga golide, mkuwa, chitsulo, mkuwa wachikasu ndi chitsulo chosapanga dzimbiri ndi zina zotero) kupatula siliva yemwe kulemera kwake kwanenedwa, sichingathe kuvalidwa. Ndi tchimo kuvala tcheni chopangidwa ndi golide, siliva kapena chitsulo china chilichonse pakhosi.

Komanso, mu nkhani yochititsa chidwi ya Madani yomwe yatchulidwa pamwambapa, zinafotokozedwanso kuti mnyamatayo anali kulekerera chikhadabo cha chala chake chaching'ono kukula motalika kwambiri. Pankhani imeneyi, lamulo la Shariah ndi lakuti sizololedwa kulekerera chikhadabo kapena tsitsi lakukhwapa kapena tsitsi lakumaliseche kwa masiku opitilira 40. Mudzakhala wochimwa pakatha masiku 40. Ngati zitachitika kamodzi kapena kawiri, lidzakhala tchimo laling'ono; ngati zisanthidwa kukhala chizolowezi, lidzakhala tchimo lalikulu ndipo kudzakhala kuphwanya lamulo. *(Fatawah Razawiyyah, buku. 22, tsamba. 678)*



www.dawateislami.net

*Sunnatayn seekhnay teen din kay liye*

*Har Mahinay chalayn, qafilay mayn chalo*

*(Wasa`il-e-Bakhshish, tsamba. 680)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

O Mbuye wa Mustafa, tipatseni ife kuthekera kogwiritsa ntchito miyambo ya poyankhula ndipo lilime lathu lisadzayankhule chilichonse chobweretsa mkwiyo wanu!

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

## Kuyitanira ku chiwongoko (mwachidule)

Ife ndife akapolo ochimwa a Allah Wamphamvu zonse komanso akapolo a Wokondedwa Wake صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Ndithudi moyo ndi waufupi. Tikuyandikira mathero a moyo. Posachedwapa tidzayikidwa m'manda amdima. Chipulumutso chili mu kumvera lamulo la Allah Wamphamvu zonse ndikutsatira Sunnah za Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Madani Qafilah ya bungwe lachipembedzo la gulu la anthu omukonda Rasool, Dawat-e-Islami, yafika kuno kuchokera ku ............. kubwera ku ............... Masjid m'dera lanu. Tabwera kuno kudzayitanira ku chilungamo. Pakali pano mu Mzikiti mukuchitika phunziro la chipembedzo (Dars). Chonde bwerani pompano kuti mudzakhale nawo pa Dars imeneyi. Tabwera kuti tikutengeni. Chonde, tiyeni tipite. (Ngati sakufuna kupita, nenani kuti) Ngati simungathe kubwera panopa, ndiye mukapemphere Swala ya Maghrib kumeneko. Pakutha pa Swala, اِنْ شَآءَاللّٰه, Ulaliki wolimbikitsidwa ndi Sunnah udzaperekedwa. Tikukupemphani kuti mudzamvere ulaliki.



www.dawateislami.net

Allah Wamphamvu zonse atipatse inu ndi ife madalitso a dziko lino ndi a tsiku lachimaliziro.

اٰمِيْنْ بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّمَ



www.dawateislami.net

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الْمُرْسَلِيْنَ

اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ ؕ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ ؕ

# UBWINO OPEWA ZOYANKHULA ZOPANDA PAKE

O Ambuye a Mustafa, aliyense amene angawerenge kapena kumvetsera masamba 142 a buku lakuti '*Kupambana Kopewa Zoyankhula Zopanda pake*,' mutetezeni ku zochita zopanda pake, mupangeni kukhala wochita zabwino ndipo mpatseni ulemerero wokachita Hajj ndi kuona Madinah mobwerezabwereza.

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

## Kuwerenga Salat mochuluka kwatsimikiziridwa kuti ndi kopindulitsa

Sayyiduna Abu Bakr Shibli Baghdadi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti: "Ndinamuona m'nansi wanga womwalira ku maloto ndipo ndinamufunsa kuti, "مَا فَعَلَ اللّٰهُ بِكَ؟" Kodi Allah Wamphamvu zonse wapanga nawe bwanji? Iye anayankha kuti, "Ndinkumana ndi zovuta zazikulu. Ndinalephera kuyankha mafunso a Munkar ndi Nakeer. Ndinaganiza kuti mwina sindinamwalire ngati wokhulupirira, mwadzidzidzi, kudamveka mawu akuti, "Chilango ichi chikuperekedwa kwa iwe chifukwa chogwiritsa ntchito lilime mosayenera padziko lapansi." Kenako, angelo achilango anabwera kwa ine. Panthawiyi, munthu wokongola komanso wonunkhira bwino anakhala mpanda pakati pa ine ndi chilango ndipo anandikumbutsa mayankho a mafunso a



www.dawateislami.net

Munkar ndi Nakeer, ndipo ndinayankha chimodzimodzi. Chifukwa cha chisomo cha Allah Wamphamvu zonse, chilangocho chinachotsedwa kwa ine. Ndinanena modzichepetsa kwa munthu woyera mtima uja kuti, "Allah Wamphamvu zonse akuchitireni chifundo! Inuyo ndindani?" Iye anayankha kuti, "Ndinalengedwa chifukwa cha kuwerenga kwanu Salat mochuluka, ndipo ndinayikidwa kuti ndizikuthandizani nthawi zonse za mavuto." *(Al-Qaul-ul-Badi', tsamba. 260)*

*Ap ka naam-e-naami aye Sall-e-ala*

*Har jagah har musibat mayn kaam agaya*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Okondedwa abale achisilamu, masiku ano m'dera lathu, tsoka lake anthu amene amakhala chete ndi ochepa. Malilime a anthu ena amangoyendayenda tsiku lonse. Kungopatula nthawi yogona ndi pamene malilime awo amapuma. Ndipo ena amayamba kuyankhula ngakhale akugona. Woyankhula mopitirira muyeso, nthawi zambiri, amatha kunama, kupanga miseche, kunena nkhani za anthu ena, kuulula zinsinsi, kukhumudwitsa anthu ena, ndi kuluza ulemu wake chifukwa chowasokoneza anthu nthawi zonse mkatikati mwa mkambirano wawo. Nthawi zambiri, zingathenso kuchitika kuti angadzanong'oneze bondo pambuyo poyankhula. Kenako, ena amatopanso ndi kuyankhula kosalekeza kwa munthu woyankhula kwambiri. Anthu amatopa naye ndipo amayesetsa kumuchotsapo. Mwachidule, pali zoyipa zosawerengeka za kuyankhula mopitirira muyeso. N'chifukwa chake wina ananena kuti pali zabwino zisanu ndi zinayi pakukhala chete, chifukwa munthu wokhala chete amakhala wotetezeka ku mavuto ambiri. Allah



www.dawateislami.net

Wamphamvu zonse atiteteze tonse kuchokera ku kuyankhula kosafunikira komanso atiteteze kuchokera ku mavuto a lilime!

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Allah Wamphamvu zonse amadana ndi zokambirana zopanda pake

Allah Wamphamvu zonse amadana ndi zokambirana zopanda pake. Iye wanena zokhudzana ndi zokambirana zopanda pake mu Qur'an Yopatulika, gawo 18, Surah al-Mu'minon, vesi nambala 3:

وَالَّذِيْنَ هُمْ عَنِ اللَّغْوِ مُعْرِضُوْنَ ۝٣

*Ndipo amene samakonda zokamba zopanda pake.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 18, Surah Al-Mu`minon, vesi 3)*

## Ndemanga ya ndime yodalitsika

Mu ndime yodalitsikayi, makhalidwe achiwiri aanthu okhulupirira opambana atchulidwa kuti amakhala kutali ndi chilichonse chopanda pake ndi chabodza. Mu vesi lopatulikali mawu oti, 'Laghw' atchulidwa. Pankhani imeneyi, zafotozedwa mu *Tafseer Sirat-ul-Jinan*, buku 6, pa masamba 499-501 kuti 'Allamah Ahmad Saawi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti: "'Laghw' amatanthauza mawu aliwonse, zochita komanso chinthu chosakondedwa kapena cha Mubah zomwe sizimupindulira Msilamu pa nkhani za chipembedzo kapena dziko lapansi, mwachitsanzo, kuwononga nthawi pochita nthabwala, zokambirana zopanda pake, masewera ndi chisangalalo komanso zochita zopanda pake, kukhala ndi chidwi



www.dawateislami.net

chongokwaniritsa zilakolako ndi zochita zina zonse zomwe Allah Wamphamvu zonse analetsa. Chidule ndi chakuti Msilamu ayenera kukhala wotanganidwa ndi kuchita zabwino kuti tsogolo lake likhale labwino kapena ayenera kukhala wotanganidwa ndi kuyesetsa kupeza chuma (cha Halal) malinga ndi zosowa zake kuti azikhala moyo wake wabwino.” *(Tefseer-e-Saawi, buku. 3-4, tsamba. 1356-1357)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Chilimbikitso kuti tipewe zinthu zopanda pake

Chilimbikitso pofuna kupewa zinthu zopanda pake komanso zosathandiza chaperekedwanso m'Mahadith.Choncho, Sayyiduna Abu Hurairah رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anafotokoza kuti Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: “Chimodzi mwa zinthu zomwe zimasonyeza kukwanira kwa Chisilamu cha munthu ndi kusiya zinthu zopanda pake.” *(Mauta Imam Malik, buku. 2, tsamba. 403, Hadith: 1718)*

Zikutanthauza kuti, iye sayenera kupanga zinthu zosathandiza. Asagwiritse ntchito lilime lake, mtima wake ndi ziwalo zina za thupi lake pa zinthu zopanda pake. *(Bahar-e-Shari’at, buku. 3, tsamba. 520)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Chipulumutso ndi chiyani ?

Sayyiduna Uqbah Ibn Aamir رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anati: Ndinapita pa maso pa Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo ndinafunsa modzichepetsa kuti,



www.dawateislami.net

"Kodi chipulumutso ndi chiyani? Iye anayankha kuti, 'Lamulirani (tetezani) lilime lanu ndipo nyumba yanu ikhale yokwanira kwa inu (kutanthauza, musamapite kwina kulikonse mosafunikira) ndipo gwetsani misozi chifukwa cha zolakwa zanu.' *(Tirmizi, buku. 4, tsamba. 182, Hadith: 2414)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب !          صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kufunika koteteza lilime komanso phindu lake ndi zoyipa zake

Kumbukirani kuti kuteteza lilime, kulileтsa komanso kulipewetsa ku zokamba zopanda pake n'kofunika kwambiri, chifukwa zambiri mwa zinthu zachipongwe komanso chisokonezo ndi zowononga zimayambitsidwa ndi lilime lomweli. Ndipo munthu amene amasiya lilime lake kuti liyendeyende mopanda kulileтsa, Satana amamupangitsa kugwera m'chiwonongeko. Ubwino winanso woteteza lilime ndiwakuti ntchito zabwino zimatetezeka, chifukwa munthu amene sateteza lilime, m'malo mwake amangoyankhula nthawi zonse, samatha kupewa kukamba miseche ya anthu. Chimodzimodzinso, pamakhala chiopsezo chachikulu choyankhula mawu osakhulupirira, ndipo ntchito zonsezi ndi zomwe zimawononga zabwino za munthu.

## Thireyi ya tende (Nkhani)

Munthu wina ananena kwa Sayyiduna Imam Hasan Basri رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ kuti: "Wakuti-wakuti amakunenani miseche." Atamva zimenezi, iye anadzazitsa thireyi ndi tende n'kutumiza kwa munthu amene anamunena miseche uja; kuwonjezera apo, anatumiza uthenga uwu: "Ndamva kuti

mwandipatsa zabwino zanu. Choncho, ndinaona kuti n'koyenera kubwezera. (Ndicho chifukwa chake, nayi thireyi ya tende)" *(Minhaj-ul-'Aabideen, tsamba. 65)*

## Kuti anthu angakugululeni mano anu

Ndipo phindu lachiwiri ndi lakuti, poteteza lilime, munthu amakhala wotetezeka ku masoka a dziko lapansi. Choncho, Sayyiduna Sufyan Sauri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Musalole kuti lilime lanu litulutse mawu omwe angapangitse kuti anthu akamva mawu amenewa akuchotseni (akugululeni) mano anu." Ndipo munthu wina woyera mtima رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti: "Musalole kuti lilime lanu likhale longoyankhula zilizonse (losatetezeka) kuti lisakupatseni mavuto aliwonse." *(Minhaj-ul-'Aabideen, tsamba. 66)*

## Chilango chapadera pa funso limodzi lopanda pake (Nkhani)

Komanso, chimodzi mwa zoyipa za kusateteza lilime n'chakuti munthuyo amangoyamba kukamba nkhani zoletsedwa, Haram, zopanda pake komanso zosathandiza, amachita machimo ndipo amawononga chuma chamtengo wapatali kwambiri pa moyo wake, chomwe ndi nthawi. Zafotokozedwa zokhudza Sayyiduna Hassan Ibn Sinan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه kuti anadutsa pafupi ndi chipinda chimodzi chomwe chinali padenga la nyumba (chipinda chapamwamba), choncho, anafunsa mwiniwake: "Ndi nthawi yayitali bwanji kuchokera pamene munamanga chipinda ichi?" Atatha kufunsa funso limeneli, anachita manyazi kwambiri ndipo anayankhula motere akuyankhula ndi Nafs yake: "E iwe Nafs yodzikweza, ukutaya nthawi yamtengo wapatali kwambiri pamafunso opanda pake komanso osathandiza." Kenako, ngati chikhululikiro cha funso lopanda



www.dawateislami.net

pakelo, anasala kudya kwa chaka chimodzi. *(Minhaj-ul-'Aabideen, tsamba. 65)*

## Palibe angakwanitse kupirira pa chilango cha ku Gahena

Ndipo choyipa chachiwiri ndi chakuti, chifukwa cha mkambirano osaloledwa ndi wa Haraam, munthu akhoza kudzapatsidwa chilango chowawa cha ku Gahena pa Tsiku la Chiweruzo, chimene palibe amene angathe kuchipirira. Choncho, chitetezo chagona poti munthu ayenera kutetetza lilime lake ndi kuligwiritsa ntchito pazinthu zimene zingam'thandize pa dziko lapansi ndi pa Tsiku la Chiweruzo. Allah Wamphamvu zonse awapatse Asilamu onse kuthekera koteteza malilime awo ndi kuwalamulira! Aameen. *(Sirat-ul-Jinan, buku. 6, tsamba. 499 -501)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Ntchito zolemera

Sayyiduna Abu Zar Ghifari رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anafotokoza kuti Mtumiki Wokondedwa wa Allah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananena kwa ine kuti, "Kodi ndikufotokozere ntchito imene ili yosavuta pa thupi koma yolemera pa sikelo?" Ine ndinayankha modzichepetsa kuti, 'Inde!' Iye anati, "Ndi kukhala chete, makhalidwe abwino, ndi kusiya zokambirana zopanda phindu." *(Al-Samt Ibn-e-Abi Al-Dunya ma' mausu'ah, buku. 7, tsamba. 87, Hadith 112)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kukongola kwa munthu chiyani?

Mtumiki wathu Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananena kwa amalume ake wolemekezeka, Sayyiduna Abbas رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ kuti, "Kukongola kwanu



www.dawateislami.net

kumandidabwitsa.” Sayyiduna Abbas رَضِیَ اللّٰہُ عَنْهُ anafunsa modzichepetsa kuti, ‘Ya Rasoolallah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, kodi kukongola kwa munthu chiyani?’ Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayankha kuti, “Lilime lake.”

*(Abab- Al-Dunya wa Al-deen, tsamba. 241)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Malangizo a Mtumiki Woyera ﷺ

Mtsogoleri wa achinyamata a ku Paradaiso, sahaba, komanso mwana wa sahaba, Sayyiduna Imam Husain رَضِیَ اللّٰہُ عَنْهُ ananena kuti kuchokera mu uphungu umene ndinamva agogo anga, Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم akuwauza masahaba wolemekezeka رَضِیَ اللهُ عَنْهُم, umodzi ndi otsatirawu: “Nkhani yabwino kwa munthu amene amapewa kuyankhula zopanda pake.” *(Hilyat Al-Awliya`, buku. 3, tsamba. 236, Hadith: 3817)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Dua ya Mustafa

Sayyiduna Anas Ibn Malik رَضِیَ اللّٰہُ عَنْهُ anafotokoza kuti Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananena mfundo iyi kokwana katatu: “Allah Wamphamvu zonse amuchitire chisoni munthu amene amapeza phindu (malipiro) akayankhula, ndipo amakhala wotetezeka akakhala chete.” *(Shu’ab-ul-Iman, buku. 4, tsamba. 241, Hadith 4938)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Chizindikiro chakuti chifundo cha Allah Wamphamvu zonse chachoka

Sayyiduna Imam Hasan Basri رَحۡمَةُ اللّٰہِ عَلَيۡه anati: "Munthu kuchita zinthu zopanda pake ndi chizindikiro chakuti Allah Wamphamvu zonse wachotsa kuyang'ana Kwake kwachifundo kuchokera kwa iyeyo." *(Al-Tamheed Ibn-e-'Abdul Bar, buku. 4, tsamba.179)*

## Munthu amene amangoyankhula zopanda pake amakhala ndi machimo ambiri

Sahaba, komanso mwana wa sahaba, Sayyiduna Abdullah Ibn Abi Awfa رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُمَا anafotokoza kuti Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Pa Tsiku la Chiweruzo, munthu amene adzakhale ndi machimo ambiri pakati pa anthu onse adzakhala amene ankayankhula zopanda pake kwambiri." *(Jami' Sagheer, tsamba. 86, Hadith 1386)*

**Kufotokozera Hadith:** Ndi chifukwa chakuti munthu woyankhula kwambiri, mu kuyankhula kumeneko, mumakhala zinthu zopanda pake komanso zotsutsana ndi Shariah. Choncho, chifukwa cha zinthu zotsutsana ndi Shariah, machimo ake amawonjezereka ndipo iye samazindikira n'komwe. *(Al-Tayseer Sharah Al- Jami' Sagheer, buku.1 tsamba. 200; Fatawah Razawiyya buku. 28 tsamba. 645)*

## Kutchulidwa kolemekezeka kwa Sayyiduna Abdullah Ibn Abi Awfa رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُمَا

Tiyeni timvetsere mbiri yodalitsika ya sahaba wa Mtumiki amene ananena nkhaniyi, Sayyiduna Abdullah Ibn Abi Awfa رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُمَا: Dzina lake ndi

Abdullah Ibn Abi Awfa ndipo Kunyah ndi Abu Mu'awiyah.

## Dua kwa munthu wopereka Zakah

Sahaba, komanso mwana wa sahaba, Sayyiduna Abdullah Ibn Abi Awfa رَضِیَ اللہُ عَنْہُمَا anafotokoza kuti: "Bambo anga (Abu Awfa رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ) anapita pa maso pa Mtumiki Woyera صَلَّی اللہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم atanyamula Zakat, choncho iye صَلَّی اللہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anamudalitsa iye ndi dua iyi "اَللّٰهُمَّ صَلِّ عَلٰى اٰلِ اَبِیْ اَوْفٰى" kumasulira kuti *O Allah, tumizani madalitso anu ku banja la Abu Awfa." (Bukhari, buku. 1, tsamba. 504, Hadith 1498)*

Sayyiduna Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba pofotokozera Hadith yopatulikayi kuti: "Sayyiduna Abdullah رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ akupereka chiyamiko monyadira kwa Ambuye kuti: ife ndi abambo athu olemekezeka tinadalitsidwa ndi mapemphero a Mtumiki Woyera صَلَّی اللہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم. Anthu ena ananena kuti mawu oti, 'Aal' apa ndi owonjezera, koma zoonadi ndizakuti 'Aal' ali ndi mu tanthauzo lake lenileni. Mtumiki Woyera صَلَّی اللہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم sanawapempherere anthu amenewa okha komanso anawapempherera ana awo ndi achibale awo onse. *(Mir`aat, buku. 3, tsamba. 11)*

## Kukumana kwa Imam Abu Hanifah ndi sahaba wa Mtumiki

Zafotokozedwa mu *Mir'aat* kuti: "Sayyiduna Abdullah Ibn Abi Awfa رَضِیَ اللہُ عَنْہُمَا ndi sahaba womaliza kumwalira ku Kufa mu chaka cha 87 Hijri. Iye ali m'gulu la masahaba amene Sayyiduna Imam Abu Hanifah رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anakumana nawo, chifukwa pa nthawi ya imfa yake, Imam Al-A'zam anali ndi zaka zisanu ndi ziwiri (ndipo malinga ndi anthu ena, iye anali ndi

zaka 17).” *(Nuzhat-ul-Qaari, buku. 1, tsamba. 70, zatengedwa kuchokera mu ; Mir`aat, buku. 5, tsamba. 382)*

Allah Wamphamvu amuchitire chisoni ndipo atikhululukire popanda chiwerengero chifukwa cha ubwino wake!

اٰمِیْن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِیّٖن صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kuyankhula kopanda pake ndi chiyani?

Okondedwa abale achisilamu, Sayyiduna Imam Muhammad Ibn Muhammad Ibn Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena mu *Ihya al-Uloom* kuti: “Ngati cholinga chake (cha woyankhula) chakwaniritsidwa ndi mawu amodzi, ndipo iye wagwiritsa ntchito mawu awiri, ndiye kuti mawu achiwiriwo ndi opanda ntchito, kutanthauza kuti ndi ochuluka kuposa momwe akufunikira.” *(Ihya’-ul-‘Uloom, buku. 3, tsamba. 141)*

Ngati mawu amodzi sakukwanira, ndiye kuti panthawi imeneyi, mawu awiri kapena ochulukirapo amene amayankhulidwa malinga ndi kufunukira, samakhala opanda pake. Zinthu zomwe zili ndi vuto, chiwerengero, ndi chilango, kuzipewa ndikofunikira pa nzeru za munthu aliyense, koma zinthu zomwe sizibweretsa phindu kapena vuto, ndizinthu zoyipa, chifukwa nthawi yomwe anali akuyankhula zinthu zimenezi, bwenzi akuwerenga ma Zikr komanso kumufunira zabwino Mtumiki mu nthawi yotalika ngati yomweyo; akadatha kuwerenga Qur’an. Ngati kusemphana ndi phindu limeneli sikuluza, ndiyeno chimenechi n’chiyani? Kenako, pamene zokambirana zopanda pake zayamba, (nthawi

zambiri) zimapita patsogolo mpaka kufika pozudzula anthu ena komanso kuwanena miseche. Ndi chifukwa chake chitetezo chogona mu kukhala chete kapena kuchita Mazikr a Allah Wamphamvu zonse, ndipo ayenera kuyankhula zinthu za dziko lapansi zokhudzana ndi zinthu zololedwa, zochepa kwambiri malinga ndi kufunikira kwake. Kuchuluka kwa zokambirana ngakhale zololedwa za dziko kumawumitsa mtima.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Ngati mu kukhala chete mulibemo kulingalira za dziko likubwera, ndiye kuti kumeneko ndi kunyalanyaza

Sayyiduna Eisa عَلَيْهِ السَّلَام anati: "Kukambirana kumene kulibe kumukumbukira Allah Wamphamvu zonse ndi Laghw (kopanda ntchito), ndipo kukhala chete kumene kulibe kuganizira za tsiku lomaliza ndi kunyalanyaza, ndipo kuyang'ana kumene kulibe kutengerapo phunziro ndi kopanda ntchito komanso kopanda pake. Ndiwodalitsika munthu amene mkambirano wake uli kumukumbukira Allah Wamphamvu zonse, kukhala kwake chete kuli ndi kuganizira, ndipo kuyang'ana kwake kuli ndi kutengera phunziro." *(Tanbeeh Al-Ghafileen, tsamba. 115)*

## Kunyalanyaza ndi chiyani?

O omukonda Rasool, kuyankhula kumeneku kwa Sayyiduna Eisa عَلَيْهِ السَّلَام kukuphatikizanso zotsatirazi: "Kukhala chete kumene kulibe kuganizira za tsiku lomaliza ndi kunyalanyaza." Tiyeni tiphunzire kuti kunyalanyaza ndi chiyani. Zafotokozedwa mu 'Al-Ta'rifat' kuti: " اَلْغَفْلَة: مُتَابَعَةُ النَّفْسِ عَلٰى مَا



www.dawateislami.net

تَشْتَهِیْهِ” kunyalanyaza kumatanthauza kuyipanga Nafs kukhala yotanganidwa ndi zilakolako. *(Al-Ta'rifat Lil-Jurjani, tsamba. 116)*

Podzudzula kunyalanyaza, Allah Wamphamvu zonse wayankhula mu Qur'an Yopatulika, gawo 9, Surah Al-A'raaf, vesi nambala 205:

وَ اذْكُرْ رَّبَّكَ فِیْ نَفْسِكَ تَضَرُّعًا وَّ خِیْفَةً

وَّ دُوْنَ الْجَهْرِ مِنَ الْقَوْلِ بِالْغُدُوِّ وَ الْاٰصَالِ وَ لَا تَكُنْ مِّنَ الْغٰفِلِیْنَ (۲۰۵)

*Ndipo kumbukirani Mbuye wanu m'mitima mwanu; modzichepetsa ndi moopa, ndipo motsitsa mawu ndi malilime anu (moti inu nokha mungathe kudzimva); m'mawa ndi madzulo, ndipo musakhale m'gulu la anthu onyalanyaza.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 9, Surah Al-A'raaf, vesi 205)*

## Ndikuopa kupezeka kwa kunyalanyaza pa inu

Izi zafotokozedwanso mu Hadith yopatulika ya Sahih Bukhari: "Ndikulumbira mwa Allah Wamphamvu zonse, sindikuopera umphawi pa inu, koma ndikuopa kuti dziko lapansi lidzatambasulidwa kwa inu monga momwe linatambasulidwa kwa mitundu akale. Choncho, chifukwa cha dziko lapansi, muzidzapikisananso wina ndi mzake monga momwe anthu akale amkachitira, ndipo izi zidzakulowetsani mu kunyalanyaza monga momwe zinawalowetsera anthu akale mu kunyalanyaza." *(Bukhari, buku. 4, tsamba. 225–226, Hadith: 6425)*



www.dawateislami.net

## M’malo mwake, ndikulira chifukwa cha mapemphero osiyidwa

Zanenedwa mu Mukashafat al-Quloob kuti Sayyiduna Shaykh Abu Ali Daqqaq رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: “Munthu wina woyera mtima wotchuka kwambiri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه amkadwala kwambiri. Ndinapita kukafunsa za thanzi lake. Gulu la odzipereka linamuzungulira. Munthu woyera mtima uja رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه amkalira. Ndinanena modekha kuti, ‘O Shaykh, mukulira chifukwa mukuchoka padziko lapansi?’ Iye anayankha kuti, “Ayi, m’malo mwake, ndikulira chifukwa chosiya mapemphero.” Ndinafunsa kuti, ‘Wolemekezeka, mumasiya bwanji mapemphero anu?’ Iye anati, “Nthawi zonse ndikagwetsa khope pansi, ndinkagwetsa monyalanyaza, ndipo ndikakweza mutu wanga kuchokera pa sajidah, ndinkakweza monyalanyaza, ndipo tsopano, ndikukakumana ndi imfa ndili onyalanyaza.” Kenako, anapuma modandaula kwambiri ndipo anawerenga ndakatulo zinayi zachiarabu zomwe tanthauzo lake ndi lotsatirali:

1. Ndinaganizira za kuuka kwanga kwa akufa, Tsiku la Chiweruzo ndi tsaya langa litagona m'manda.

2. Ngakhale pambuyo pa ulemu ndi kukwezedwaa kotereko (kumene ndinakolola), ndidzakhala ndekha ndipo ndidzaperekedwa chifukwa cha zolakwa zanga ndipo nthaka yokha ndiyo idzakhale pilo yanga.

3. Ndinaganizira za kutalika kwa nthawi yoti ndidzayankhe komanso kuchititsidwa manyazi pa nthawi yopatsidwa buku la ntchito.



www.dawateislami.net

4. Koma O Mlengi ndi Mthandizi wanga, ndikuyembekeza chifundo kuchokera kwa Inu. Inu nokha ndinu wokhululuka pa zolakwa zanga. *(Mukashafah Al-Quloob, tsamba. 22)*

## Adzalowa ku Gahena akulira

Okondedwa abale achisilamu, nkhani yophunzitsa imeneyi! Tangoyang'anani akapolo oyera a Allah Wamphamvu zonse amene anakhala nthawi yawo yonse pomukumbukira Allah Wamphamvu zonse, komabe, kudzichepetsa kwawo ndikwakuti samakutengera kupembedza kwawo komanso zochita zawo zauzimu, ndipo amalira poopa kudziyimira payekha kwa Allah Wamphamvu zonse ndi dongosolo Lake lachinsinsi. Kodi ndi zomvetsa chisoni bwanji m'mene alili anthu omwe samadziwa chinthu choyambilira chokhudza ntchito yabwino ndipo mulibe chizindikiro chilichonse cha kuwona mtima mwa iwo, komabe, ngakhale zili choncho iwo samatopa ndi kunena zokhudza kupembedza kwawo! Ngakhale ali otetezedwa ku machimo, akapolo oyera a Allah Wamphamvu zonse amanjenjemera ndi kulira mosalekeza chifukwa choopa Allah, koma mkhalidwe wa iwo amene amakhala onyalanyaza ndiwakuti amapitirizabe kusamvera kwawo mosazengereza, amalengeza poyera machimo awo ndipo, samachita manyazi ngakhale pang'ono poseka za zimenezi. Mvetserani mosamala. Zafotokozedwa mu Mukashafat al-Quloob: "Sayyiduna Ibn Abbas رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُمَا ananena kuti, 'Munthu amene amapanga tchimo akuseka, adzalowa ku Gahena akulira.'" *(Mukashafah Al-Quloob, tsamba. 275)*

*Gunahon say mujh ko bacha Ya Ilahi!*

*Buri aadatayn bhi chhura Ya Ilahi!*

*(Wasa`il-e-Bakhshish, tsamba. 100)*



www.dawateislami.net

## Munthu woyera anapereka nkhani yabwino ku maloto

Odzipereka a Rasool, kuti mudzuke kuchokera ku tulo la kunyalanyaza, muchotse chizolowezi chochita machimo ndikuwonjezera chidwi chotsatira Sunnah, yendani ndi ma Madani Qafilah a Dawat-e-Islami kuti muphunzire ndi kuphunzitsa Sunnah. Kuti mulimbikitsidwe, chozizwitsa cha Madani chowonjezera chikhulupiriro chabweretsedwa: Choncho, m'bale wina wachisilamu wochokera ku Vihari, Punjab amkachita machimo osiyanasiyana asanalowe mu zochitika za chipembedzo za Dawat-e-Islami. Ngakhale anali wathanzi, anali wofooka kwambiri pa nkhani yopembedza. Pamene ankayandikira unyamata wake, ankangochulukirachulukira kutalikira kuchokera ku ntchito zabwino. Anayamba kukhala moyo wa machimo. Nthawi yake imkawonongeka ndi nyimbo, mafilimu, sewero, kunama, miseche ndi machimo ena osiyanasiyana, ndipo osati zimenezo zokha, analinso ndi sitolo yomwe inkathandizira ntchito yoyika nyimbo ndi mafilimu, kudzera m'menemo, mwachionekere, iye mwiniyo amkachita machimo, komanso, amkayika mafilimu, masewero ndi nyimbo m'mafoni a anthu ena ndikugawana nawo machimo awo, ndipo amkalipiritsa ndalama. Moyo wake unali mu mdima wa machimo, moti anayamba kudziona kuti ndi munthu woyipa kwambiri padziko lapansi. Komabe, kuyambira ali mwana, amkakonda Dawat-e-Islami, ndi chifukwa chake anakwanitsa kuyankhulana ndi abale achisilamu ndipo anakhala woyenda m'Madani Qafilah kwa masiku atatu. Anaphunzira zambiri pa nthawi ya Madani Qafilah, zomwe zinawonjezera chikondi chake pa Dawat-e-Islami. Tsiku lina pamene anali kuda nkhawa chifukwa cha zinthu za m'nyumba mwake ndipo pamene anagona ali wopwetekedwa mtima, analota kuti munthu woyera mtima akumuuza kuti: Ubwere ku Faizan-e-Madinah (Karachi) ndi mng'ono wako. اِنْ شَآءَاللّٰہ, zonse zidzakhala bwino. Anadzuka atangomva zimenezi.



www.dawateislami.net

Kenako, anafotokozera banja lake malotowo ndipo anapempha chilolezo chopita ku Faizan-e-Madinah, Karachi ndi mng'ono wake, ndipo achibale ake anavomera. Atafika ku Faizan-e-Madinah, Karachi, onse awiri anapanga I'tikaf ya mwezi wonse wa Ramadan. Mwa chisomo cha Allah Wamphamvu zonse komanso chifukwa cha ubwino wa I'tikaf, analapa machimo ake onse ndipo kuwonjezera pamenepo anayambanso kuvala Imamah, analowanso m'gulu la otsatira a Sayyiduna Ghaus Al-A'zam رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه.

O okonda Auliya, kulapa uli wamng'ono komanso kuchita ntchito zomvera Allah Wamphamvu zonse ndi madalitso akuluakulu. Mawu otsatirawa a Mtumiki Wokondedwa wa Allah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ali ndi nkhani yabwino kwambiri: "Munthu amene amalapa ali wamng'ono amakondedwa ndi Allah Wamphamvu zonse." *(Kitab Al-Twbah ma' mausu'ah Imam Ibn-e-Abi Dunya buku 3, tsamba. 422, Hadith 184)*

Munthu amene amakhala chinyamata chake akupembedza adzapeza mthunzi wa Arsh pa Tsiku la Chiweruzo. *(Muslim tsamba. 399 Hadith: 2380)*

Komanso, Masufi olemekezeka ananena kuti kupembedza kwa unyamata kumakhala kopambana kuposa kupembedza kwa ukalamba, chifukwa nthawi yeniyeni yopembedza ndi nthawi ya unyamata.

*Kar jawani mayn ibadat kahili achi nahiṉ*

*Jab burhapa agaya kuch baat ban parti nahi*

*Hay burhapa bhi ghanimat jab jawani ho chuki*

*Yeh burhapa bhi na hoga maut jis dam aa gayi*

*(Mir`aat Al-Minajih, buku. 3, tsamba. 167)*



www.dawateislami.net

Allah Wamphamvu zonse atipange kukhala omumvera Iye mpaka mpweya wathu womaliza ndipo atipatse kuwona mtima ndi chisangalalo popembedza!

اٰمِيْن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Mitundu iwiri ya mayankhulidwe komanso kukhala chete

Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "اِمْلَاءُ الْخَيْرِ خَيْرٌ مِّنَ السُّكُوْتِ وَالسُّكُوْتُ خَيْرٌ مِّنْ اِمْلَاءِ الشَّرِّ" kuyankhula zabwino ndi kwabwino kuposa kukhala chete, ndipo kukhala chete ndi kwabwino kuposa kuyankhula zoyipa. *(Shu'ab-ul-Iman, buku. 4, tsamba. 256, Hadith: 4993)*

Sayyiduna Ali Ibn Usman Hujweri Hanafi, wodziwika ndi dzina loti Daata Ganj Bakhsh رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, ananena mu *Kashf al-Mahjoob* kuti: "Pali mitundu iwiri ya kuyankhula: umodzi ndi kuyankhula zabwino ndipo wachiwiri ndi kuyankhula molakwika komanso kopanda pake. Chimodzimodzinso, palinso mitundu iwiri ya kukhala chete:

1. Kukhala chete mwadala (kutanthauza kukhala chete pofuna kuganizira za tsiku lomaliza kapena kuganizira za malamulo a Shari'ah)

2. Kukhala chete monyalanyaza (kapena, Allah aletse, kudzazidwa ndi malingaliro oyipa kapena maganizo opanda pake a dziko lapansi).

Aliyense ayenera kuganizira bwino akakhala chete kuti ngati kuyankhula kwake kuli kwabwino, tsopano, kuyankhula kwake kuli bwino kuposa



www.dawateislami.net

kukhala chete kwake, ndipo ngati kuyankhula kwake kuli kolakwika kapena kopanda pake, ndiye pa nthawi yotere, kukhala chete kwake kuli bwino kuposa kuyankhula kwake. Pofuna kulangiza zokhudza kuyankhula kukhala kolondola kapena kolakwika, Sayyiduna Daata Ganj Bakhsh Ali Hujweri رَحْمَةُاللّٰہِعَلَیْہ anafotokoza nkhani ndipo anati: "Tsiku lina akudutsa m'dera lina la Baghdad, Sayyiduna Abu Bakr Shibli Baghdadi رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَیْہ anamumva munthu akunena kuti, "اَلسُّکُوْتُ خَیْرٌ مِّنَ الْکَلَامِ", kutanthauza kuti kukhala chete ndikopambana kuposa kuyankhula. Iye رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَیْہ anaena kwa iye, '(Kukhala chete sikwabwino nthawi zonse, choncho,) kukhala chete kwanu ndi kwabwino kuposa kuyankhula kwanu, ndipo kuyankhula kwanga ndi kwabwino kuposa kukhala chete kwanga.'" *(Al-Kashf Al-Mahjob, tsamba. 402)*

صَلُّوا عَلَی الْحَبِیْب! صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Satana amamugonjetsa munthu amene samateteza lilime lake

Satana amalamulira anthu amene amayankhula zopanda pake, chifukwa munthu akakhala oyankhula kwambiri, kuthekera kolakwitsa kumachuluka, ndipo n'zotheka kuti Satana angamupambane pomupangitsa iye kuti achite tchimo. Komabe, munthu amene ali ndi chizolowezi chokhala chete, amagonjetsa Satana. Sayyiduna Abu Saeed Khudri رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anafotokoza kuti ananena modzichepetsa kwa Mtumiki Woyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم kuti, "Ya Rasoolallah صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم, Ndipatseni malangizo." Mtumiki Woyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'Gwiritsitsani pa kumuopa Allah Wamphamvu zonse, chifukwa ndiwo muzu wa zabwino zonse, ndipo gwiritsitsani pa kumenya nkhondo munjira ya Allah, chifukwa kumeneku ndiko kudzipatula kwa otsatira Chisilamu, ndipo



www.dawateislami.net

nthawi zonse pangani ma Zikr a Allah ndi kuwerenga Qur'an Yopatulika, chifukwa izi zidzakhala kuwala kwanu padziko lapansi komanso chifukwa choti inu muzitchulidwa kumwamba. Ndipo kupatula mawu abwino, tetezani lilime lanu, chifukwa cha ubwino wa zimenezi, mudzagonjetsa Satana.' *(Mu'jam Sagheer, buku. 2 tsamba. 66)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Chida chachikulu cha Satana

Sayyiduna Imam Muhammad Ibn Muhammad Ibn Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena mu *Ihya al-Uloom* kuti: "Lilime ndiye chida chachikulu cha Satana posocheretsa munthu." *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 133)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Siddiq-e-Akbar amkayika mwala mkamwa mwake

Khalifah woyamba wa Asilamu, wodzipereka wosayerekezeka, Sayyiduna Siddiq-e-Akbar رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ ankasamala kwambiri pankhani ya lilime ngakhale kuti anali wotsimikizika kuti akalowa ku Paradiso. Zafotokozedwa mu *Ihya al-Uloom*: "Sayyiduna Abu Bakr Siddiq رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ ankayika mwala mkamwa mwake modala kuti pasakhale mpata woyankhula." *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3 tsamba. 137)*

## Kukhala chete kwa zaka 40 (Nkhani)

Okondedwa abale achisilamu, ngati mukufunitsitsa kukhala ndi chizolowezi chokhala chete, ndiye kuti muyenera kuchita izi mozama



www.dawateislami.net

ndipo muyenera kuchita masewera olimbitsa thupi okhala chete; apo ayi, nkovuta kukhala ndi chizolowezi chokhala chete ndi khama lochepa kwambiri. Dzichenjezeni nokha za chiwonongeko cha kugwiritsa ntchito lilime mosafunikira ndikuyesetsa momwe mungathere kuti mukhale ndi chizolowezi chokhala chete; إِنْ شَآءَاللّٰه kupambana kudzakhala m'mapazi anu. Tiyeni timvetsere nkhani ya kukhazikika kwa munthu wolimbikira. Sayyiduna Artah Ibn Munzir رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه anati: "Munthu wina anakhala chete kwa zaka 40 motere: amkadziyika mwala m'kamwa mwake, kotero kuti kungopatula pa (Salah kapena powerenga zowerenga kapena) kudya kapena kumwa kapena kugona, sankachotsa mwalawo m'kamwa." *(Al-Samt ma' Mausu'ah Ibn-e-Abi Al-Dunya, buku. 7, tsamba. 256 mawu nambala. 438)*

## Tabi'i woyera amene analemba mikambirano komanso ndi kuyiwunikira

Tabi'i woyera mtima, Sayyiduna Rabi' Ibn Khuthaim رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه sanayankhule ngakhale mawu amodzi apadziko lapansi kwa zaka 20. Kukacha, amatenga cholembera, inki ndi pepala, ndipo amalemba chilichonse chimene ankayankhula tsiku lonse n'kudziwerengera yekha madzulo, kutanthauza kuti molingana ndi zimene analemba, amkawunikira zokambirana zake. *(Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 339; Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 137)*

## Momwe tingawunikire mkambirano

Njira yowunikira mkambirano wanu ndi yakuti munthu ayenera kuganizira mawu aliwonse amene wanena n'kumadzifunsa mafunso, mwachitsanzo, azidzifunsa mumtima posasuntha lilime lake kuti: Chifukwa chiyani wanena mawu akuti-akuti? chofunika chinali chiyani



www.dawateislami.net

kuti ayankhule pamalopo? Kukambirana kwakuti-kwakuti kukanatheka ndi mawu ochepa chabe, koma chifukwa chiyani anawonjezera mawu ena? Pamene amayankhula ndi munthu wakuti-wakuti, chifukwa chiyani ananena kuti, 'Chani? Pepani? Mwati chani?' ndi zina zotero n'kumuvutitsa munthuyo kuti abwerezenso mawu ake? Mawu amene munanena kwa munthu wakuti-wakuti anali opangitsa mtima kusweka; mwangomupweteka mtima mosayenera. Chabwino, tsopano lapani komanso pemphani chikhululuko kwa m'bale wachisilamu ameneyo. Chifukwa chiyani munapita kumsonkhano wakuti-wakuti pamene mumadziwa kuti kumakhala nkhani zopanda pake? Ndipo chifukwa chiyani munagwirizana ndi mawu akuti-akuti? Munamvanso miseche kumeneko. Ndipotu, munamvetseranso misecheyo ndi chidwi. Chabwino, lapani zenieni ndipo tsimikizani kuti mudzikhala kutali ndi misonkhanoyi. Mwanjira imeneyi, munthu wanzeru akhoza kuwunukira zokambirana kwake, kapena kuti, pa zochita zake zonse za tsiku ndi tsiku. Motero, machimo, kusasamala, ndi zolakwika zina za munthu zikhoza kuwonekera ndipo chifukwa chomwe chingabweretse kusintha chikhoza kupezeka. M'malo a zochitika za chipembedzo a Dawat-e-Islami, kuwunikira kumeneku kumatchedwa, 'Jaiza', ndipo m'malo a zochitika za chipembedzo a Dawat-e-Islami, chilimbikitso chimaperekedwa kuti munthu aziganizira zochita zake tsiku lililonse kwa mphindi zosachepera 12 ndipo pa nthawi imeneyi azilemba kabuku ka 'Nchito Zabwino'.

*Zikr-o-Durood har ghari wird-e-zabaṉ rahay*

*Mayri fuzool goyi ki 'aadat nikal do*

*(Wasa`il-e-Bakhshish, tsamba. 305)*

## Kuwunikira ntchito

Onse omukonda Rasool ayenera kuwunika zochita zawo za tsiku lonse



www.dawateislami.net

tsiku lililonse kwa mphindi zosachepera 12 ndikulemba zomwe zili m'kabuku ka Maktaba-tul-Madinah ya Dawat-e-Islami kotchedwa, 'Ntchito Zabwino', ndipo pa tsiku loyamba la mwezi uliwonse, ayenera kupereka kwa nthumwi ya Nthambi yoongolera (yokonza) ntchito ya Dawat-e-Islami ya m'dera mwawo. اِنْ شَآءَاللّٰه, chuma chochuluka cha makhalidwe abwino ndi kulungama chidzapezedwa ndipo adzakhala ndi chikondi chachikulu kwa Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Dandaulo kwa Allah Wamphamvu zonse lokhudzana ndi kuthwa kwa lilime

Khalifah wachiwiri wa Asilamu, Sayyiduna Umar Farooq A'zam رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anaona kuti khalifah woyamba wa Asilamu, Sayyiduna Abu Bakr Siddiq رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ amkakoka lilime lake lodalitsidwa ndi dzanja lake. Iye anafunsa, 'E, wachiri kwa Mtumiki, mukuchita chiyani?' Iye رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anayankha, "Chimenechi chandifikitsa kumalo a chiwonongeko, ndipo Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: Palibe gawo la thupi lomwe silidandaula kwa Allah Wamphamvu zonse za kuthwa kwa lilime."

*(Ihya al-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 335; Ihya al-'Uloom, buku. 3, tsamba. 135)*

## Musatilole ife kutuluka pa lilime

Mwaona? Khalifah woyamba wa Asilamu, Sayyiduna Abu Bakr Siddiq رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ amene anali sahaba wokhulukidwa, anali kuopa kwambiri mavuto a lilime. Ndithudi, pali zambiri zoti tiphunzire mmenemo chifukwa timayankhula chilichonse chimene chimabwera m'maganizo mwathu. Sayyiduna Imam Muhammad Ibn Muhammad Ibn

Muhammad Ghazali رَحْمَةُاللّٰهِعَلَيْه analemba kuti: “Pali mawu ambiri oterowo amene amapempha kwa munthu woyankhulayo kuti: Musatitulutse ife pa lilime.” *(Minhaj Al-‘Aabideen (Urdu), tsamba. 145, Minhaj Al-‘Abideen, tsamba. 66)*

## Lilime liyenera kukhala m’ndende

Pali mwambi wa chiarabu: “مَا شَیْءٌ اَحَقَّ بِطُوْلِ السِّجْنِ مِنَ اللِّسَانِ” palibe chilichonse choyenera kutsekeredwa m’ndende kuposa lilime. *(Minhaj Al-‘Aabideen (Urdu), tsamba. 210; Minhaj Al-‘Aabideen, tsamba. 96)*

## Kukhazikika pa kupembedza kumabwera chifukwa choteteza lilime

M'modzi mwa opembedza asanu ndi awiri mwaulemu ananena kwa (M’neneri wokondedwa wa Allah Wamphamvu zonse) Sayyiduna Yunus عَلَیْهِ السَّلَام: “Amene amakhala akulambira ndi khama lonse, kukhazikika kumene amakhala nako polambira, kumachitika chifukwa cha kuteteza lilime mosamalitsa.” Kenako, wopembedzayo anati: “Palibe chilichonse choyenera kukondedwa kwambiri ndi inu kuposa kuteteza lilime, chifukwa iyi ndi njira yokhayo yoyeretsera mtima ku manong'ononong'o onse oyipa a satana.” *(Minhaj Al-‘Aabideen (Urdu), tsamba. 210; Minhaj Al-‘Aabideen, tsaamba. 96-97)*

## Kudzikakamiza kunena zopanda pake (Nkhani)

Sayyiduna Malik Ibn Zaigham رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti: “Bambo anga wolemekezeka anandiuza ine kuti Sayyiduna Qaisi رَحْمَةُاللّٰهِعَلَيْه anatiyendera pambuyo pa Asr ndipo anafunsa za abambo anga. Tinayankha kuti, ‘Akugona.’ Iye رَحْمَةُاللّٰهِعَلَيْه anati, “Kodi akugona pambuyo pa Asr? Nthawi



www.dawateislami.net

zino? Kodi ino ndi nthawi yoyenera kugona?" Kenako, iye رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه anabwelera. Tinatuma munthu pambuyo pake kuti akamuuze kuti abwerere ndipo ndikawadzutsa. Munthuyo anabwerera pambuyo pa Maghrib. Choncho, tinamufunsa kuti, 'Kodi unamufotokozera uthengawo?' Iye ananena kuti: Anatanganidwa kwambiri ndi iye mwini kotero sanasamale za mawu anga. Ndinawona kuti anali akulowa m'manda ndipo anali akunena kwinaku akuzidzudzula yekha kuti: Munthu akhoza kugona nthawi iliyonse yomwe akufuna. Nchifukwa chiyani unanena kuti, "Kodi ino ndi nthawi yanji yogona? Siumayenera kufunsa funso lopanda pake." Tsopano, ndalumbira kwa Allah Wamphamvu zonse ndipo sindidzaphwanya, kuti sindidzakulola kugona chaka chonse. Nditamva izi, ndinamusiya ndipo ndinabwerera." *(Allah walon ki baatayn, buku. 6, tsamba. 269 – 280)*

سُبۡحٰنَ اللّٰه! Mbali ina, kuli machitidwe a anthu athu achipembedzo akale; kumbali ina, kuli mkhalidwe wathu woyipa womwe oti nthawi zonse timakhala ndi zotsutsana zosafunikira, kudzudzula kopanda pake komanso mafunso osafunikira. Tikanapeza njira yotetezera lilime lathu!

## Nditha kupirira kusala kudya kwa nyengo yotentha kwambiri koma …

Sayyiduna Yunus Ibn Ubaid رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه ananena (chifukwa chodzichepetsa) kuti: "Nafs yanga imatha kupirira ululu wosala kudya mu kutentha kwambiri kwa (mzinda wa Iraq) Basra, koma ilibe mphamvu yosiya ngakhale mawu amodzi kuchokera pazokambirana zopanda pake." *(Minhaj al-'Aabideen (Urdu), tsamba. 141; Minhaj al-'Aabideen, tsamba. 64)*

## Lilime ndi loyenera kwambiri chitetezo

O omukonda Rasool, ndithudi, kusasunga ziwalo zobisika kuchokera ku machimo ndi tchimonso lalikulu, Haraam ndi ntchito imene imatsogolera ku Gahena, ndipo mosakaikira, pali zabwino poyankhula zabwino ndipo pali zoipa poyankhula zoyipa. Mwinamwake, ku Bwalo la Chiweruzo, lilime lidzawapagitsa anthu ambiri otchuka kukhala m'mavuto. Ndikofunikira kwambiri kuliteteza. Tabi'i woyera mtima, Sayyiduna Abu Hazim رَحْمَةُاللّٰہِعَلَيْه ananena kuti: "Wokhulupirira ayenera kuteteza lilime lake kuposa ziwalo zake zobisika." *(Allah walon ki baatayn, buku. 3, tsamba. 331; Hilyat-ul-Auliya, buku. 3, tsamba. 267, mawu nambala: 3909)*

## Chifukwa chimodzi choyambitsa kusowa kwa chakudya

Sayyiduna Malik Ibn Dinar رَحْمَةُاللّٰہِعَلَيْه ananena kuti: "Mukamaona kuuma kwa mtima wanu, kufooka kwa thupi lanu komanso kuchepa kwa chakudya chanu, dziwani kuti munayankhula zinthu zopanda pake kuchokera pakamwa panu." *(Minhaj al-'Aabideen, tsamba. 65; Minhaj al-'Aabideen (Urdu), tsamba. 142)*

## Allah Wamphamvu zonse amamva zinthu zonse

Sayyiduna Bishr Haafi رَحْمَةُاللّٰہِعَلَيْه amkayankhula pang'ono ndipo ankanena kwa anzake: "Ganizirani zimene mukupangitsa kuti zilembedwe m'mabuku anu a zintchito, chifukwa adzaperekedwa pamaso pa Mbuye wanu Wopatsa. Choncho, woyankhula zoyipa, tsoka kwa iye! Ngati, pamene mukulembera mnzanu chinachake, mwalemba mawu oyipa mmenemo, ndiye kuti zoyipazo zidzatengedwa ngati zake komanso zanu.



www.dawateislami.net

Ndiye, kodi vuto lanu ndi chiyani ndi Allah Wamphamvu zonse?” *(Tanbih al-Mughtareen, tsamba. 190)*

## Bwanji munakakhala kuti muzilipira ndalama chifukwa choyankhula choyankhula zopanda pake?

Sayyiduna Malik Ibn Dinar رَحۡمَةُ اللّٰہِ عَلَیۡہ anati: “Ngati angelo amene amalemba ntchito zanu, anakhala kuti amakufunsani ndalama tsiku lililonse pa mabuku amene amalembera ntchito zanu, ndiye (pofuna kusunga ndalama) munakasiya zambiri zomwe mumayankhula zopanda pake, koma ngakhale mukudziwa kuti mabukuwa (odzaza ndi zokambirana zanu zopanda pake) adzaperekedwa pa bwalo lolemekezeka la Ambuye wanu Wamphamvu zonse, nchifukwa chiyani simudziletsa nokha (kuchokera ku mkambirano opanda pake)?” *(Ibn Asakir, buku. 56, tsamba. 418)*

## Angelo amalemba china chilichonse

Pamene anthu olemekezeka ali pamaso pa munthu kapena pamene munthu akuyenera kupita kwa atsogoleri a dziko lapansi, lilime limakhala lotetezedwa kwambiri, koma ngakhale amadziwa kuti angelo olemekezeka akulemba chilichonse, Mulungu amadziwa chifukwa chake chimene anthu amalimbira mtima ndi kumayankhula mawu opanda manyazi ndi osayenera komanso momwe mawu otukwana amatulukira pakamwa!

Sayyiduna Imam Hasan Basri رَحۡمَةُ اللّٰہِ عَلَیۡہ anati: “Ndimadabwa ndi munthu oti Kiraman Katibeen (angelo olemekezeka, olembera) ali naye limodzi, ndipo lilime lake ndi cholembera chawo ndipo malovu ake ndi inki yawo,



www.dawateislami.net

komabe, amayankhula mawu osayenera (zokambirana zopanda pake komanso zonyansa).” *(Tanbih al-Mughtareen, tsamba. 190)*

*Ilahi buri guftugu say bachana*

*Mayri yawa-goyi ki ‘aadat mitana*

*Tanthauzo la Yawagoi: Kuyankhula zinthu zopanda pake.*

## Nkhani yokhudzana ndi mkambirano opanda pake

Hazrat Abu Ubaid رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza kuti: Tinapita pa maso pa Hazrat Muhammad Bin Suqah رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ndipo iye anati, ‘Kodi ndikufotokozereni chinthu chomwe chinandipindulitsa ine, ndipo n'zotheka kuti chikhoza kukupindulitsaninso? Tsiku lina Hazrat Ata Bin Abu Rabah رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti, “O mzukulu wanga! (anthu anu) a m'mbuyomu sankakonda zokambirana zopanda pake. Kupatula kuwerenga Qur'an Yopatulika, kulamula zabwino, kuletsa zoyipa ndikukambirana zofunikira, amaphatikizanso mitundu ina yonse ya zokambirana mu 'zokambirana zopanda pake'. Kodi mukukana malamulo awa a Allah Wamphamvu zonse?" (Ngati momwe zafotokozedwera kuti:)

وَ اِنَّ عَلَيْكُمْ لَحٰفِظِيْنَ ﴿۱۰﴾ كِرَامًا كَاتِبِيْنَ ﴿۱۱﴾

*Ndipo ndithudi pali alonda ena (oikidwa) pa inu. Alembi olemekezeka ( Kiraaman Kaatibeen).*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 30, Surah Al-Infitaar, mavesi 10-11)*

(Zafotokozedwa mu vesi lina loyera:)

عَنِ الْيَمِيْنِ وَ عَنِ الشِّمَالِ قَعِيْدٌ ﴿۱۷﴾ مَا يَلْفِظُ مِنْ قَوْلٍ اِلَّا لَدَيْهِ رَقِيْبٌ عَتِيْدٌ ﴿۱۸﴾



www.dawateislami.net

*Pamene (angelo) awiri owerengera amamulembera (mbiri); wina atakhala kumanja ndipo wina kumanzere. Iye samayankhula mawu, kungopatula kuti pali mngelo wokonzeka kulemba amene amakhala pafupi naye.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 26, Surah Qaaf, mavesi 17-18)*

Kodi palibe mmodzi wa inu amene angachite manyazi kuti ngati Buku lanu la Ntchito za tsiku lonse litatsegulidwa pamaso panu, nthawi zambiri mumapeza zinthu m'bukumo zomwe sizikugwirizana ndi chipembedzo kapena ndi dziko lapansi. *(Allah walon ki baatayn, buku. 3, tsamba. 440)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب!     صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Mfundo za Madani zisanu ndi ziwiri (7) za Farooqi

Khalifah wachiwiri wa Asilamu, Sayyiduna Umar Farooq-e-A'zam رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anati:

1. Munthu amene amapewa kuyankhula zopanda pake amapatsidwa nzeru ndi luntha.

2. Munthu amene amapewa kuyang'ana kwake kopanda pake, ndiko kuti, amene amazitalikitsa kuchokera ku kuyang'ana zinthu zosafunikira kapena kuyang'ana zinthu zosiyanasiyana kapena malo angapo osafunikira amapatsidwa mtima wodandawula.

3. Munthu amene amazitalikitsa kuchokera ku chakudya chopanda pake (ndiko kuti, kudya zosafunikira kapena kudya zakudya zosiyanasiyana chongofuna kukoma basi) amapatsidwa kukoma mu kulambira.



www.dawateislami.net

4. Amene amapewa kuseka mopanda pake amapatsidwa ulemu.

5. Amene amapewa kuwaseka anthu ena amapatsidwa kuwala kwa Chikhulupiriro.

6. Amene amazitalikitsa kuchokera ku kukonda dziko lapansi amapatsidwa chikondi cha Dziko likubwera.

7. Amene amazitalikitsa kuchokera ku kupeza zolakwa za wina aliyense amapatsidwa kukonza zolakwa zake *(Al-Munabahat, tsamba. 89-90, Zatengedwa kuchokera)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kuyankha mlandu wa mkambirano opanda wake kudzakhala kotalika

Zafotokozedwa kuti:

اِيَّاكَ وَالْفُضُوْلَ فَاِنَّ حِسَابَهٗ يَطُوْلُ

*Kumasulira: Pewani zokambirana zopanda pake, chifukwa kuyankha mlandu kwake kudzakhala kwakutali.*

*(Minhaj-ul-ʻAabideen, tsamba. 67; Minhaj-ul-ʻAabideen, (Urdu) tsamba. 147)*

## Kukhala kutali ndi zoyankhula zopanda pake kuti mupewe mavuto

Munthu wina woyera mtima,

اِحْفَظْ لِسَانَكَ لَا تَقُوْلُ فَتُبْتَلِى، اِنَّ الْبَلَاءَ مُوَكَّلٌ بِالْمَنْطِقِ



www.dawateislami.net

*Kumasulira: Tetezani lilime lanu. Khalani kutali ndi zokambirana zopanda pake kuti mupewe mavuto. Ndithudi, mavuto amalumikizana ndi zokambirana.* *(Minhaj-ul-'Aabideen, tsamba. 67)*

## Kuyankhula kumasonyeza nzeru za munthu woyankhula

Hazrat Abdullah Ibn-e-Mubarak رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti,

(١ أَلَا احْفَظْ لِسَانَكَ إِنَّ اللِّسَانَ، سَرِيْعٌ إِلَى الْمَرْءِ فِيْ قَتْلِهِ

(٢ (وَإِنَّ اللِّسَانَ دَلِيْلُ الْفُؤَادِ، يَدُلُّ الرِّجَالَ عَلٰى عَقْلِهِ

Kumasulira

(1) Tetezani lilime lanu, chifukwa chiwalo chaching'ono choterechi chimayika munthu pachiwonongeko nthawi yomweyo.

(2) Ndithudi, lilime ndi umboni wa mtima wa munthu umene umaonetsa mlingo wa nzeru za wokamba nkhani.

*(Minhaj-ul-'Aabideen, tsamba. 66; Minhaj-ul-'Aabideen, (Urdu) tsamba. 144)*

## Malangizo kwa munthu amene amayankhula zonyansa

Pamene Sheikh Afzal-ud-Deen رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه Anamva munthu akuyankhula zinthu zonyansa, iye anati, "E m'bale! Allah Wamphamvu zonse analenga makutu ndi lilime za kapolo Wake kuti azitha kumva ndi kuyankhula zabwino, kumvetsera Qur'an yopatulika, Hadith, Azaan ndi Takbir-e-Tahrimah kuchokera kwa Imam, ndi kumvetsera kwa amene akumulangiza. Komanso, makutu anu ndi lilime lanu sizinapangidwe pofuna kunyoza, miseche, kuwayipitsira mbiri anthu, kunama, kunena za anthu ena ndi kukambirana zopanda pake. E m'bale! Pewa kugwiritsa ntchito makutu ako ndi lilime lako mopanda pake. Ichi ndi chiwonongeko chokwanira. Ndipo ngati mawu aliwonse (a machimo)



www.dawateislami.net

anenedwa chifukwa cha mkwiyo, lapani nthawi yomweyo.” *(Al-Minan Al-Kubra, tsamba. 547)*

## Dawat-e-Islami inandipanga ine kukhala munthu wopemphera Salah

اَلْحَمْدُ لِلّٰه! Malo a zochitikachitika za chipembedzo a Dawat-e-Islami amapindulitsanso alongo achisilamu, kuwonjezera pa abale achisilamu. Mlongo wina wachisilamu wochokera ku Daska (Punjab) anali kutsatira mafashoni oletsedwa komanso kukhala kutali ndi Salah monga ena ambiri. Kenako, anapita kukaphunzira ku Madrasah yachipembedzo yoyang’aniridwa ndi amalume ake kumene alongo ena achisilamu ogwirizana ndi Dawat-e-Islami anabwera kudzayitanira ku msonkhano wapasabata wolimbikitsa Sunnah. Potsatira zimenezi, mzake anamulimbikitsa ndipo nayenso anapezekapo pamsonkhano wachipembedzo. Iye anamvetsera ulaliki wolimbikitsa Sunnah pamsonkhano wachipembedzo. Du’a yamphamvu kwambiri yodzaza ndi misozi inamukhudza ndipo analapa machimo ake. Atagwirizana ndi malo a ochitikachiitika za chipembedzo a Dawat-e-Islami, tsiku lina nayenso anamamaliza ‘Maphunziro a Ntchito 12 za Madani a Alongo Achisilamu’ (amene tsopano amatchedwa kuti Maphunziro a Ntchito za Chipembedzo).

Analandira madalitso ambiri kuchokera ku Dawat-e-Islami moti anayambanso kupemphera Nafl Salah kuwonjezera pa Fard Salah. Chidwi chake ndi chakuti adzachita ntchito zachipembedzo mochuluka m’mudzi mwake ndipo adzakhalabe ndi gulu lachipembedzo la omukonda Rasool, la ‘Dawat-e-Islami’ mpaka kumapeto kwa moyo wake.



www.dawateislami.net

*Pila kar ma`ay ‘ishq dayga bana yeh*

*Tumhayn ‘Aashiq-e-Mustafa madani mahol*

*Aye islami behno! Tumharay li`ay bhi*

*Suno hay bahut kam ka madani mahol*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 648)*

## Lilime lili ngati mkango, wokonzeka kuyendayenda

Hazrat Sayyiduna Ibn-e-Abi Mutee’ رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati,

(١) لِسَانُ الْمَرْءِ لَيْثٌ فِيْ كَمِيْنٍ اِذَا خَلَّى اِلَيْهِ لَهٗ اِغَارَهٗ

(٢) فَصُنْهُ عَنِ الْخَنَا بِلِجَامِ صَمْتٍ يَكُنْ لَكَ مِنْ بَلِيَّاتٍ سِتَارَهٗ

### Kumasulira

(1) (powononga) lilime lili ngati mkango wobisala, wokonzeka kuyendayenda, umene umabweretsa chiwonongeko ukangopeza mpata.

(2) Choncho, mangirirani lilime ndi chingwe cha kukhala chete ndipo mulileletse ku zinthu zopanda pake. Mwanjira imeneyo, udzapulumutsidwa ku zoyipa zambiri.

*(Minhaj-ul-‘Aabideen, tsamba. 66; Minhaj-ul-‘Aabideen, (Urdu) tsamba. 145)*

## chilombo

Munthu wina woyera mtima wa chi Quraish anati, “Ophunzira wina anafunsidwa chifukwa chiyani amakhala chete.” Iye anati, “Ndapeza lilime langa ngati chilombo. Ndimawopa kuti ndikalimasula, lidzandidya.” *(Ayk chup sou sukh (Khamoshi kay Faza`il), tsamba. 21)*



www.dawateislami.net

## Kuteteza chuma ndi kosavuta, koma kuteteza lilime…

Munthu akhoza kuyika chuma m'kabokosi lotetezera ndi kuchiteteza. Ngati pali chuma chambiri, chikhoza kutetezedwa poyika mlonda wokhala ndi zida, koma ndi zabwino ngati wina angapambane poteteza lilime lake. Hazrat Muhammad Waasay رَحۡمَةُ اللّٰہِ عَلَیۡه ananena kwa Hazrat Malik Bin Dinar رَحۡمَةُ اللّٰہِ عَلَیۡه kuti, "Kwa munthu, ndi kovuta kwambiri kuteteza lilime kusiyana ndi kuteteza chuma."

*(Ittihaaf Al-Sadat, buku. 9, tsamba. 144)*

Aliyense nthawi zambiri amakhala wochenjera mokwanira pankhani yoteteza chuma chake. Ngakhale chuma chiwonongeke, kumakhala kuluza kwa pa dziko lapansi lokha. Koma kalanga! Maganizo oteteza lilime ndi osowa. Mopanda kukayikira kulikonse, chifukwa chosateteza lilime, n'kutheka kuti padzakhala chiwonongeko cha Tsiku Lomaliza kuwonjezera pa kuluza kwa pa dziko lapansi.

*Bak bak ki yeh 'adat na sar-e-hashr phansa day*

*Allah zaban ka ho 'ata Qufl-e-Madinah*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 93)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد



www.dawateislami.net

# Zizindikiro 6 za odzipereka

Zanenedwa kuti:

عاشقاں راشِش نشاں سَت اے پسر! آہِ سَردورنگ زَرد چشمِ تر
گِر تُراپُر سَند سِہ دیگرگُدام؟ کم خُورَد، کم گُفتن و خُفْتَن حرام

### Kumasulira

Zotsatirazi ndi zizindikiro zisanu ndi chimodzi za odzipereka: (1) kuusa moyo modandaula (2) khungu lotumbuluka la kunkhope (3) maso odzaza ndi misozi (4) kudya pang'ono (5) kuyankhula pang'ono ndi (6) kugona pang'ono

## Zizindikiro 6 za umbuli

Kukwiya pa mawu aliwonse, kukambirana kopanda pake, kuwononga zinthu mopambanitsa, kuuza anthu zinsinsi, kudalira aliyense, kusapewa maubwenzi oyipa komanso kusasankha maubwenzi abwino – zonsezi ndi zizindikiro za umbuli. Munthu wanzeru anati pali zinthu zisanu ndi chimodzi zimene munthu wosazindikira amadziwika nazo:

1. Pakukwiya, kutanthauza kukwiya pa chilichonse chosagwirizana ndi chikhalidwe chake, kaya chimayambitsidwa ndi munthu kapena nyama, ndi zina zotero.

2. Kukambirana kopanda pake, kutanthauza kuti munthu wanzeru sayenera kulankhula zopanda pake, koma ayenera kulankhula zinthu zothandiza, kaya zothandiza pa dziko kapena pa Tsiku Lomaliza.



www.dawateislami.net

3. Kuwononga zinthu mopambanitsa, kutanthauza kuti ndi chizindikiro cha umbuli kuti munthu ayike ndalama pamalo omwe sangapeze phindu lililonse.

4. Kuuza anthu zinsinsi.

5. Kudalira aliyense.

6. Kusatha kusiyanitsa pakati pa bwenzi ndi mdani, kutanthauza kuti ndi koyenera kuti munthu azizindikira abwenzi ake (kutanthauza anthu olungama), azichita zinthu monga iwo, ndi kutsatira mapazi awo; azizindikira adani ake (kutanthauza anthu oyipa) ndikuyesera kukhala kutali nawo. Mopanda kukayikira kulikonse, mdani woyamba wa munthu ndi Satana. Choncho, sayenera kutsatira Satana pa nkhani iliyonse (ndipo ayenera kusiya machimo amtundu uliwonse). *(Tanbeeh Al-Ghafileen, tsamba. 115, Mwachidule)*

## Zoyipa zinayi za zokambirana zopanda pake

Sayyiduna Imam Abu Hamid Muhammad Ibn Muhammad Ibn Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anadzudzula mkambirano opanda pake chifukwa cha zifukwa zinayi izi:

1. Kiraman Katibeen (kutanthauza angelo olemekezeka amene amalemba zintchito) amayenera kulemba zokambirana zopanda pake. Choncho, munthu ayenera kuchita nawo manyazi ndipo sayenera kuwavutitsa kulemba zokambirana zopanda pake. Allah Wamphamvu zonse akuyankhula mu vesi 18, Surah Qaaf, Gawo 26:

مَا يَلْفِظُ مِنْ قَوْلٍ اِلَّا لَدَيْهِ رَقِيْبٌ عَتِيْدٌ ﴿۱۸﴾

*Iye sayankhula ngakhale mawu amodzi, kungopatula kuti pali mlembi (mngelo) wokonzeka kulemba pafupi naye.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 26, Surah Qaaf, vesi 18)*

2. Si chinthu chabwino kuti Buku la Zintchito lodzaza ndi zokambirana zopanda pake lidzawonetsedwe pa bwalo la Allah Wamphamvu zonse.

3. Kapolo adzalamulidwa kuwerenga Buku lake la Zintchito pa bwalo la Allah Wamphamvu zonse pamaso pa anthu onse. Tsopano adzakumana ndi zilango zaukali pa Tsiku Lachimaliziro. Adzakhala wopanda zovala, wokhala ndi ludzu lalikulu, ndipo msana wake udzakhala ukuphwanyika chifukwa cha njala. Adzaletsedwa kulowa Ku Paradaiso, ndipo zinthu zonse zapamwamba zidzakhala zoletsedwa kwa iye. Tangoganizirani! Kuwerenga Buku la Zintchito lodzaza ndi zokambirana zopanda pake pazovuta zonsezi kudzakhala kosokoneza kwambiri. (Werengerani kuti ngati mwakambirana zopanda pake kwa mphindi 15 tsiku lililonse ndipo ngati titayerekeza kuti mwezi umodzi uli ndi masiku 30, ndiye kuti mwezi umodzi udzakhala ndi maola 7.50 ndipo chaka chimodzi chidzakhala ndi maola 90. Mwachitsanzo, ngati wina wakambirana zopanda pake tsiku lililonse kwa mphindi 15 pafupifupi mpaka zaka 50, adzakhala masiku 187 ndi maola 12, kutanthauza miyezi yoposa isanu ndi umodzi. Tangoganizirani! Pa Tsiku Lachimaliziro lowopsa pamene dzuwa lidzakhala likuwala kuchokera pa mtunda wa kilomita imodzi basi, kutanthauza kuti kudzakhala kotentha kwambiri, ndindani adzathe kuwerenga Buku lake la Zinchito mosalekeza kwa miyezi isanu ndi umodzi pa tsiku lotentha kwambiri. Uku ndi kuwerengera kokambirana zopanda pake tsiku lililonse kwa mphindi 15 ngati



www.dawateislami.net

munthu wakhala ndi moyo zaka 50. Nthawi zina, timakhala maola ambiri ndi abwenzi tikukambirana zopanda pake kupatula zokambirana zoyipa komanso zoyipa zina.)

4. Pa Tsiku Lachiweruzo, kapolo adzadzudzulidwa pa zokambirana zopanda pake, ndipo adzachititsidwa manyazi. Kapolo adzakhala wopanda yankho pa nkhaniyi, ndipo adzachita manyazi kwambiri pamaso pa Allah Wamphamvu zonse. *(Minhaj-ul-'Aabideen, tsamba. 67)*

*Har lafz ka kis tarha hisaab aah! Mayn donga*

*Allah zaban ka ho 'ata Qufl-e-Madihah*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 93)*

صَلُّوا عَلَی الْحَبِیب! صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Phunzirani kukhala chete

Sayyiduna Jabir Bin Abdullah رَضِیَ اللہُ عَنْھُمَا anafotokoza kuti: "Phunzirani kukhala chete kenako phunzirani kuleza mtima, kenako phunzirani maphunziro kenako phunzirani momwe mungagwiritsire ntchito, kenako falitsani (ndi kuphunzitsa) maphunziro." *(Shu'ab-ul-Iman, buku. 2, tsamba. 288, mawu nambala. 1791)*

## Kupembedza kumayamba ndi kukhala chete

Imam Sufyan Sauri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Chiyambi cha kulambira ndi kukhala chete, kenako kupeza maphunziro, kenako kuwaloweza, kenako kuwagwiritsa ntchito, kenako kuwafalitsa." *(Tarikh-e-Baghdad, buku. 6, tsamba. 6)*



www.dawateislami.net

## Kukhala chete ndi kiyi wa kupembedza

Hazrat Imam Sufyan Sauri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza kuti: "Kukhala chete kwambiri ndi chinsinsi cha kulambira." *(Al-Samt ma' Mausu'ah Ibn-e-Abi Al-Dunya, buku. 7, tsamba. 255, mawu nambala. 436)*

## Malangizo asanu abwino kwambiri

Tabi'i woyera mtima Hazrat Imam Mujahid رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza kuti anamumva Sayyiduna Abdullah Bin Abbas رَضِىَ اللّٰهُ عَنْهُمَا akunena kuti amakonda zinthu zisanu kuposa akavalo akuda abwino, okonzeka kuwakwera:

1. Osakambirana zopanda pake, chifukwa zilibe ntchito, ndipo ndikuwopa kuti mutenga nawo mbali muzochita zauchimo, ndipo musamakambirane zinthu zothandiza popanda nthawi yabwino, chifukwa anthu ambiri amene amakambirana zinthu zothandiza amagwa m'mavuto pokambirana zinthu zothandiza popanda nthawi yabwino.

2. Musatsutsane ndi munthu wopirira ndi woleza mtima komanso wopanda nzeru ndi wopusa, chifukwa (n'kutheka kuti) wopirira (akhoza kukwiya ndipo) akhoza kuyamba kukudani inuyo, koma wopusa (adzayankhula zopanda pake) ndikukuvulazani.

3. Tchulani za m'bale wanu kumbuyo kwakenso (iyeyo palibe) monga momwe mumafunira kuti iye azikamba zokhudza inu; ndipo mukhululukireni pazinthu zimene mukufuna kuti iye akukhululukireni.

4. Chitirani m'bale wanu zabwino monga momwe mukufunira kuti iye akuchitireni inu zabwino.

5. Chitani ngati munthu amene amakhulupirira kuti adzapatsidwa (mphoto yabwino) pa ntchito iliyonse ndipo adzagwidwa pa tchimo lililonse. *(Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 344)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Mahadith anayi okhudzana ndi kukhala chete

1. "مَنْ صَمَتَ نَجَا" Kutanthauza kuti aliyense amene amakhala chete amapulumuka. *(Tirmizi, buku. 4, tsamba. 225, Hadith. 2509)*

**Kufotokozera Hadith:** Kutanthauza kuti kukhala chete kumabweretsa chipulumutso, koma kulankhula zabwino, kulamula zabwino, kuletsa zoyipa, kukhala wokhazikika popanga ma Zikr, ndi kuwerenga Qur'an yoyera n'kwabwinoko kuposa kukhala chete. *(Al-Istizkaar, buku. 7, tsamba. 372)* Malingana ndi Hazrat 'Allamah Munawi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, tanthauzo la Hadith imeneyi yolemekezeka ndilakuti: (مَنْ صَمَتَ) عَنِ النُّطْقِ بِالشَّرِّ (نَجَا) Kutanthauza kuti, aliyense amene amakhala chete (osayankhula chilichonse choyipa) amapeza chipulumutso. *(Al-Tayseer, buku. 2, tsamba. 428)*

2. "اَلصَّمْتُ سَيِّدُ الْاَخْلَاق" Kutanthauza kuti kukhala chete ndi mtsogoleri wa makhalidwe abwino. *(Al-Firdaus, buku. 2, tsamba. 417, Hadith. 3850)*



www.dawateislami.net

3. "اَلصَّمْتُ اَرْفَعُ الْعِبَادَةِ" Kutanthauza kuti kukhala chete ndi mlingo wapamwamba wa kulambira.

*(Al-Firdaus, buku. 2, tsmba. 417, Hadith. 3849)*

**Kufotokozera Hadith:** Kutanthauza kuti kukhala chete ndi chimodzi mwa mitundu yabwino kwambiri ya kupembedza, chifukwa zolakwa zambiri zimachokera pa lilime.

*(Siraj-e-Muneer Sharh Jami'-us-Sagheer, buku. 3, tsamba. 279)*

4. "اَلصَّمْتُ زَيْنٌ لِّلْعَالِمِ، وَسِتْرٌ لِّلْجَاهِلِ" Kutanthauza kuti kukhala chete ndi kukongola kwa munthu wophunzira komanso chophimba kwa munthu wosazindikira. *(Jami'-e-Sagheer, tsamba. 318, Hatidh 5169)*

## Zabwino kuposa kupembedza kwa zaka 60

Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Kukhala chete n'kwabwino kuposa kupembedza kwa zaka makumi asanu ndi limodzi." *(Shu'ab-ul-Iman, buku. 4, tsamba. 245, Hadith 4953)*

**Kufotokozera Hadith:** Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena motere ponena za Hadith yodalitsikayi: "Ndiko kuti, ngati munthu akupembedza kwa zaka 60 koma amayankhula kwambiri ndipo samasiyanitsa pakati pa kukambirana kwabwino ndi koyipa, ndi bwino kuti akhale chete kwakanthawi, pakuti kukhala chete kumaphatikizaponso kulingalira (za Tsiku Lomaliza), kusintha kwa Nafs, kumira mu kumukumbukira Allah Wamphamvu zonse, kumira mu nyanja ya Zikr-e-Khafi (ya mumtima) ndi kusinkhasinkha (kumira mu



www.dawateislami.net

kumukumbukira Allah Wamphamvuyonse komanso kusiya zina zonse). *(Mir'aat, buku. 6, tsamba. 361)*

## Yankhulani zokhudza chinthu chabwino kapena khalani chete

Zikanakhala kuti Hadith yodatsikayi ya Sahih Bukhari ikumalowa kwambiri m'maganizo mwathu, yomwe imaphatikizanso, "مَنْ كَانَ يُؤْمِنُ بِاللّٰهِ وَالْيَوْمِ الْاٰخِرِ فَلْيَقُلْ خَيْرًا اَوْلِيَصْمُتْ" aliyense amene amakhulupirira Allah Wamphamvu zonse ndi Tsiku la Chiweruzo ayenera kuyankhula zabwino kapena kukhala chete. *(Bukhari, buku. 4, tsamba. 105, Hadith 6018)*

## Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amkakhala chete nthawi yayitali

"كَانَ رَسُوْلُ اللّٰهِ صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم طَوِيْلَ الصَّمْت" Mtumiki Woyera amkakhala chete kwa nthawi yayitali. *(Sharh-us-Sunnah, buku. 7, tsamba. 45, Hadith 3589)* Hazrat Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena pofotokoza tanthauzo la Hadith yodalitsikayi kuti: "Kukhala chete kumatanthauza kukhala chete pa nkhani za dziko; apo ayi, lilime la Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse limakhala lotanganidwa ndi kumukumbukira AllahWamphamvu zonse. Sankayankhula ndi anthu mopanda cholinga. Zonsezi ndi zokhudza kukambirana kololedwa; lilime lake lodalitsika silimkapanga mkambirano osaloledwa. Kunama, miseche, kunena nkhani za anthu ena, ndi zina zotero sizimkabwera konse pa lilime lake lodalitsika pa moyo wake wonse wodala. Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi chitsanzo cha choonadi, choncho bodza lingamfikire bwanji? *(Mir'aat, buku. 8, tsamba. 81)*



www.dawateislami.net

## Kalanga! Anthu ambiri anachokapo atamva kuwerengedwa kwa Qur'an

Sayyiduna Ubaid Bin Abu Ja'd رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza kuti pamene anthu anadziwa kuti sahaba wa Mtumiki Sayyiduna Salman Farsi رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ ali mu Mzikiti wa Madain (mzinda wa Iraq), anthu anayamba kubwera kwa iye mpaka pafupifupi anthu okwana chikwi chimodzi (1000) anasonkhana pamenepo. Iye رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anayimirira ndi kunena kuti, "Nonse khalani pansi." Pamene anthu anakhala pansi, iye رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anayamba kuwerenga Surah Yusuf. Anthu anayamba kuchoka pang'onopang'ono mpaka panatsala anthu zana limodzi (100) okha. Iye mokwiya anati, "Mumafuna kumvetsera zongopeka komanso zopanda pake, koma pamene ndinakupangani kumvetsera Mawu a Allah, munanyamuka ndi kuchoka." *(Hilyat Al-Awliya, buku. 1, tsamba. 261, mawu nambala. 643; Allah walon ki baatayn, buku. 1 tsamba. 377)*

## Chikondi chomvetsera kuwerengedwa kwa Qur'an

O omukonda Rasool! Kuwerenga Qur'an Yopatulika ndikuyimvetsa ndi ntchito ya malipiro akulu. Kalanga! Chidwi chochepa tsopano chikupezeka pakati pa anthu. Ngati Qari akuwerenga, sitikonda kumvetsera. Zokhudza kufunitsitsa kwa masahaba olemekezeka رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُم pakuwerenga Qur'an, zafotokozedwa mu *Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 1, pa tsamba 845:* "Zikunenedwa kuti pamene masahaba wolemekezeka رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُم amkasonkhana, amkapempha m'modzi wa iwo kuti awerenge Surah iliyonse ya Quran yopatulika." *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 1, tsamba. 372)*

## Ubwino omvetsera ndime imodzi yoyera

Sayyiduna Abdullah Bin Abbas رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُمَا anati," Aliyense amene angamvetsere vesi imodzi ya mu Qur'an Yopatulika, idzakhala Nur [kuwala] kwa iye pa Tsiku la Chiweruzo." *(Musnaf 'Abd-ur-Razzaq, buku. 3 tsamba. 229, mawu nambala. 6032)*

Kodi mwawona? Mphotho yakumvetsera Qur'an Yopatulika ndi yayikulu kwambiri, ndipo wowerengayo amene ndi chifukwa cha mphothoyi amagawananso nawo mphothoyo malinga ngati alibe cholinga choziwonetsera.

## Kuvutika zaka 20 mu kuwerenga Qur'an

Kaya mukumazipeza zosangalatsa kapena ayi, kupembedza komanso kuwerenga Qur'an ziyenera kupitirira. اِنْ شَآءَاللّٰه Tsiku lina, mudzayamba kuzipeza zosangalatsa. Hazrat Sayyiduna Sabit Bunani رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Ndinavutika kwa zaka 20 ndi (kuwerenga kwa) Qur'an Yopatulika (ngakhale sindinazipeze kukhala zosangalatsa), ndipo pambuyo pake ndinapeza chisangalalo chake kwa zaka 20."

*(Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 1, tsamba. 871)*

*Har roz mayn Qur`an parhon kash! Khudaya*

*Allah! Tilawat mayn mayray dil ko laga day*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد



www.dawateislami.net

## Ngati mukufuna Paradiso, musayankhule kungopatula zabwino

Pamene chilichonse chabwino chokha chidzatuluka pa lilime ndipo Zikr-o-Durood zidzanenedwa, simudzakhala ndi chizolowezi cholankhula zopanda pake. Mudzakhalanso kutali ndi machimo monga kunama, miseche, kukamba nkhani za anthu ena, kupeza zolakwika, ndi zina zotero. Mwanjira imeneyo, إِنْ شَآءَاللّٰه, padzakhala njira zolowera Ku Paradaiso. Sayyiduna Imam Muhammad Bin Muhammad Bin Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba kuti anthu modzichepetsa anamufunsa Sayyiduna Eisa Ruhullah عَلَيْهِ السَّلَام za ntchito yomwe imatsogolera ku Paradaiso. Iye عَلَيْهِ السَّلَام anati, "Osayankhula nkomwe." Anthu modzichepetsa anati, "Izi sizingatheke." Iye anati, "Osayankhula chilichonse kungopatula chinthu chabwino." *(Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 336; Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 136)*

*Aksar mayray honton pay rahay Zikr-e-Madinah*

*Allah zaban ka ho 'ata Qufl-e-Madinah*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 93)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kulapa kwenikweni kuchokera ku machimo

O inu ofunafuna Paradiso! Tidaphunzira kuchokera m'nkhaniyi kuti kuwongolera lilime ndi kudziletsa ku zokambirana zosafunikira ndi zinthu zomwenso zimatsogolera ku Paradiso. Mutateteza lilime ndi ziwalo zina za thupi ku machimo, kuti mupeze chidwi chochita zinthu zomwe zimatsogolera ku Paradiso, gwirizanani ndi malo zichitochito za



www.dawateislami.net

chipembedzo a Dawat-e-Islami. اِنْ شَآءَاللّٰه, Mudzapindula. Kuti muwonjezere chidwi cholandira madalitso a tsiku lomaliza, 'Nkhani ya Madani' yabweretsedwa kwa inu. Kalekale, mayi wina wa ku Sindh ankagwira ntchito pamalo pomwe panali kuchotsa chophimba ndi kuyang'ana molakwika, kuwonjezera pa zoyipa zina zambiri zomwe mwatsoka sizimaonedwa ngati zoyipa m'dera la masiku ano. Zinali zotsatira za malo oyipa amenewo kuti iye anayamba kukonda kuonera mafilimu ndi masewero, kumvera nyimbo, kutsatira mafashoni osaloledwa, ndi kuyendayenda opanda chophimba chilichonse. Kusamvera makolo ake, komanso kuwatonza ndi kuwayankha achikulire ake pobwenzera kunali mbali ya chizolowezi chake. Tsiku lina mlongo wina wachisilamu woziphimba wovala Burqa anabwera kunyumba kwake. Pamene mlongo wachisilamu anachotsa chophimba chake pamaso pa mayiyo, anadabwa kuona kuti mlongo wachisilamu anali mnzake wakale amene anali ngati iye amene ankakhala opanda chophimba ndikutsatira mafashoni oyipa. Mlongo wachisilamu anasiya ntchito kalekale, ndipo tsopano anali mlaliki wa Dawat-e-Islami. Poona kusintha kwakukulu m'nthawi yochepa kwambiri, mayiyo sanathe kudziletsa ndipo anachita chidwi kwambiri. Mlongo wachisilamu mwaulemu anamuyitanira ku chilungamo ndikumulimbikitsa kuti atenge nawo mbali pamsonkhano wa sabata uliwonse wolimbikitsa Sunnah wa Dawa-e-Islami wa alongo achisilamu. Mayiyo anatsimikza zotenga nawo mbali pamsonkhano wachipembedzo. Kusintha kwakukulu kumene kunabwera m'moyo wa mlongo wachisilamu kunali kutagunda kale mtima wake, tsopano kutenga nawo mbali pamsonkhano wolimbikitsa Sunnah ndi ulaliki odzazidwa ndi kuganizira za tsiku lomaliza kunangomudzutsa ku tulo takunyalanyaza. Du'a yamphamvu kwambiri komanso yodzaza ndi misozi yopemphedwa kumapeto kwa msonkhano wachipembedzo inawonjezera mafuta pamoto. Sanathe kudziletsa ndipo anagwetsa misozi.



www.dawateislami.net

Anali ndi manyazi pa machimo ake ndipo analapa moona mtima pamaso pa Allah Wamphamvu zonse. Tsopano akuthokoza kwambiri Allah Wamphamvu zonse kuti anamudalitsa ndi Dawat-e-Islami kuti atuluke mu dzenje la machimo.

*Salaamat rahay Ya Khuda madani mahol*

*Bachay bad nazar say sada madani mahol*

*Du'a hay yeh tujh say dil aysa laga day*

*Nah chotay kabhi bhi Khuda madani mahol*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kukhala chete ndi gwero la chitetezo cha chikhulupiliro

Aliyense amene lilime lake limadula mkambirano wa aliyense ngati lumo, sadzatha kumvetsa bwino zomwe munthu wina akunena. Ndipotu, kuwopa kumeneku kumakhalanso kwa munthu wolankhula kwambiri kuti angathe مَعَاذَالله kulankhula mawu okanira pamene akukamba zopanda pake. Hazrat Imam Abu Hamid Muhammad Bin Muhammad Bin Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba mu '*Ihya-ul-'Uloom*' kuti ophunzira ena achipembedzo akale anati, "Mikhalidwe iwiri imasonkhana mwa munthu wodekha:

1. Chipembedzo chake chimakhala chotetezedwa, ndipo
2. Amamvetsetsa munthu wina bwino kwambiri."

*(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 137)*

## Chinsinsi chokhala woyikidwiratu ku Paradaiso (Nkhani)



www.dawateislami.net

Mwa chisomo cha Allah Wamphamvu zonse, Mtumiki wathu wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankangowayang'ana anthu ndikuwadziwa ngati adzalowe ku Paradaiso kapena ku Gahena. Ndipotu, ankalandira nkhani kale ngati munthuyo adzalowe Kumwamba kapena ku Gahena. Mtumiki Womaliza صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم tsiku lina anati, "Munthu woyamba kulowa pakhomo ili adzalowa ku Paradaiso." Panthawiyo, Sayyiduna Abdullah Bin Salaam رَضِیَ اللّٰہُ عَنْهُ analowa pakhomo limenelo. Iye anati, "Ntchito yanga ndi yochepa kwambiri, ndipo chinthu chimene ndilinacho chiyembezo kuchokera kwa Allah Wamphamvuzonse ndi kuteteza mtima wanga ndi kusiya zokambirana zopanda pake." *(Al-Samt, buku. 7, tsamba. 86, mawu nambala. 111)*

Tanthauzo la "سَلَامَتُ الصَّدْر", chitetezo cha mtima mu Hadith yodalitsikayi ndi chakuti mtima ukhale wopanda matenda amkati (mwachitsanzo, matenda obisika a machimo) monga chidani, nsanje, ndi zina zotero, ndipo chikhulupiriro chikhale champhamvu mumtima.

*Raftar ka guftar ka kirdaar ka day day*

*Har 'uzw ka day mujhko Khuda Qufl-e-Madinah*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 95)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Sahabi aliyense wa Mtumiki anayikidwiratu kuti akalowa ku Paradaiso

سُبْحٰنَ اللّٰه! Thanzi lathu, thupi lathu, moyo wathu ndi chuma chathu ziperekedwe nsembe kwa Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم!



www.dawateislami.net

Tsogolo la sahaba, Abdullah Bin Salam رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ ndi loyamikirika kuti iye رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ analandira uthenga wabwino woti adzakhala wokhala ku Paradaiso kuchokera pa lilime lodalitsika la Mtumiki Woyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم. Ndithudi, iye adzalowâ ku Paradaiso. Ndipo si iye yekha, sahabi aliyense adzalowâ ku Paradaiso. Zanenedwa m'masamba 329-330 a *'Faizan-e-Namaz'*: Allah Wamphamvu zonse wanena mu vesi 10, Surah Al-Hadeed, Gawo 27:

لَا یَسْتَوِیْ مِنْكُمْ مَّنْ اَنْفَقَ مِنْ قَبْلِ الْفَتْحِ وَ قٰتَلَ ؕ اُولٰٓىٕكَ اَعْظَمُ دَرَجَةً مِّنَ الَّذِیْنَ
اَنْفَقُوْا مِنْۢ بَعْدُ وَ قٰتَلُوْا ؕ وَ كُلًّا وَّعَدَ اللّٰهُ الْحُسْنٰى ؕ وَ اللّٰهُ بِمَا تَعْمَلُوْنَ خَبِیْرٌ۠ ﴿۱۰﴾

*Sangafanane mwa inu (Masahaba a Mtumiki Wokondedwa) amene anapereka chuma ndi kumenya nkhondo Makkah isanati kutsegulidwa ndi ena, iwo ndi opambana pa ulemerero kuposa amene anapereka chuma ndi kumenya nkhondo pambuyo pa kutsegulidwa kwa Makkah. Ndipo Allah wawalonjezera Paradaiso onse; ndipo Allah Ngodziwa za ntchito zanu.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 27, Surah Al-Hadeed, vesi 10)*

## Masahabah onse anayikidwiratu kuti akalowa ku Paradaiso

Wothitrira ndemanga wa Quran Yopatulika, Hazrat Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena za vesi lopatulikali kuti: “Ngakhale kuti milingo ya ulemerero ya Masahaba amenewa ndi yosiyana, koma palibe kukayika kuti Masahabah onse رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُم adzalowâ ku Paradaiso, chifukwa Ambuye Wamphamvu zonse anawalonjeza. Masahaba onse ndi olungama komanso ochita zabwino chifukwa Ambuye Wamphamvu zonse



www.dawateislami.net

anawalonjeza onse Paradiso. Lonjezo la Paradiso silipangidwa ndi Fasiq (wochimwa).” (Malingana ndi *Noor-ul-Irfan*, zanenedwa za vesi lopatulika lomwe latchulidwa pamwambapa), "chifukwa chakuti Sahabi aliyense ndi wotsatira wa Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, Ndi Wajib kuti tiziwalemekeza onse, ndipo kusawalemekeza Sahabi aliyense ndi Haraam komanso kusochera.”

*Har Sahabi-e-Nabi: Jannati Jannati*

*Sab Sahabiyat bhi: Jannati Jannati*

*Char Yaran-e-Nabi: Jannati Jannati*

*Hazrat-e-Siddeeq bhi: Jannati Jannati*

*Hayn ‘Umar Farooq bhi: Jannati Jannati*

*‘Usman-e-Ghani: Jannati Jannati*

*Fatimah aur ‘Ali: Jannati Jannati*

*Hayn Hasan Hussain bhi: Jannati Jannati*

*Walidayn-e-Nabi: Jannati Jannati*

*Har Zoujah-e-Nabi: Jannati Jannati*

*Aur Abu Sufiyan bhi: Jannati Jannati*

*Hayn Mu’awiyah bhi: Jannati Jannati*

Okondedwa abale achisilamu! Ngakhale‘mkambirano wopanda pake si tchimo, komabe mulibe madalitso. سُبْحٰنَ اللّٰه! Mwangowerenga nkhani yomwe Sahabi analandira nkhani yabwino ya Paradiso padziko lapansi kuchokera pa lilime lodalitsika la Wolemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. modzi mwamakhalidwe ake analinso kuti sanali kuchita nawo zokambirana



www.dawateislami.net

zopanda pake. Iye رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ samkafunsa chilichonse chomwe analibe nacho chochita. Koma kalanga! Ife timalowererabe nkhani zomwe tilibe nazo chochita ndipo timafunsa za nkhanizi popanda cholinga.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب!　　　صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kudya kwambiri ndi chifukwanso chimodzi choyambitsa kuyankhula kwambiri

Mu Qur'an ndi Hadith, muli kudzudzula za kudya ndi kumwa **kwambiri chifukwa cha kukoma chabe.** Pamene mimba yakhuta **kwambiri**, munthu amakonda kuchita zinthu zoyipa lilime limayambanso kuyenda ngati lumo; ndipo munthu akayamba kumva njala, amakhala waulesi; samafuna kuyankhula kwambiri. Hazrat Sheikh Abdul Wahhab Sha'rani رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَیْه anati: "Anthu akale athu (kutanthauza, anthu oyera mtima achisilamu omwe anamwalira) amkapirira njala yayikulu ndipo samkadzaza mimba zawo ndi cholinga chakuti akhale chete kwambiri ndipo zokambirana zawo zopanda pake zichepe, monga momwe chinaliri chizolowezi cha ophunzira athu achisilamu akale رَحِمَهُمُ اللّٰہُ. Izi zili chonchi chifukwa aliyense amene amakhala okhuta, mchitidwe wake woyankhula zopanda pake umawonjezereka." *(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 189)*

## Aliyense amene amadya opanda chilakolako ndi munthu wokonda kuyankhula

Hazrat Sayyiduna Muhammad Rahibi رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَیْه anati: "Zokambirana zopanda pake zidzatulukanso pakamwa pa munthu amene amadzaza mimba yake ndi zakudya zosafunikira." *(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 189)*

## Mawu oyipa amacheka kwambiri kuposa lupanga



www.dawateislami.net

Muvi ndi lupanga zimangovulaza thupi, komano mtima umavulazidwa ndi lilime. Hazrat Sufyan Sauri رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ ananena kuti kumenya munthu ndi muvi sikumakhala koopsa kuposa kunena mawu oyipa kwa iye, chifukwa zolinga za lilime sizimaphonyedwa. *(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 189)*

## Sungani lilime kukhala lomangidwa

Aliyense amene angathe kumanga lilime lake, adzapulumutsidwa ku zoyipa zambiri. Sahaba wa Mtumiki, Sayyiduna Abdullah Bin Mas'ood رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anati, "Ndikulumbira Mwa Allah Wamphamvu zonse, kungopatula Iye palibenso woyenera kupembedzedwa, palibe chofunika kwambiri kuti chikhale m'ndende kuposa lilime." *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 137; Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 338)*

## Mawu osayenera pakamwa sangakhalenso oyenera kulikonse

Ganizirani mosamala musanalankhule, chifukwa ndikotheka kuti munganyozeke pambuyo pake. Hazrat Sayyiduna Imam Shafi'i رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَيْه (mtsogoleri wa mamiliyoni a anthu a Shafi'i) anati mawu ali ngati muvi. Ngati mutawatulutsa, munthu wina adzakhala mwini wake ndipo simudzakhalanso mwini wake. *(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 189)*

*Bashar raz-e-dili keh kar zaleel-o-khuwar hota hay*

*Nikal jati hay jab khushboo to gul baykar hota hay*

مَا شَآءَ الله! Anthu ena ndi anzeru kwambiri komanso osunga zinsinsi. Samaulula chinsinsi chilichonse kapena kukamba nkhani za m'nyumba



www.dawateislami.net

kunja, zivute zitani. Chimodzimodzinso, nkhani ya munthu wanzeru yomwe yaperekedwa pansipa ndiyofunika kutsatira.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Aliyense angawulule nkhani za m'banja ndi munthu wotsika mtengo wotsika

Munthu woyera mtima رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: Munthu wosunga chinsinsi anakwatira, koma panali kusamvetsetsana pakati pa mwamuna ndi mkazi. Mwanjira ina mzake anadziwa za momwe zinaliri. Iye anafunsa kuti, "Kodi vuto lanu lam'banja ndi chiyani?" Munthu wosunga chinsinsiyo anati, "Ine sindine munthu wotsika mtengo yemwe amaulula nkhani zake za m'banja." Nthawi inadutsa. Pamapeto pake, analephera kukhazikitsa ubale ndipo anasiyana. Pamene mzake anadziwa, anati, "Iye si mkazi wakonso tsopano, ndiudze vuto linali chiyani." Munthu wanzeruyo anati, "Iye tsopano ndi mkazi amene si-Mahram kwa ine, ndipo sindingathe kukamba za mkazi aliyense amene si-Mahram." *(Gheebat ki tabah kaariyan, tsamba. 363)*

*Allah ham ko fazl say 'aql-e-saleem day*

*Sharm-o-Haya Tufayl-e-Rasool-e-Kareem day*

## Nthawi zina mawu amatuluka pakamwa omwe...

Hazrat Bilal Bin Haris رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُ anafotokoza kuti Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Anati munthu amayankhula mawu osonyeza kufuna chisangalalo cha Allah Wamphamvu zonse koma samadziwa kuti adzapeza chisangalalo chachikulu. Komabe, chifukwa cha zimenezi, Allah



www.dawateislami.net

Wamphamvu zonse amalemba kuvomereza (kutanthauza chisangalalo) mpaka Tsiku Lachiweruzo. Ndipo iye amayankhula mawu osamukondweretsa Allah koma samadziwa kuti padzakhala kusakondwa kwakukulu. Komabe, Allah Wamphamvu zonse amamulembera kusakondwa Kwake mpaka Tsiku Lachiweruzo. *(Tirmizi, buku. 4, tsamba. 143, Hadith 2326)*

## Iye adzachepetsa kuyankhula mkambirano opanda pake

Aliyense amene ali ndi mantha a Allah Wamphamvu yonse, amakumbukira kwambiri imfa, amakhala woyamika ngakhale pa ndalama zochepa, alibe dyera la chuma chambiri, komanso amazimva kuti 'kuyankhula' ndi ntchito yomwe ayenera kudzayankha, ndiyeno munthu wotere sangathe kuyankhula zopanda pake mpaka kale. Monga momwe Sayyiduna Umar Bin Abdul Aziz رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananenera kuti, "Aliyense amene amakumbukira kwambiri imfa, amakhala wokhutira (ndi tsogolo) lokhudza chinthu chosakwanira chotengedwa kudziko lapansi, komanso amakutenga kukambirana kwake ngati ntchito, motero amachepetsa kuyankhula mopanda pake." *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 137; Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 338)*

## Kutelereka kwa lilime ndi koopsa kuposa kutelereka kwa phazi

Pamene akuyankhula nthawi zonse, pamakhalanso mantha kuti ikhoza kukhala nthawi yolandiridwa (mapemphero) ndipo ngati chiganizo chilichonse chosavomerezeka chituluka (pakamwa), chikhoza kukhala momwe chilili. Kumasulira kwa timavesi ta ndakatulo yachiarabu kulil motere: "Munthu amawonongedwa ndi kuterereka kwa lilime lake;



www.dawateislami.net

mosiyana, iye samamwalira chifukwa cha kutetereka kwa phazi. Musalole ngakhale lilime lanu kunena chilichonse chosakondedwa. Nthawi zina, chilichonse chotuluka pakamwa chimachitikadi momwe chilili."

*(Tanbeeh Al-Ghafileen, buku. 116)*

## Ndani amadziwa nthawi ya kuyankhidwa?

O omukonda Rasool! Kupewa kuyankhula zambiri zosafunikira kumabweretsa madalitso. Nthawi iliyonse mukakhala ndi mpata, bweretsani Zikr ndi Durood pa lilime lanu nthawi yomweyo. Ndani akudziwa nthawi yomwe imalandiridwa mapemphero imabwera ndipo titha kutuluka m'mavuto athu. Hazrat Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anamuuza mwana wake kuti: "O mwana wanga! Udzikhala ukunena mawu oti 'اَللّٰهُمَّ اغْفِرْلِىْ', chifukwa pali nthawi zina zochokera kwa Allah Wamphamvu zonse mu nthawi zimenezi pemphero la aliyense amene wapempha limalandiridwa." *(Kitaab Husn-uz-zan billah ma' Mausu'ah Ibn-e-Abi Al-Dunya, buku. 1, tsamba. 110, mawu nambala. 118)*

## Mavuto pa malo okwana asanu pa Tsiku la Chiweruzo kwa munthu amene amayankhula zopanda pake

Zanenedwa kuti munthu adzadzudzulidwa ndikuletsedwa kupereka kufotokozera kulikonse m'malo asanu (ku Bwalo Chiukiriro) pa mtundu uliwonse wonyoza kapena chiganizo chilichonse chopanda pake:

1. Chifukwa chiyani munanena izi? Kodi zinali zothandiza kwa inu?
2. Kodi munapeza phindu lililonse pa zimene munazinenazo?

3. Kodi mukanakhala kuti simunanena zimenezo, kukanakhala kuti mukanataika chilichonse?

4. Chifukwa chiyani simunakhala chete kuti mukhale otetezeka ku zotsatira zake?

5. Chifukwa chiyani simunapeze malipiro ponena kuti "سُبْحٰنَ اللّٰه اَلْحَمْدُ لِلّٰه" m'malo mwa zimenezo? *(Qoot Al-Quloob, buku. 1, tsamba. 428)*

Hazrat Fuzail Bin 'Iyaz رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Mutu umatetezedwa ndi lilime." *(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 190)*

Aliyense amene wadzudzudzidwa akhoza kulowa mundewu mokwiya ndikumenya mutu, ndi zina zotero.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kukhala chete kuli ndi ubwino 7

Munthu wina wanzeru ananena kuti kukhala chete kuli ndi ubwino wokwana zikwi zisanu ndi ziwiri (7000) zomwe zasonkhanitsidwa m'ziganizo zisanu ndi ziwiri, ndipo chiganizo chilichonse chili ndi ubwino chikwi chimodzi:

1. Kukhala chete ndi kulambira kopanda zovuta (ndi malamulo ena).

2. Kukhala chete ndi kukongola kopanda zokongoletsera.

3. Kukhala chete ndi ulemu wopanda ufumu.

4. Kukhala chete ndi linga lopanda makoma.



www.dawateislami.net

5. Mu kukhala chete, munthu samayenera kupepesa kwa wina.

6. Kukhala chete kumakhala chitonthozo kwa Kiraman Katibeen (angelo olemba ntchito).

7. Kukhala chete ndi chotchinjira cha zolakwa za munthu.

*(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 118)*

## Chinyamata ndi nthawi ya misala; pewani zoyipa zake

Thanzi pa nthawi ya unyamata nthawi zambiri limakhalabe labwino. Zilakolako zimakhala zambiri, ndipo ndithudi mayesero amakhala ovuta pa nthawi ya unyamata. Zikunenedwa kuchokera kwa Hazrat Hasan Basri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه kuti Sayyiduna Umar Farooq-e-A'zam رَضِىَ اللّٰهُ عَنْهُ anamuuza mnyamata wina kuti: "E mnyamata! Ngati utapewa zoipa za zinthu zitatu, udzatetezedwa ku zoipa za unyamata:

1. Zoipa za lilime.

2. Zoipa za ziwalo zobisika.

3. Zoipa za m'mimba."

*(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 117)*

*Dhalnay wali hai jawani jis pay tujh ko naaz hay*

*Tu baja lay chahay jitna char din ka saaz hay*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب!          صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kukhala chete kuli ndi ubwino 9

Ndithudi, mtendere ndi chitetezo zili mu kuyankhula pang'ono. Hazrat Wuhaib Bin Ward رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ anati, "Mtendere uli ndi magawo 10; zisanu ndi zinayi mwa izo zimachokera ku kukhala chete ndipo chimodzi chimachokera ku kuthawa kuchokera kwa anthu." *(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 190)*

## Tetezani lilime ngati golide ndi siliva

Sayyiduna Abdullah Bin 'Amr Bin 'Aas رَضِیَ اللہُ عَنۡہُمَا anati, "Siyani ntchito iliyonse yosathandiza, pewani zokambirana zopanda pake, ndipo tetezani lilime lanu ngati mukuteteza golide ndi siliva."

*(Allah walon ki baatayn, buku. 1, tsamba. 508; Hilyat Al-Awliya, buku. 1, tsamba. 359)*

## Kukhala chete ndi golide

M'neneri Wokondedwa wa Allah Sayyiduna Sulaiman عَلَیۡہِ السَّلَام anati: "Ngati kuyankhula ndi siliva, ndiye kuti kukhala chete ndi golide." *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 136)*

## Munthu wanzeru ndindani?

Mtumiki Woyera صَلَّی اللہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, "Mukamuwona munthu wodzipatula kuchokera ku dziko lapansi ndikumupeza akuyankhula pang'ono, khalani naye chifukwa ndi wodala ndi nzeru." *(Ibn-e-Majah, buku. 4, tsamba. 422, Hadith, 4101)*

Zafotokozedwa mu Mir'aat zokhudzana ndi Hadith yodalitsikayi: "Nzeru zikutanthauza kugwiritsa ntchito maphunziro. Ena (anthu ophunzira)



www.dawateislami.net

anati: Kuphatikiza kwa Shari'ah ndi Tariqah ndi nzeru." *(Mir'aat, buku. 7, tsamba. 57)*

## Kuyankhula pang'ono, ntchito yambiri

Munthu wochita zabwino samasiya Zikr, Durood, ndi ntchito yoyitanira anthu ku kuchita zabwino, motero sangathe kugwera mu mkamano opanda pake; mbali inayi, munthu wachinyengo ndi wopanda ntchito. Ngati salowa mu mkambirano opanda pake, ndi chiyani chinanso chomwe angachite? Monga ndi mawu otchuka a Imam Auzai رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه onena kuti, "Msilamu amayankhula pang'ono ndipo amagwira ntchito kwambiri, koma wachinyengo amagwira ntchito zochepa ndipo amayankhula kwambiri (zopanda pake)." *(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 115)*

## Kuzitalikitsa kuchokera ku kuyankhula zopanda pake m'mausiku a zaka 40

Pali akapolo a Allah Wamphamvu zonse ndi anthu omutsatira Rasool صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amene amakhala otanganidwa kwambiri ndi Zikr ndi Durood moti sangathe kulowa mu mkambirano opanda pake. Hazrat Mansur Bin Mu'tamir رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه sanatenge nawo mbali pa zokambirana ndi aliyense pambuyo pa 'Isha Salah kwa zaka makumi anayi. *(Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 339; Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 137)*

اَللهُ اَكْبَر! Okondedwa abale achisilamu! Akapolo a Allah Wamphamvu zonse anakwanitsa kulamulira (kuteteza) malilime awo kwa zaka makumi anayi,

ndipo vulo lathu ndilakuti sitingathe kuteteza malilime athu ngakhale kwa mphindi makumi anayi.

*Baykar guftugu say Khudaya bacha mujhay*

*Zikr-o-Durood-e-Pak ka shayda bana mujhay*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Ngakhale liwu lotukwana litha kukakulowetsa ku Gahena

Nthawi zina Msilamu amayankhula chinthu chabwino mwangozi chomwe samachidziwa ndipo Allah Wamphamvu zonse amakondwera naye. Ndipo wina amayankhula chinthu mosasamala chomwe samachidziwa ngakhale chiwonongeko chimakhala tsogolo lake chifukwa cha kuipa kwa zopanda pakezo. Sayyiduna Abu Hurairah رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anafotokoza kuti Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Ndithu, nthawi zina kapolo amayankhula chiganizo chokondweretsa Allah Wamphamvu zonse chomwe samachidziwa, ndipo chifukwa cha ichi, Allah Wamphamvu zonse amamukweza mu ulemero wake kwambiri. Ndipo nthawi zina, kapolo amayankhula chiganizo chosamvera Allah Wamphamvu zonse chomwe samachidziwa, ndipo chifukwa cha ichi, amapitiriza kugwera ku Gahena." *(Mishkaat, buku. 2, tsamba. 189, Hadith, 4813)*

## Abwenzi oyipa anandiwononga ine

O omukonda Rasool! Hadith yodalitsika yodzutsa mtima yatchulidwa. Ndithudi, lilime liyenera kugwiritsidwa ntchito mosamala kwambiri. Kuti pakhale maganizo oteteza lilime, udindo wa Dawat-e-Islami ndi wofunika kwambiri. Pokhala ogwirizana ndi malo a zochitika za chipembedzo a



www.dawateislami.net

Dawat-e-Islami, tiyenera kuchita ntchito zachipembedzo mochuluka ndikukhala kutali ndi abwenzi oyipa nthawi zonse. Mvetserani nkhani yozizwitsa ya Madani ya m'bale wachisilamu wodala, yemwe atawonongedwa ndi abwenzi oyipa, anapeza mwayi wopeza abwenzi odala omukonda Rasool. M'bale wina wachisilamu wochokera ku Karachi, Gulistan-e-Johar, anakodwa dambo la makhalidwe oipa ndi machimo chifukwa cha abwenzi oipa. Anali wokonda kwambiri kumvetsera nyimbo, ndipo chikondi chimenechi chinakula kufika poti iye mwini anayamba kuyimba m'mapulogalamu osiyanasiyana ndipo amkalandira ulemu kuchokera kwa anthu. Kuwonjezera pamenepo, kugwiritsa ntchito chamba chinali chizolowezi chake. Chizolowezi chake cha machimo chinakula kwambiri moti kuyankhula zonyansa ndi kunama sizinali machimo pamaso pake. Mwamwayi, mu 2005, anapeza mwayi wopezeka pa msonkhano wa masiku atatu wa Dawat-e-Islami wolimbitsa Sunnah womwe unachitikira ku Madina-tul-Awliya, Multan, komwe anakhala wotsatira wa Ghaus Pak رَحۡمَةُ اللّٰہِ عَلَیۡه. Komabe, atabwerako ku msonkhano wachipembedzo, adabwereranso kwa abwenzi oipa ndipo anapitiriza kuchita machimo. Tsiku lina, mwadzidzidzi, anadwala matenda amisala, chifukwa cha zimenezi samkakumbukira ngakhale Surah Fatihah ndipo anayamba kukhala m'nyumba mwake ngati anthu amisala. Iye anayamba kuwaona makolo ake ngati adani ake. Matenda ake anaipiraipira kwambiri moti samkadya kapena kugona chifukwa cha matenda ake. Pamapeto pake, adagonekedwa kuchipatala cha matenda amisala. Amayi ake sakanatha kumuona mwana wawo ali chonchi, ndipo anapitiriza kumupempherera ndikuwerenga mapemphero mochuluka. Usiku wina, amayi ake anawona munthu woyera mtima m'maloto ake momwe anamupempha kuti azichita 'Amal [ntchito] ina. Amayi ake anayamba kuchita 'Amal imeneyo tsiku ndi tsiku. Chifukwa cha madalitso a 'Amal imeneyo, matenda a m'bale wachisilamu anayamba



www.dawateislami.net

kusintha pang'onopang'ono, ndipo anayamba kuchira m'thupi mwake. Ndipo اَلْحَمْدُ لِلّٰه tsiku lina anapita ndi Madani Qafilah ya Dawat-e-Islami kuti akaphunzire ndi kuphunzitsa Sunnah, kumene anakapeza maganizo opewa machimo pokhala ndi gulu la anthu omukonda Rasool, ndipo anakhazikika m'malo achipembedzo, ndipo pamene ankachita nawo ntchito zachipembedzo za Dawat-e-Islami, anakhala Zimmadar (woimira) wa Madani Inaa'mat (zomwe tsopano zimatchedwa 'Nayk A'maal' kutanthauza ntchito zabwino) pa Division level.

O anthu okonda masahaba komanso Ahl-e-Bayt! Nkhani yomwe yatchulidwa pamwambapa ikutikumbutsa kuti tiganizire za anzathu ndi ubwenzi wathu. N'kutheka kuti chifukwa cholephera kuchita zabwino ndi ubwenzi wathu oipa komanso abwenzi oipa. Hazrat Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Sizingatheke kuti kucheza ndi anthu oipa kubweretse phindu, ndipo kucheza ndi anthu abwino kubweretse kuluza. Simudzapeza Musk kwa msula zitsulo koma kutentha ndi utsi wokha. Simudzapeza kutentha kapena utsi kuchokera kwa yemwe ali ndi Musk koma Musk kapena zonunkhira zokha." Iye ananenanso kuti, "Pewani kucheza ndi anthu oipa momwe mungathere, chifukha kumawononga Deen ndi dziko; ndipo khalani ndi abwenzi abwino, chifukwa kumasunga chipembedzo ndi dziko. Kucheza ndi njoka kumatenga moyo. Kucheza ndi bwenzi loipa kumawononga Chikhulupiriro." *(Mir`aat, buku. 6, tsamba. 591)*

Hazrat Maulana Rum رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati:

صُحبتِ صالِح تُرا صالِح كُنَد        صُحبتِ طالِح تُرا طالِح كُنَد



www.dawateislami.net

*Kucheza ndi munthu wabwino kudzakupangitsani kukhala wabwino, ndipo kucheza ndi munthu woipa kudzakupangitsani kukhala woipa*

(Musnawi, Daftar awwal, tsamba. 22)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Malangizo kuti upewe mfundo zosafunikira mu mkambirano

Amene akufuna kuchepetsa zokambirana zawo ndikupewa mfundo zosafunikira komanso zoipa zosiyanasiyana, umu ndi mmene zafotokozedwera mu '*Ihya-ul-'Uloom*': "Mkambirano uli mitundu inayi:

1. Mkambirano ovulaza kwambiri
2. Mkambirano othandiza kwambiri
3. Mkambirano umene uli ovulaza komanso othandiza, komanso
4. Mkambirano omwe siuli ovulaza kapena othandiza

Choncho, n'kofunikira nthawi zonse kupewa mtundu woyamba wa mkambirano omwe uli ovulaza kwambiri. Chimodzimodzinso, n'kofunikiranso kupewa mtundu wachitatu wa mkambirano omwe uli ovulaza komanso othandizanso, ndipo mtundu wachinayi umaphatikizidwa mu gulu la 'Zopanda pake' zomwe sizivulaza kapena kuthandiza. Choncho, kuwononga nthawi pa zokambirana zoterewu ndi mtundu wina wa kuluza. Zitatha zonsezi, mtundu wachiwiri unatsala wokha wa mkambirano. Zikutanthauza kuti ¾, kutanthauza 75%, ya mkambirano si zothandiza, ndipo ndi mtundu wachiwiri wokha umene uli wopindulitsa ndi wothandiza. Komabe, mu mtundu uwu wa zokambirana zothandiza, pali mantha ochepa a kudzionetsera, kuchita

zinthu mopupuluma, miseche, kunyozana, kulingalira zongopeka, kudzitamandira kutanthauza kuti kufotokoza ubwino ndi chiyero cha munthu, ndi zina zotero. Komanso, pali mantha a kuyamba zokambirana zopanda pake pamene mukuchita zokambirana zothandiza ndipo Allah Aletse, pamene mukupitirira ndi izi, munthu akhoza kuchita machimo, ndi zina zotero pa nkhaniyi. Kuwonjezereka kwa zoipa zonsezi ndi kochepa kwambiri moti munthu nthawi zambiri samazindikira. Choncho, munthu nthawi zonse amakhala pachiwopsezo ngakhale pa zokambirana zothandiza. *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 138)*

## Ngati munthu akuchita mkambirano wa m'dziko lapansi, pangani ma Zikr a Allah Wamphamvu zonse

Akapolo a Allah Wamphamvu zonse Samkakutenga kukambirana nkhani zapadziko lapansi (zokhala ndi cholinga) ngati kwabwino. Pamene Sayyiduna Hammad Bin Salamah رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه amkapanga mkambirano okhudza za dziko lapansi, pambuyo pake amkawerenga. "سُبۡحٰنَ اللّٰهِ وَالۡحَمۡدُ لِلّٰهِ وَلَآ اِلٰهَ اِلَّا اللّٰهُ وَاللّٰهُ اَکۡبَرۡ" ndipo amati, "Anthu athu akale (amuna ochita zabwino a Allah) sankalola kukambirana nkhani zapadziko lapansi mu Majlis iliyonse pokhapokha ngati aphatikizapo nkhani yachipembedzo mkati mwake." *(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 190)*

## Pamene chifundo chachotsedwa

Munthu woyankhula kwambiri ayenera kuopa ngati Allah Wamphamvu zonse wachotsa chifundo chake pa iye. Sayyiduna Sheikh Ma'roof Karkhi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Kuchita kwa munthu kukambirana zopanda pake kumayamba pamene Allah Wamphamvu zonse wamusiya wosathandizidwa." *(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 190)*



www.dawateislami.net

## Kusowekera makhalidwe abwino komanso kumvetsetsa Deen

Ngakhale wachinyengo atakhala ndi wanzeru bwanji pa nkhani za dziko lapansi, popeza alibe makhalidwe abwino komanso kumvetsetsa Deen, ndiye kuti iye ndi wopanda mwayi komanso wosauka. Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananena kuti, "Wachinyengo sangakhale ndi makhalidwe awiriyi nthawi imodzi:

1. Makhalidwe abwino.
2. Kumvetsetsa Deen."

*(Tirmizi, buku. 4, tsamba. 313, Hadith, 2693)*

## Woyankhula nthawi zambiri amanong'oneza bondo

Kutanthauzira kwa ndakatulo yochenjeza yachiarabu ili motere: "Maphunziro ndi kukongola, ndipo kukhala chete ndi mtendere, ndipo nthawi zonse pamene uyenera kuyankhula, usayankhule zambiri. Mwina sunanyozekeko chifukwa chokhala chete, koma uyenera kuti unanong'onezapo bondo komanso kunyozeka nthawi zambiri pambuyo poyankhula." *(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 116)*

Okondedwa abale achisilamu! Ndizowona kuti kukhala chete kumakhala ndi mwayi wochepa wochititsidwa manyazi. Kumbali ina, chifukwa cha chizolowezi choyankhula molakwika, munthu amayenera kupepesa nthawi zambiri kapena kunong'oneza bondo mumtima mwake, kwinaku akuganiza kuti, "Zikanakhala bwino ndikanakhala chete; chifukwa nditayankhula, kukayikira kwa munthu wina kunachotsedwa. Ndinadzudzulidwa, munthu wakuti-wakuti anakwiya, wakuti-wakuti anamva kuwawa, wakuti-wakuti anavulazidwa, malingaliro anga anawonongekanso, ndi zina zotero." Sayyiduna Muhammad Bin Nazr Harisi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anapereka uphungu wabwino kwambiri: "Munthu



www.dawateislami.net

amapitiriza kuluza ulemu chifukwa choyankhula mopitirira muyeso” *(Al-Samt ma’ Mausu’ah Ibn-e-Abi Al-Dunya, buku. 7, tsamba. 60, mawu nambala. 52)*

## Kunong’oneza bondo chifukwa siunayankhule ndi kwabwino kuposa utayankhula

Zowonadi, ‘Kunong'oneza bondo chifukwa chosayankhula ndi bwino kuposa kunong'oneza bondo mutayankhula’ ndipo ‘Kunong'oneza bondo mutadya kwambiri ndi bwino kuposa kunong'oneza bondo mutadya pang’ono’, chifukwa aliyense amene amangoyankhula amapitiriza kukumana ndi mavuto, ndipo amene amadya kwambiri amawononga mimba yake, nthawi zambiri amakhala wonenepa kwambiri ndipo amadwala matenda osiyanasiyana. Ngakhale atakhala wotetezeka ku matendawa mpaka pamlingo winawake ali wamnyamata, amakhala ‘wodwala matenda’ unyamata wake ukatha. Kuti mudziwe za kuipa kwa kudya mopitirira muyeso komanso machiritso a kunenepa kwambiri, werengani ‘*Ubwino wa Njala*’, limodzi mwa mitu ya buku loyamba la *Faizan-e-Sunnat*.

## Munthu woyankhulitsa kwambiri amachititsidwa manyazi

Abwenzi oyipa amawononga. Aliyense wopita kumalo oyipa amanyozeka, ndipo munthu wokonda kuyankhula amanyozeka. Zafotokozedwa zokhudza Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه kuti anamuuza mwana wake: “E mwanawe!

1. Aliyense amene amacheza ndi munthu woipa ndipo amakhala mnzake samalandira mtendere; ndiponso

2. Aliyense wopita kumalo oyipa amanyozeka; ndiponso



www.dawateislami.net

3. Aliyense amene sateteza lilime lake amachititsidwa manyazi."

*(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 115)*

## Aliyense amene amaganizira kaye asanayankhule amazitalikitsa kuchokera ku mkambirano opanda pake

Makhalidwe abwino kwambiri a munthu wanzeru ndi akuti ayenera kuganiza asanayankhule, asataye nthawi yake ndipo ayenera kupereka chidwi choyenera ku nkhani yake; choncho, iye sadzapeza mpata wochita zokambirana zopanda pake. Sayyiduna Abu Zar Ghifari رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anafotokoza kuti iye anamufunsa Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰہُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم modzichepetsa za mitu yomwe inali m'Mapepala a Ibrahimi (kutanthauza mabuku omwe adavumbulutsidwa kwa Sayyiduna Ibrahim عَلَيْهِ السَّلَام). Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰہُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayankha kuti, "Iwo anali ndi machenjezo ndi malangizo, (zomwe zinaphatikizapo kuti) ndi zoyenera kwa munthu wanzeru kuti azidziwa zinthu zomwe zikuchitika mu nthawi yake ndikuteteza lilime lake. Iye ayenera kuchita zinthu m'malo moyankhula, ndipo zokambirana zake zisakhale ndi zokambirana zopanda pake." *(Allah walon ki baatayn, buku. 1, tsamba. 319; Hilyat Al-Awliya, buku. 1, tsamba. 222)*

## Wodwala khansa anachira

اَلْحَمْدُ لِلّٰه! Madalitso a malo a zochitika za chipembedzo a Dawat-e-Islami ndi odabwitsa. Kuti mumvetsetse madalitsowa, mvetserani 'nkhani ya Madani' ndipo sangalalani. M'bale wina wachisilamu wochokera ku Old Kanpur (Al Hind) anali ndi mwayi wopezeka m'malo a zochitika za chipembedzo a Dawat-e-Islami. Agogo ake aakazi anali kudwala kwambiri; analandira chithandizo chambiri koma sanasonyeze kuchira. Madokotala ananena kuti anali kudwala khansa. Kuwonjezera pamenepo,

iwo ananena kuti anali atatsala ndi masiku owerengeka. Iye anadzidzimuka ndi nkhani yoopsayi. Kuti apemphe Du'a kuti agogo ake akazi achire, ndi kudalira mwa Allah Wamphamvu zonse, iye anatenga nawo mbali pa msonkhano wa pasabata wa Dawat-e-Islami wolimbikitsa Sunnah ndipo anapanga Du'a mopempha kuti, "O Allah Wamphamvu zonse! Adalitseni agogo anga aakazi okondedwa ndi kuchira kudzera mu kupambana kwa munthu amene ali okondedwa kwa inu pano." Tsiku lotsatira, pamene anapita kukawaona agogo ake aakazi, iye anali okhutira kwambiri poona kuti madalitso a Du'a opangidwa pamsonkhano wachipembedzo pakati pa anthu omukonda Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anawonekera m'njira yoti agogo ake aakazi sanali kungokhala pansi basi komanso anali athanzi ndiponso amayenda.

*Tayra shukr Maula diya madani mahol*

*Nah chotay kabhi bhi Khuda madani mahol*

*Salaamat rahay Ya Khuda madani mahol*

*Bachay bad nazar say sada madani mahol*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 647)*

## Palibe matenda osachiritsika

Ulemerero ukhale kwa Allah! Iye ali ndi mphamvu pa chilichonse. Ngati Iye akufuna, khansa imachiritsidwanso. Ndithudi, pali machiritso a matenda aliwonse kupatula ukalamba ndi imfa. Komabe, ndi mutu wosiyana kuti madokotala sanapezebe mankhwala a matenda angapo. Choncho, ndi bwino kunena kuti, "Tilibe mankhwala a matendawa kapena madokotala sanapeze mankhwalawo" m'malo monena kuti, "matenda amenewa sangachiritsidwe". Komabe, ngati Allah Wamphamvu zonse akufuna, mankhwala amakhala gwero la machiritso;



www.dawateislami.net

apo ayi, n'kutheka kuti mankhwala omwewo amakhala chifukwa cha imfa. Komanso, zimawonekanso kuti ngakhale madokotala atapereka mankhwala olondola, odwala ena amavutika ndi zotsatira zake zoyipa.

## Machiritso auzimu a khansa

Mutawerenga Durood-e-Ibrahim kakhumi ndi kamodzi (11) musanawerenge komanso mutamaliza kuwerenga 'Surah Maryam', pepelerani m'madzi. Muzingowonjezera madzi ngati pali kufunikira. Odwalawo azimwa madzi amenewo tsiku lonse. Muzichita zimenezi tsiku lililonse kwa masiku makumi anayi. اِنْ شَآءَاللّٰه, wodwalayo adzachira. (Munthu wina akhozanso kuwerenga, kupepelera, ndi kumwetsa wodwalayo madzi.)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Munthu wopusa samadziwika ngati atakhala chete

Nthawi zina kukhala chete kumawadabwitsa anthu. Amakuyang'anani mwaulemu. Ngati wina aliyense amayankhula nthawi zonse, ulemu wake umawonongeka, ndipo maganizo ake amakhala 'opanda phindu. Ibrahim Nakha'i رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه Anati, "Ngati wina aliyense amaganizira, adzapeza aliyense amene nthawi zambiri amakhala chete ngati wofewa ndi wolemekezeka kwambiri kuposa onse amene amapezekapo pamsonkhano wachipembedzo, chifukwa kukhala chete ndi kukongola kwa wophunzira ndi chivundikiro kwa munthu wosadziwa."

*(Tanbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 190)*



www.dawateislami.net

## Nanga bwanji dzuwa litapanda kulowa mpaka pakati pa usiku? (Nkhani)

O omukonda Rasool! Ndithudi, ulemu umakhalabe wokhazikika pokhala chete. Munthu akayamba kuyankhula, nzeru zake zimawonekera. Zikufotokozedwa kuti munthu wina amkakonda kukhala ndi Sayyiduna Imam Abu Yusuf رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه komano samkayankhula. Sayyiduna Imam Yusuf رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه tsiku lina anamufunsa kuti, “Bwanji simufunsapo funso lililonse? Mumakhala chete nthawi zonse.” Atamva zimenezi, iye anafunsa, “Chabwino ndiwuzeni, kodi Iftar iyenera kuchitika nthawi yanji?” Imam wolemekezekayo anayankha kuti, “Dzuwa likamalowa.” Iye anafunsa, “Nanga bwanji ngati dzuwa litapanda kulowa mpakana pakati pa usiku?” Atamva funso limeneli, Sayyiduna Imam Abu Yusuf رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه Anaseka ndipo anati, “Kukhala kwanu chete kunali bwino. Ine ndinalakwitsa kukupangitsani kuyankhula.” *(Tareekh-e-Baghdad, buku. 14, tsamba. 251)*

## Ndimalakalaka ndikanakhala wosayankhula

O omukonda Rasool! Ngati titayang'ana, munthu wakhungu amakhala ndi ubwino woti amatetezeka ku machimo monga kuonerera mafilimu ndi masewero, kuyang'ana akazi osakhala *mahram*, mawondo ndi ntchafu za munthu wovala zazifupi zosaoneka bwino, komanso kuyang'ana anyamata okongola ndi chilakolako cha thupi, ndi zina zotero. Chimodzimodzinso, munthu wosalankhula amatetezekanso ku zoyipa zambiri zomwe zimachitika pakamwa. Khalifah woyamba wa Asilamu, womukonda kwambiri Mtumiki, Sayyiduna Siddiq Akbar رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ ananena (modzichepetsa) kuti: “Ndikulakalaka ndikanakhala wosalan

khula ndipo ndikanakhala ndi mphamvu yokha yopangira Zikr ya Allah Wamphamvu Zonse.” *(Mirqaat Al-Mafatih, buku. 10, tsamba. 87)*

## Ndimalakalaka iye akanakhala wosayankhula

Zafotokozedwa mu ‘*Ihya-ul-Uloom*: Sahaba wa Mtumiki Woyera, Sayyiduna Abu Darda رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anaona mayi wokonda kulankhula kwambiri, ndipo anati, “Zikanakhala bwino kwa iye akanakhala wosalankhula.” *(Ihya-ul-‘Uloom, buku. 3, tsamba. 142)*

## Momwe nyumba ingakhalire ya mtendere!

Kuchokera ku zoyankhula za Sayyiduna Abu Darda رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ, makamaka alongo achisilamu amene amalephera kupewa kuyankhula zinthu zopanda pake, kufunsa mafunso osafunikira, kukayikira molakwika, ndi miseche ayenera kuphunzira phunziro. Ngati alongo achisilamu aphunzira momwe angakhalire chete, mavuto awo apakhomo, mikangano ndi achibale, kukangana ndi apongozi, ndi mavuto ena ambiri adzatha, ndipo nyumba yonse idzakhala yamtendere, chifukwa mavuto ambiri apakhomo amayamba chifukwa chogwiritsa ntchito molakwika lilime.

## Nkhani yodziwika ya pa tsamba la mchezo

Nkhani yodziwika bwino yapa tsamba la mchezo ikuperekedwa pano ndi kusintha pang'ono. Mtsikana wina analemba kuti: Ngati ana aakazi akanakhala ndi ufulu wokhala ndi makolo awo akakwatiwa, sipakanakhala "nyumba ya anthu okalamba" iliyonse m'dzikoli. Pa izi, mnyamata wina anayankha mwanzeru kuti ngati ana aakazi amenewo akanati aziwatenga apongozi awo aamuna ndi aakazi ngati makolo awo, sipakanakhala

nyumba iliyonse ya anthu okalamba padziko lonse lapansi, osati m'dziko lino lokha.

Munkhaniyi, khama lapangidwa pofuna kusintha akazi okhawo omwe amagwiritsa ntchito lilime lawo polankhula zoyipa za apongozi awo aakazi ndi alongo awo a mwamuna wawo ndikuwononga bata panyumba; apo ayi, m'dera lathu, palinso akazi ambiri omwe amapirira kuzunzidwa ndi achibale awo a mwamuna wawo.

## Njira yothetsera mikangano pakati pa mkazi ndi apongozi

Ngati apongozi aakazi akalipira, mpongozi ayenera kungokhala oleza mtima. Poyankha, asanene mawu aliwonse kapena kudandaula kwa mwamuna wake kapena kukwinyata nkhope kapena kusonyeza mkwiyo pokalipira ana ake kapena kuponya mphika uliwonse kapena kunena chilichonse kunyumba kwa abambo ake. إِنْ شَآءَالله, Mavuto onse apakhomo adzathetsedwa pang'onopang'ono. Chimodzimodzinso, ngati mpongozi akukangana ndi apongozi aakazi, apongozi aakazi sayenera kubwezera ayi, ayenera kungokhala chete, ndipo asadandaule kwa aliyense m'banjamo ngakhale kwa mwana wake. إِنْ شَآءَالله malinga ndi mwambi wa Chiurdu uwu, ‘khala chete, pezani chisangalalo chambiri’, adzapeza mtendere. Inde! Ngati yankho la Sag-e-Madinah likutsatiridwa mokwanira, إِنْ شَآءَالله nkhondo ya pakati pa mpongozi wamkazi ndi apongozi idzatha posachedwa, ndipo nyumba idzakhala ya mtendere.

## Kumuona Mtumiki Woyera ﷺ chifukwa cha m’dalitso okhala chete

Mlongo wina wa Chisilamu anamvetsera kaseti ya ulaliki wolimbikitsa Sunnah yotchedwa 'kufunika kokhala chete' yotulutsidwa ndi Maktaba-



www.dawateislami.net

tul-Madinah ya Dawat-e-Islami ndipo adayamba kukhala chete. Pasanathe masiku atatu, anazindikira kuti amalankhula zopanda pake. اَلْحَمْدُ لِلّٰه chifukwa cha madalitso okhala chete, anayamba kulota maloto abwino. Pa tsiku lachitatu lopewa kukambirana zopanda pake, adamvetsera kaseti ya ulaliki wolimbikitsa Sunnah yotchedwa 'chimene chimatchedwa kumvera' yotulutsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah.

Atagona usiku, اَلْحَمْدُ لِلّٰه anayamba kuona chochitika m'maloto ake chomwe chatchulidwa mu kaseti. Chinali pa malo a nkhondo. Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anatumiza sahaba wake wokondedwa, Sayyiduna Huzaifah رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ, kuti akapange ukazitape pa adani. Atangofika ku mahema a osakhulupirira, iye anapeza mkulu wawo, (Sayyiduna) Abu Sufyan (amene anali asanasandulike kukhala Msilamu panthawiyo). Pofuna kugwiritsa ntchito mwayi, pamene Sayyiduna Huzaifah رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anayika muvi pa uta, anakumbukira mawu awa a Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم akuti, 'Osakhulupirira asadziwe'. Pomumvera Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, anasiya kuponya muvi. Pambuyo pake, anapita pa maso pa Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo anakasiya zomwe anapeza.

اَلْحَمْدُ لِلّٰه m'maloto amenewo, mlongo wachisilamu anakhala ndi mwayi womuona Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi masahaba awiri رَضِیَ اللهُ عَنْهُمَا. Kupatula apo, zochitika zina zonse zinali zosawoneka bwino. اَلْحَمْدُ لِلّٰه kuchokera ku kuyesetsa kwa masiku atatu okha kupewa kukambirana zopanda pake, analandira madalitso akuluakulu a Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Tsopano akunena kuti: "Ndikulakalaka kuti ndikakhala osayankhula mawu aliwonse osafunikira."



www.dawateislami.net

*Allah! Karon mayn nah kabhi falto baatayn*

*Bas zikr mayn guzrayn mayray din aur mayri raatayn*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Zoyipa za lilime ndi zazikulu

Sahaba wa Mtumiki Woyera, Sayyiduna Abdullah Ibn-e-Mas'ood رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anati: "Ndikofunikira kulamulira lilime kuposa zinthu zina zonse *(Mu'jim Kabeer, buku. 9, tsamba. 149)* (chifukwa zoyipa za lilime ndi zambiri). Lilime ndi loopsa kwambiri pa ziwalo zonse za thupi pomuchulukitsira machimo munthu. M'pofunika kusunga ziwalo zonse za thupi kuti zisachite machimo, (koma poyerekeza ndi ziwalo zina za thupi,) n'kofunika kwambiri kusamalira lilime ndi kulilamulira.

## Umar Bin Abdul Aziz رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ anagwetsa misozi

Sayyiduna Abu Abdullah رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ ananena kuti anamva kuti wophunzira kuti iye anamva kuti wophunzira wina anayamba kunena pamaso pa Sayyiduna Umar Bin Abdul Aziz رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ kuti, "Wophunzira wosayankhula ali ngati wophunzira woyankhula." Iye anati, "Malingaliro anga ndi akuti wophunzira woyankhula adzakhala wabwino kuposa wophunzira wosayankhula pa Tsiku Lachiweruzo, chifukwa ubwino wa wophunzira wolankhula udzafika kwa anthu; komano, wophunzira wosayankhula adzangopeza ubwino wake yekha." Wophunzira anati, "O Ameer-ul-Momineen! Kodi simukudziwa za kuyipa kwa kuyankhula?" Atamva izi, Sayyiduna Umar Bin Abdul Aziz رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ anayamba kulira.

*(Al-Samt, buku. 7, tsamba. 345, mawu nambala. 648)*



www.dawateislami.net

Allah Wamphamvu zonse amuchitire chifundo ndipo atikhululukire popanda chiwerengero kudzera mu ubwino wake!

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

## Kufotokozera nkhani

O omukonda Rasool! Kusamala ndi chidwi cha anthu athu akale oyera pankhani yoopa Allah Wamphamvu zonse kunali kwakukulu! Komabe, palibe kukayika kuti ntchito yosamala ya akatswiri wophunzira achisilamu yopereka malangizo, kufotokoza malamulo a Shar'i, ntchito ya alaliki yopereka ulaliki olimbikitsa Sunnah ndi kuyitanira ku chilungamo ndi ntchito zabwino kwambiri poyerekeza ndi kukhala chete. Komabe, mchitidwe wa katswiri wophunzira za chipembedzo womufunsa Sayyiduna Umar Bin Abdul Aziz رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه kuti'Kodi simukudziwa za zoyipa za kuyankhula?' Kuti amuchenjeze zinali zolondola pa malo ake, ndipo Ameer-ul-Momineen's رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه kulira kwake chifukwa choopa Allah Wamphamvu Zonse kunali chifukwa chakuti anazindikira mozama mawu a katswiri wophunzira wachisilamuyo. Ndithudi, ngakhale kuyankhula ndi cholinga kumathandiza anthu, komabe pali zoopsa zambiri kwa woyankhulayo. Mwachitsanzo: Ngati mlaliki ali wabwino, akhoza kugwa mu zoyipa zoyankhula mawu okoma ndi miyambi, ndi zina zotero chifukwa cha kuyamikiridwa kumene akulandira kuchokera kwa ena chifukwa cha njira yake yabwino yofotokozera komanso kuyankhula bwino, kapena chifukwa chongodzikuza ndi luso lake kapena chifukwa chodziona kuti ndi wapamwamba ndipo ena ali otsika kapena chifukwa chongonyada chifukwa cholandira kuyamikiridwa chifukwa choyankhula miyambi yovuta. Ngati ali ndi luso m'chinenero cha Chiarabu, ndiye kuti pofuna kukopa ena ndi chinenero chake cha Chiarabu panthawi yoyankhula ndi kukambirana, akhoza kugwa mu choyipa chogwiritsa



www.dawateislami.net

ntchito miyambi yambiri ya Chiarabu, ndi zina zotero. Chimodzimo dzinso, aliyense amene ali ndi mawu okongola, amakumana ndi zoopsa. Chimodzimodzinso, aliyense amene ali ndi mawu okoma, amakumana ndi zoopsa. Nthawi zonse pamakhala mantha olakwitsa, ndi zina zotero chifukwa anthu nthawi zambiri amayamikira anthu oterowo amene amanyadira, kugwa m'kudzikuza, ndipo amaganizira mawu abwino ngati luso lawo m'malo mowatenga kuti ndi opatsidwa ndi Allah Wamphamvu Zonse. Choncho, chenjezo la akatswiri wophunzira achisilamu amenewo lonena za 'kuyankhula' ndi lolondola, ndipo ndithudi, mlaliki amene ali ndi makhalidwe oyipa, kuyankhula kwake ndi mayesero aakulu mwa iye ndiponso gwero la chiwonongeko cha moyo wake wa pambuyo pake, ngakhale anthu atapindula kuchokera kwa iye.

## Tsatirani njira zosiyanasiyana zoyankhulira kuti mulimbikitse

Kupanga zokambirana ndi cholinga chokopa anthu ndipo motero kuwapanga kukhala okukondani ndi chinthu chonyansa. Anthu amene ngakhale amawoneka ngati oyera koma nthawi zonse 'amadzitamandira' okha ndipo amayesa kukopa ena ndi umunthu wawo ayenera kuphunzira phunziro kuchokera ku Hadith yodalitsikayi.

Sayyiduna Abu Hurairah رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anafotokoza kuti Mtumiki Woyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, "Aliyense amene amaphunzira njira zosiyanasiyana zokambirana ndi cholinga chongotsekera mitima ya anthu (kutanthauza kuti, kuwapanga anthu kukhala otsatira ake), pa Tsiku Lachiweruzo, Allah Wamphamvu Zonse sadzalandira Fard yake kapena Nafl yake."

Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ anafotokoza mogwirizana ndi Hadith yodalitsikayi: "Kufotokoza mutu pogwiritsa ntchito mafotokozedwe osiyanasiyana, kuyankhula ziganizo zabwino, kusandutsa bodza kukhala



www.dawateislami.net

choonadi, zomwe zikutanthauza kuti katswiri wophunzira amayankhula nthawi yayitali ndipo amapereka ulaliki wosangalatsa ndi cholinga chongokopa anthu ndi kuwapanga kukhala otsatira ake.” *(Mir`aat, buku. 6, tsamba. 439)*

## Kuyankhula kwambiri, zolakwika zambiri

Pali mantha kuti munthu woyankhula kwambiri angagwere m'machimo monga kunama, miseche, kunena nkhani za anthu ena, kutchulana mayina oipa, ndi zina zotero. Chimodzimodzinso, pali mantha kuti munthu wolemera angagwere m'machimo monga kupondereza, kudzikweza, ndi zina zotero chifukwa chokhala ndi chuma chochuluka. Sayyiduna Hasan Basri رَحْمَةُاللّٰهِعَلَيْه anati:

1. Aliyense amene amayankhula kwambiri, zolakwa zake zidzakhala zambiri;

2. Aliyense amene ali ndi chuma chochuluka, machimo ake adzakhala ochuluka; ndipo

3. Aliyense amene ali ndi makhalidwe oyipa, adzakumana ndi chilango.

*(Tanbeeh Al-Ghafileen, tsamba. 117)*

## Chakudya chapaulendo chiyenera kukwanira ulendowo

Sahaba wotchuka, Sayyiduna Abu Zar Ghifari رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ, anayamba kuyankhula atayimirira pa Ka’bah yopatulika kuti, “Aliyense amene akundidziwa, akundidziwa, ndipo amene sakundidziwa, adziwe kuti ndine Jundub Bin Junadah Abu Zar Ghifari. Bwerani kwa m’bale wachisilamu wachifundo komanso wachikondi!” Pamene anthu



www.dawateislami.net

anabwera, iye anayamba kunena kuti: "O Anthu! Pamene aliyense wa inu asankha kuyenda ulendo wopita ku mzinda uliwonse padziko lapansi, samayenda popanda zinthu zofunikira pa ulendo. Choncho, kuli bwanji munthu amene akufuna kuyenda ulendo wopita ku Tsiku Lachiweruzo popanda zinthu zofunikira pa ulendo?" Anthu anafunsa, "O Abu Zar! Kodi zinthu zathu zofunikira pa ulendo ziyenera kukhala chiyani?" Iye anati, "Pempherani Maraka't awiri mu mdima wa usiku kuti mupewe mavuto a m'manda, salani kudya kwa chilimwe chifukwa cha Tsiku Lachiweruzo, perekani Sadaqah kwa osauka kuti mupeze chipulumutso ku chilango cha tsiku lovuta, ndipo pangani Hajj chifukwa cha nkhani zina zazikulu. Gawani dziko lapansi mu magawo awiri, gawo limodzi lofunafuna dziko lapansi, ndipo gawo lina lofunafuna Dziko limene likubwera. Kupatula apo, kupanga gawo lachitatu ndi koyipa, sikopindulitsa. Chimodzimodzinso, gawani zokambirana zanu mu magawo, gawo limodzi lokuthandizani padziko lapansi, ndipo lina likukuthandizani ku Tsiku Lachiweruzo, ndipo lachitatu ndi loyipa osati lopindulitsa." Kenako iye anati, "Ah! Chisoni cha tsikulo chandipha chimene ndilibe machiritso." Anafunsidwa kuti, "Ndi chiyani chimenecho?" Iye anati, "Ziyembekezo zanga zapitirira msinkhu wanga, ndipo ndakhala ndikunyalanyaza za ntchito yanga." *(Tanbeeh Al-Ghafileen, tsamba. 118)*

Okondedwa abale achisilamu okondedwa! Ngakhale kuti Sayyiduna Abu Zar Ghifari رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anali wochita zabwino, akunena za iye yekha modzichepetsa kuti, "Ndakhala ndikunyalanyaza za ntchito yanga", nanga tidzakhala chiyani ife? Timalephera kuchita ntchito iliyonse yabwino, ndipo ngati tichita kulambira kulikonse kosakwanira, Satana amatibweretsera m'mitima mwathu kuti ndife oyera kwambiri, ndife



www.dawateislami.net

abwino, ndipo timanyengedwa ndi Satana, ifenso timagwera m'maganizo olakwika akuti ndife anthu oyera. Kuchokera ku nkhaniyi, tiyenera makamaka kuphunzira phunziro la kudzichepetsa, ndipo tiyenera kudziona ngati ochimwa, ngakhale titachita ntchito zabwino zochuluka motani.

## Udindo wa kukhala chete popanga malo wolimbikitsa-Sunnah pa khomo

**O omukonda Rasool!** Posiya zizolowezi za mkambirano osafunikira, kuseka, ndi khalidwe loyipa, ulemu wanu udzawonjezereka panyumba. Ndipo pamene anthu a m'banjamo alimbikitsidwa kuchokera mu kukhwima kwanu, اِنْ شَآءَاللّٰه 'kuyitanira kwanu ku chilungamo' kudzalowa m'mitima mwawo nthawi yomweyo, ndipo zidzakhala zosavuta kupanga malo olimbikitsa Sunnah panyumba. Choncho, pambuyo pomvera ulaliki wolimbikitsa Sunnah pa mutu wa 'kufunika kokhala chete' woperekedwa mu msonkhano wolimbikitsa Sunnah wa Dawat-e-Islami, اَلْحَمْدُ لِلّٰه M'bale wachisilamu woyankhula kwambiri anayamba kukhala ndi chizolowezi chokhala chete.

سُبْحٰنَ اللّٰه zinayamba kumubweretsera phindu. Banja lake linali litatopa ndi chizolowezi chake 'choyankhula zopanda pake', koma atayamba kukhala chete, udindo wake panyumba udakhala wamphamvu, makamaka amayi ake omwe anatopa naye kalekale anakhala okondwa. Ngakhale nthawi zonse ankayankhula zopanda pake, komabe zokambirana zake zothandiza zinkakhala zopanda mphamvu. Koma tsopano akamawauza amayi ake Sunnah iliyonse, samangomvera mwatcheru, komanso amayesa kuchita zinthu molingana ndi Sunnah yo.



www.dawateislami.net

*Barhta hay khamoshi say waqaar ay mayray piyaray*

*Ghar walay bhi hoja`ayn gay Khush ap say saray*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Zoyipa za kufunsa mafunso opanda pake

Sayyiduna Imam Muhammad Bin Muhammad Bin Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Kufunsa munthu wina funso lokhudza chinthu chopanda pake kumachokera ku zokambirana zopanda pake, ndipo pofunsa funso lamtunduwu, mudzataya nthawi yanu komanso kukakamiza munthu winayo kuti atayenso nthawi yake poyankha funso limenelo. Izi zimagwira ntchito pokhapokha ngati palibe vuto lililonse pofunsa funso lililonse; apo ayi, nthawi zambiri pamakhala mavuto pofunsa mafunso. Mwachitsanzo, pofunsa funso kwa munthu wokhudza kulambira kwake kuti 'kodi mukusala kudya?', ngati atayankha kuti inde, iye ndiye wochita kulambira kwake ndipo motero akhoza kugwera mu kudzionetsera. Ngati sangadzionetsere, kupembedza kwake kudzacho tsedwa mu buku la 'kulambira kobisika', ndipo kulambira kobisika kuli ndi madalitso ambiri kuposa kulambira koonekera, ndipo ngati atayankha kuti ayi, adzakhala wabodza, ndipo ngati atakhala chete, adzakuonani ngati otsika ndipo mudzakumana ndi mavuto chifukwa cha zimenezo, ndipo ngati atachita zinthu molakwika, adzayenera kuvutika. Choncho, mwamupangitsa kuti azionetsere, kunama, kudziona ngati otsika kapena kuchita zinthu molakwika chifukwa cha funso limodzi chabe.

Izi zili zofanana ndi zimene mumamufunsa za zochita zake za kulambira. Komanso, izi zili zofanana ndi zimene mumamufunsa za tchimo lake ndi



www.dawateislami.net

zina zonse zimene amabisa kwa anthu ndipo amapanga manyazi kunena. Chimodzimodzinso, ngati wina akuyankhula ndi munthu wina ndipo pambuyo pa zokambiranazo, inu mukumufunsa kuti 'mumanena chiyani?' ndi 'munali kuyankhula zokhudza chiyani?' Chimod zimodzinso, pomuyang'ana munthu wina wake panjira, mukumufunsa kuti 'mukuchokera kuti?'. Ndiye nthawi zina pamakhala chifukwa chomwe chimamulepheretsa kunena, ndipo ngati wanena, amakumana ndi mavuto ndipo amapanga manyazi, ndipo ngati asanene zoona, amayamba kunama, ndipo inu mumakhala chifukwa cha zimenezo. Chimodzimodzinso, mumafunsa funso limene simukufuna, ndipo amene wafunsidwa funso, nthawi zina Nafs yake (umunthu wamkati) siyimamulola kunena kuti "لَا اَدْرِی" (kutanthauza, sindikudziwa) ndipo motero ngakhale alibe uzindikiri, amapereka yankho. (Zitsanzo za mafunso opanda pake zikubwera patsogolo" *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 140)*

## Nzeru za Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه

Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafunsidwa kuti: "Kodi nzeru zanu ndi chiyani?" Iye anati, "Chilichonse chimene sindikuchifuna, sindimufunsa zokhudza chimenecho, ndipo chilichonse chimene sichindipindulitsa, sindimapanga chimenemo." *(Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 345)*

## Kukhala chete ndi nzeru (Nkhani)

Zokambirana zopanda pake, sindikutanthauza mafunso amtunduwu, chifukwa amangobweretsa machimo kapena zoyipa. Chitsanzo cha



www.dawateislami.net

zokambirana zopanda pake ndi nkhani yomwe inafotokozedwa yokhudza Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه. Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anabwera tsiku lina pa bwalo loyera la Mtumiki Wokondedwa wa Allah Wamphamvu zonse Sayyiduna Dawood عَلَيْهِ السَّلَام. Panthawiyo, iye عَلَيْهِ السَّلَام anali kupanga zida zankhondo (chishango chopangidwa ndi chitsulo chovala pankhondo). Chifukwa Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه sanawonepo zida zankhondo, n'chifukwa chake anali odabwa kuziona ndipo anafuna kufunsa za izi, koma anakhala chete chifukwa cha 'nzeru'. Panthawi yomwe Sayyiduna Dawood عَلَيْهِ السَّلَام anali atamaliza kupanga chishango, ndiye ananena atachivala kuti," Chinthu chabwino kwambiri chishango pankhondo!" Atamva izi, Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Kukhala chete ndi nzeru, koma amene amazisunga ndi ochepa kwambiri." Ndiko kuti, popanda kufunsa funso lililonse, ndinadziwa zokhudza chimenechi, ndipo panalibe chifukwa chofunsira. *(Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 347; Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 141)*

## Ndi mkambirano uti umene umatchedwa opanda pake?

Sayyiduna Imam Muhammad Bin Muhammad Bin Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Zafotokozedwa kuti Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه amkapita pa maso pa Sayyiduna Dawood عَلَيْهِ السَّلَام kwa chaka chimodzi kuti akadziwe za zida zankhondo popanda kufunsa funso lililonse. Pamene kuwululidwa kwa vuto lililonse kapena kuluza komanso kutenga mbali pa (kunama) ndi kudzionetsera sikumapezeka pamenepa ndi mafunso ena otere, ndiyeno uwu ndi mkambirano wopanda pake, ndipo kusiya izi ndi khalidwe la Chisilamu. Ili ndi tanthauzo la mkambirano wopanda pake." *(Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 347)*



www.dawateislami.net

## Uthenga okhudzana ndi Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُاللّٰہِعَلَیْہ

Ubwino wa Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُاللّٰہِعَلَیْہ ndi waukulu kwambiri. Mu Gawo 21 la Qur'an Yopatulika, muli Surah 'Surah Luqman' yonse yotchulidwa ndi dzina lake. Allah Wamphamvu Zonse watchula za nzeru za Sayyiduna Luqman mu vesi 12:

وَلَقَدْ اٰتَیْنَا لُقْمٰنَ الْحِكْمَةَ اَنِ اشْكُرْ لِلّٰهِؕ وَمَنْ یَّشْكُرْ فَاِنَّمَا یَشْكُرُ لِنَفْسِهٖۚ

وَمَنْ كَفَرَ فَاِنَّ اللّٰهَ غَنِیٌّ حَمِیْدٌ ﴿۱۲﴾

*Ndipo ndithudi Ife tinamupatsa nzeru Luqmaan (kunena kuti) 'Khalani oyamika kwa Allah.' Ndipo aliyense woyamika, amayamika pa ubwino wake yekha; ndipo aliyense wosayamika, ndithudi Allah ndi Woyima payekha, Wotamandika Kwambiri.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 21, Surah Luqman, vesi 12)*

## Luqman Hakeem anali ndani?

Zafotokozedwa mu *Sirat-ul-Jinan*, tsamba 483, buku 7 kuti: "Sayyiduna Wahb رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ ananena kuti Sayyiduna Luqman رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَیْہ Anali mwana wa mlongo wa Sayyiduna Ayyub عَلَیْہِ السَّلَام. Komabe, Maqaatil رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَیْہ, wothirira ndemanga wa Qur'an Yopatulika, ananena kuti anali mwana wa azakhali ake a Sayyiduna Ayyub عَلَیْہِ السَّلَام. Anali mu nthawi ya Sayyiduna Dawood عَلَیْہِ السَّلَام ndipo anaphunzira maphunziro kuchokera kwa iye. Asanalengeze uneneri wa Sayyiduna Dawood عَلَیْہِ السَّلَام, iye ankapereka Fatwa, ndipo pamene Sayyiduna Dawood عَلَیْہِ السَّلَام analandira uneneri (pamene analengeza uneneri), iye رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَیْہ anasiya kupereka Fatwa. Pali maganizo osiyansiyana pa za uneneri wake. Akatswiri ophunzira ambiri

amakhulupirira kuti anali Hakeem (kutanthauza, munthu wanzeru ndi luntha), osati mtumiki. *(Tafseer-e-Baghwi, buku. 3, p. 423; Tafseer-e-Madarik, p. 917)*

## Sayyiduna Luqman ndi m'modzi mwa atsogoleri aku Paradaiso

Sayyiduna Abdullah Bin Abbas رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ anafotokoza kuti Mtumiki Woyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, "Khalani nawo mu gulu la anthu a ku Sudan, anthu atatu mwa iwo ndi atsogoleri a anthu aku Paradaiso:

1. Sayyiduna Luqman Hakeem
2. Sayyiduna Najashi
3. Moazzin (wa Mtumiki Woyera) Sayyiduna Bilal رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ.

*(Mu'jam Kabeer, buku. 11, tsamba. 158, Hadith, 11482)*

## Matanthauzo anayi a nzeru

Pali matanthauzo ambiri a nzeru. Anayi mwa iwo atchulidwa mu Sirat-ul-Jinan, buku 7, tsamba 484:

1. Nzeru zimatchedwa luntha ndi kumvetsa.
2. Nzeru ndi maphunziro omwe amagwiritsidwa ntchito moyenerera.
3. Nzeru zimatchedwa Ma'rifat [kuzindikira] ndi mphamvu ya zochita.
4. Nzeru ndi chinthu chomwe ngati Allah Wamphamvu zonse wachiyika mumtima mwa munthu, chimawalitsa mtima wake.

*(Tafseer Khaazin, buku. 3, tsamba. 470)*



www.dawateislami.net

## Sayyiduna Luqman anali Dokotala

Sayyiduna Allamah Ismail Haqqi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza mu '*Ruh-ul-Bayan*': "Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anali dokotala komanso munthu wodziwa zambiri komanso wanzeru." *(Tafseer Ruh Al-Bayan, buku. 7, tsamba. 73)*

## Kuyipa kokhala m'chimbudzi nthawi yayitali

Sayyiduna 'Ikramah رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti: "Pamene mbuye wake anapita kuchimbudzi, anachedwa. Sayyiduna Luqman رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafuula kuti: 'Kukhala nthawi yayitali kuno kumabweretsa vuto ku chiwindi, ndipo kumabweretsa matenda a zotupa, ndipo kutentha kumafika kumutu. Khalani kanthawi kochepa kuchimbudzi ndipo tulukani nthawi mwachangu.' Mankhwala wa a Sayyiduna Luqman رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analembedwa ndikupachikidwa pakhomo." *(Tafseer Durr-e-Mansor, buku. 6, tsamba. 510)*

## Ngati lilime ndi mtima zitakhala zoyipa, ndiyeno…

Bwana wa Sayyiduna Luqman Hakeem رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Iphani mbuzi yaikazi ndipo mubweretse ziwiri mwa ziwalo zake zabwino kwambiri." Iye anabweretsa lilime ndi mtima. Patapita masiku angapo, bwana wake anamupemphanso kuti, "Iphani mbuzi yayikazi ndipo mubweretse ziwiri mwa ziwalo zake zoipitsitsa." Iye anabweretsanso lilime ndi mtima. Pamene bwana wake anamufunsa, Sayyiduna Luqman رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Ngati lilime ndi mtima zili bwino, ndiye kuti ndi zabwino kwambiri; ndipo ngati zisokera, palibe choipa kuposa izo." *(Tafseer Tabri, buku. 10, tsamba. 209)*



www.dawateislami.net

## Zitsanzo za mafunso opanda pake

- Kufunsa popanda funikira kulikonse: Mwagula zingati? Mwatenga pa zingati? Mtengo wa malo pakuti-pakuti ndi zingati?

- Ngati mwapita kunyumba kwa munthu kapena wina wagula nyumba yatsopano, mumafunsa funso langati 'mwagula zingati?' 'Muli zipinda zingati?' 'Ndalama yolipira ndi zingati?' 'Mwini nyumba ndi wotani?' (Kufunsa za mwini nyumba nthawi zina, Allah aletse, kungakhale chifukwa chotsegula chitseko cha miseche ndi kuyipitsirana mbiri ponena nkhani za anthu ena. Mwachitsanzo, mutha kupeza yankho loti: mwini nyumba wathu ndi wamwano kwambiri, wankhanza kwambiri, kapena wosayenera kapena wokwiya msanga kapena womana chuma, ndi zina zotero.

- Kumufunsa munthu amene mukukumana naye kuti 'Muli ndi ana angati?' 'Mwana wanu wamwamuna (kapena wamkazi) wamkulu ali ndi zaka zingati?' 'Kodi ali pachibwenzi (kapena wokwatira)?'

- Chimodzimodzinso, pamene wina wagula sitolo yatsopano, galimoto kapena njinga yamoto, ndi zina zotero, mumafunsa wogulayo mafunso osafunikira okhudza mtengo wake, kulimba kwake, ndalama zolipira nthawi yomweyo, ndalama zolipira pang' onopang'ono, ndi zina zotero.

- Zochita za othandizira kufunsa mafunso osiyanasiyana opanda pake komanso zambiri za mankhwala kuchokera kwa wodwala wosauka yemwe satha ngakhale kuyankhula; ngati opaleshoni inachitika, ngakhale kufunsa za chiwerengero cha masitichi mpaka ngati pali nkhani ya 'malo obisika', ena samachita manyazi ngakhale kufunsa za



www.dawateislami.net

izo. Ngakhale amayi samatsalira mwanjira iliyonse pazinthu zopanda pake zoterezi.

- Kuyankhula za zoipa za nyengo yachilimwe kapena yachisanu popanda chifukwa chilichonse monga munthu woyankula kwambiri kunena pa nthawi yotentha kuti: "Kuli kutentha kwambiri lero, ndipo magetsi amathima mobwerezabwereza."

- Chimodzimodzinso, kuchita ndi kunena nthawi yachisanu kuti: "Kukuzizira kwambiri lero."

- Ngati ndi nyengo yamvula, kuyika ndemanga popanda chifukwa chilichonse monga: "Masiku ano kukugwa mvula yambiri. Madzi angoyima palikonse. Boma silimakhala ndi chidwi chilichonse pankhani yoyeretsa zonyansa, ndi zina zotero."

- Chimodzimodzinso, kusanthula kosafunikira pazochitika za dziko komanso za ndale popanda cholinga chosintha; kutsutsa kosafunikira magulu osiyanasiyana a ndale.

- Ngati mwayenda mumzinda kapena dziko, kufotokozera kosafunikira mapiri ake ndi zobiriwira, kufotokoza kosafunikira nyumba ndi misewu, ndi zina zotero. Ngati ichi si chokambirana chopanda pake, ndiye kuti ndi chiyani? Komabe, kumbukirani kuti ngati tapeza wina akuyankhula zopanda pake, tiyenera kudziteteza ku kukayikira koyipa, chifukwa nthawi zina zokambirana zomwe timaganiza kuti ndi zopanda pake zimapezeka kuti zinachitika ndi woyankhulayo chifukwa cha cholinga china choyenera, chifukwa chake, sizimakhalabe zopanda pake. Kuchita zinthu za Mubah (kutanthauza kuti palibe mphoto kapena tchimo) ndi zitsimikizo zabwino kumakhala chifukwa chopezera mphoto.



www.dawateislami.net

## Ndi zovuta kwa munthu woyankhulitsa kwambiri kupewa kukokomeza

Kumbukirani kuti kuyankhula zopanda pake si tchimo, koma kukambirana zopanda pake kumakhala kopanda pake pamene kwanenedwa molondola momwe kuliri. Vuto ndilakuti kuchita zokambirana zamtunduwu mosamala kuti zisapitirire malire a 'kusafunikira' ndi ntchito yovuta kwambiri. Kukokomeza kumachitika mobwerezabwereza. Nthawi zina munthu amene amayankhula zopanda pake amalowanso mu dzenje la miseche, kunyoza, ndi kuvulaza maganizo a anthu mosalungama. Choncho, muli mtendere mu kukhala chete monga 'khalani chete, pezani chisangalalo chachikulu'.

## Udindo wa kukhala chete popanga malo kukhala achipembedzo m'dera

Asanamvetsere ulaliki wolimbikitsa Sunnah pa mutu wa 'kukhala chete' pamsonkhano wolimbikitsa Sunnah wa 'Dawat-e-Islami', m'bale wina wachisilamu anali woyankhulitsa kwambiri. Sanali wokonda kuwerenga Salat mochuluka. Pamene anayamba kukhala chete, anayamba kudalitsidwa ndi kuwerenga Salat tsiku lililonse kokwana chikwi. Kale, ankawononga nthawi yake yamtengo wapatali pokambirana zopanda pake. Atayamba kukhala chete, ine (Sag-e-Madinah) anandipatsa mphatso (Isal-e-Sawab) ya Salat 12 000 zomwe zinawerengedwa m'masiku 12. Chifukwa cha kuipa kwa zokambirana zopanda pake zomwe zinatuluka chizolowezi chake chokonda kuyankhula kwambiri, ntchito yachipembedzo ya Dawat-e-Islami yomwe imachitika mu Zayli Halqah yake inakhudzidwanso kwambiri. Masiku apitawo Madani Mashwarah anachitikira ku Halqah kwake kuti achotse kusagwirizana pakati pawo.



www.dawateislami.net

Chodabwitsa n'chakuti, chifukwa cha kukhala kwake chete, اَلْحَمْدُ لِلّٰه mikangano yonse inathetsedwa mosavuta. Posonyeza chimwemwe, 'Nigran' wake ananena moona mtima motere, 'Ndinali ndi mantha kwambiri kuti mungayambe kukangana ndipo zinthu zidzaipiraipira, koma dalitso la inu la kukhala chete linatipatsa mtendere.' Chifukwa chake ndi chakuti, zisanachitike zimenezi, chifukwa cha mkangano wake wosafunikira komanso chizolowezi choipa chokambirana zopanda pake zikanawononga malo a 'Madani Mashwarah', ndi zina zotero.

## Chida cha Madani cha ntchito za chipembedzo

Okondedwa abale achisilamu! Kodi mwazindikira kuti! Kukhala kutali ndi zokambirana zopanda pake kumathandizanso kwambiri pa ntchito zachipembedzo. Choncho, aliyense amene ali mlaliki wa Sunnah, ayenera kukhala wosamala kwambiri komanso kukhala chete zivute zitani. Aliyense amene amayankhula kwambiri, amadula zokambirana za ena, amayankhula mobwerezabwereza pakati pa mkambirano, amakangana pa zinthu zazing'ono, chifukwa cha zonsezi, pamakhala kukayikira kuti ntchito zachipembedzo zidzakhudzidwa kwambiri, chifukwa woyankhulitsayu alibe kukhala chete kotere komwe ndi 'chida' chothamangitsira Satana.

Popanga chifuniro chake kwa Sayyiduna Abu Zar Ghifari, Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Kupangeni kukhala chete mochuluka kukhala kokakamiza, chifukwa kudzathamangitsa Satana, ndipo mudzapeza thandizo pa ntchito zachipembedzo." *(Shu'ab Al-Iman, buku. 4, tsamba. 242, Hadith 4942)*

*Allah is say pehlay iman pay mout dayday*

*Nuqsan mayray sabab say ho Sunnat-e-Nabi ka*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 178)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Munthu wopusa amayankhula opanda kuganizira

Okondedwa abale achisilamu! Munthu wanzeru amaganiza kaye kenako amayankhula, pamene wopusa amayankhula chilichonse chimene chamubwerera mkamwa. Sasamala kuti adzachititsidwa manyazi chifukwa cha zimenezi. Sayyiduna Hasan Basri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Zinali zodziwika pakati pa anthu kuti lilime la munthu wanzeru lili kumbuyo kwa mtima wake. Asanayankhule, amayankhulana kaye ndi mtima wake. Zikutanthauza kuti amaganiza kaye ngati ayenera kunena izi kapena ayi. Ngati zili zaphindu, amayankhula; apo ayi amakhala chete. Kumbali ina, lilime la munthu wopusa lili patsogolo pa mtima wake, chifukwa alibe mwayi woyankhulana ndi mtima wake. Amangoyankhula chilichonse chimene chamubwerera mkamwa." *(Tanbeeh Al-Ghafileen, tsamba. 115)*

## Samalirani lilime, chilichonse chidzakhala bwino

Aliyense amene angathe kusamalira lilime lake, ntchito zake zonse zimayenda bwino. Sayyiduna Yunus Bin 'Ubaid رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti Aliyense amene lilime lake liri bwino, ntchito zake zonse zimakhala bwino. *(Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 3, tsamba. 339; Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 137)*

## Ganizirani musanayankhule



www.dawateislami.net

Monga momwe munthu amanong'oneza bondo akachitiridwa chinyengo chifukwa cha kusasamala pogula chinachake, momwemonso, munthu amene amagwiritsa ntchito lilime mosafunikira amanong'onezanso bondo. Munthu wina wochita zabwino wa Allah anati, "Sungani zokambirana zanu motetezeka ngati chuma, ndipo mukafuna kugwiritsa ntchito (chuma ichi), ganizirani mosamala musanachigwiritse ntchito."

## Njira yolingalira musanayankhule

O omukonda Rasool! Kumbukirani kuti Mtumki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Sanatulutsepo mawu opanda pake kuchokera pa lilime lake lodala kapena kuseka. Ndikukhumba kuti Sunnah yakukhala chete igwiritsidwenso ntchito ndipo chizolowezi chathu choseka chithe. Ndikukhumba kuti tikhale omwe amaganiza kaye asanayankhule. Njira yoganizira musanayankhule ingakhale yakuti, tisanayankhule mawuwo, tiyenera kufunsa mtima wathu kuti 'Cholinga chonena zimenezi ndi chiyani?' 'Kodi ndikuwuza wina aliyense za chilungamo?' 'Kodi chinthu chimene ndikufuna kunena chili ndi phindu lililonse kwa ine kapena ena?' 'Kodi ndidzapeza mphotho iliyonse ponena izi?' 'Kodi mawu anga akukhazikika pa kukokomeza kuti andilowetse pakunama?' Pamene ndikupereka chitsanzo cha kukokomeza, Sayyiduna Allamah Maulana Mufti Muhammad Amjad Ali A'zami رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Ngati wina anabwera kamodzi ndipo zanenedwa kuti anabwera kokwana chikwi (1000), ndiye kuti ndi wabodza." *(Bahar-e-Shari'at, bku. 3, tsamba. 519)*

Ayeneranso kuganizira kuti 'Ngati ndikungomusangalatsa munthu wina kapena kuyamikira zoipa za munthu wina' 'Ngati ndikumunena miseche munthu wina' 'Kodi pali wina amene angapwetekedwe ndi mawu angawa?' 'Nditatha kuyankhula, kodi ndidzapeza kuti ndikuyenera



www.dawateislami.net

kunena mawu oti ‘pepani’ chifukwa cha manyazi?’ ‘Kodi ndidzafunika kupepesa chifukwa cha zomwe ndinanena mwaukali?’ ‘Kodi ndidzaulula chinsinsi changa kapena cha wina aliyense?’ Ngakhale mutaganizira musanayankhule, ngati zitapezeka kuti kuyankhula kumeneku kulibe phindu kapena kuluza, kapena mphoto kapena machimo, ngakhale zili choncho pali kuluza kwina pakuyankhula chinthu chotere, chifukwa m’malo movutitsa lilime kuti linene zinthu zopanda pake komanso zosafunika zotere, ngati mawu oti “لَآ اِلٰهَ اِلَّا اللّٰهُ مُحَمَّدٌ رَّسُوْلُ اللّٰه صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم” atanenedwa ndi cholinga chofuna malipiro kapena kuwerenga Salat, ndithudi muli phindu mu ntchito imeneyi, ndipo uwu ndi mwayi wabwino kwambiri wogwiritsa ntchito nthawi yanu yomwe imakutsogolerani ku Paradiso. Ndithudi ndi kuluza kuwononga phindu lalikulu lotere.

*Zikr-o-Durood har ghari wird-e-zaban rahay*

*Mayri fuzol goyi ki ‘aadat nikaldo*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 305)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب ! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Njira yokhalira chete

Okondedwa abale achisilamu! Ngakhale mkambirano wopanda pake si tchimo lililonse, komabe umakhala ndi kuluza komanso zoyipa. Choncho, n’koyenera kupewa. Ndikukhumba tikanakhala ndi mwayi wokhala ndi chizolowezi chokhala chete. Sikofunikira kuti tipatsidwe madalitso okhala chete nthawi yomweyo. Tiyenera kuyesetsa kwambiri pa izi. Aliyense amene akufuna kukhala ndi chizolowezi chokhala chete,



www.dawateislami.net

ayenera kuchita izi mozama kwambiri ndikuyesetsa kwambiri kuchotsa mawu oti 'kusowa chiyembekezo' mu dikishonale mwake. Sayyiduna Muwarriq 'Ijli رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه ananena kuti, "Panali chinthu china chimene ndinayesetsa kukwaniritsa kwa zaka 20 koma osakwaniritsa, komabe sindinataye mtima kuti ndichikwaniritse." Anafunsidwa kuti: "Kodi chinthu chofunikira chimenecho ndi chiyani?" Zinayankhidwa kuti: "Kukhala chete." *(Al-Zuhd lil Imam Ahmad, tsamba. 310, mawu nambala, 1762)*

Aliyense amene akufuna kukhala ndi chizolowezi chokhala chete sayenera kugwiritsa ntchito lilime lake. M'malo mwake, ngati n'kotheka, ayenera kupanga zokambirana zofunikira pang'ono polemba kapena pogwiritsa ntchito manja tsiku lililonse. اِنۡ شَآءَاللّٰه, mwanjira imeneyo chizolowezi chokhala chete chidzayamba kukula.

## Palinso kuyankha mlandu pa kuyankhula zopanda pake pogwiritsa ntchito chinenero cha manja

Kumbukirani kuti padzakhala chiwerengero cha zokambirana zopanda pake pa Tsiku Lachiweruzo, kuyang'ana moipa kutanthauza kuyang'ana mozungulira mopanda cholinga, kuyang'ana zinthu zopanda pake, kugwiritsa ntchito manja opanda pake kuchokera kwa munthu wabwinobwino kapena wosamva, kupanga phokoso mopanda pake, ndi zina zotero.

اَلۡحَمۡدُ لِلّٰه pali 'Ntchito yabwino ' nambala 53 yotchulidwa mu kabuku kokhudza kupanga ntchito zabwino kotchedwa 'Ntchito Zabwino' kochokera ku 'Dawat-e-Islami': Kodi mwagwiritsa ntchito zizindikiro zina lero pofuna kukhala ndi chizolowezi choletsa lilime lanu kukambirana zopanda pake (kutanthauza kuti zokambirana zomwe sizipindulitsa

padziko lapansi kapena pa tsiku lomaliza)? (Ndi zabwino ngati mukukambirana tsiku ndi tsiku polemba osachepera kanayi komanso pogwiritsa ntchito chiyankhulo cha manja osachepera katatu.) Pamene mukuyesetsa kukhala ndi chizolowezi chokhala chete, n'zothekanso kuti masiku ena mungathe kupewa zokambirana zopanda pake, koma m'malo mwake mumabwerera ku chizolowezi choyankhula kwambiri monga kale. Ngati zimachitika, musataye mtima. Pitirizani kuyesetsa mobwerez abwereza. Ngati chidwi chili chenicheni, اِنْ شَآءَاللّٰہ mudzapambana tsiku lina. Malingana ndi mwambi wachiarabu umanena kuti: "اَلسَّعْیُ مِنِّیْ وَالْاِتْمَامُ مِنَ اللهِ" kutanthauza kuti, Khama ndi langa, ndipo kumalizitsa ntchitoyo kumachokera kwa Allah Wamphamvu zonse. Malinga ndi mwambi wina wachiarabu: "مَنْ جَدَّ وَجَدَ" kutanthauza kuti, Aliyense amene amayesetsa amakwaniritsa. Pamene mukuyeserera kukhala ndi chizolowezi chokhala chete, n'koyenera kuyipanga nkhope yanu kukhala yomwetulira kuti munthu winayo asaganize kuti mwamukwiyira, n'chifukwa chake mukukwinyata nkhope. M'masiku oyeserera kukhala chete, mkwiyo ukhoza kubuka; choncho, ngati wina sakumvetsa chizindikiro chanu, musamusonyeze mkwiyo wanu, kuti musadzapalamule tchimo lovulaza munthu mopanda chilungamo. Chiyankhulo cha manja ndi choyenera kwa anthu okha amene muli ndi maganizo ofanana; apo ayi, ndi zotheka kuti munthu wachilendo akhoza kukukwiyirani, chifukwa sakumvetsa mkambirano wanu ogwiritsa ntchito manja, ndi zina zotero. Choncho, yankhulani naye monga momwe zikufunikira. Nthawi zina, kuyankhula kumakhala Wajib – mwachitsanzo, kuyankha Salam kwa mlendo ndi lilime, ndi zina zotero. Kumbukiraninso kuti muyenera kunena Salam ndi lilime osati ndi chiyankhulo cha manja. Kupatula zimenezi, pali nthawi zosiyanasiyana zimene muyenera kunena Salam ndi lilime.



www.dawateislami.net

Chimodzimodzinso, ngati makolo ndi achibale ena akukhalabe ndi kukayikira, yankhulani ndi lilime monga momwe zikufunikira.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Phindu lolingalira kaye usanayankhule

Ngati munthu aganizira, kutanthauza kuti ngati iye achita chizolowezi choganizira asanayankhule, iye mwiniyo amayamba kuzindikira ziganizo zake zambiri zopanda pake. Ngati pali 'ziganizo zopanda pake' zokha zokha, si tchimo ayi, koma zimakhala ndi mitundu ingapo ya zoyipa. Mwachitsanzo, munthu amavutika kugwiritsa ntchito lilime lake pa zokambirana zoterezi ndipo nthawi yofunika kwambiri imatayika. Ngati Zikr ya Allah Wamphamvu zonse, Salat, kapena kuphunzira zachipembedzo zimachitidwa panthawiyi kapena Sunnah iliyonse yatchulidwa, pamakhala malipiro ambiri, ndipo chimodzi mwa zoyipa zazikulu za zokambirana zopanda pake ndichakuti pali chiwerengero cha zimenezo (zokambirana).

## Mkambirano opanda pake wa uchigawenga

مَعَاذَالله Ngati nkhani iliyonse ya uchigawenga yachitika kwinakwake, anthu amalowa m'zokambirana zopanda pake ndipo nthawi zina, zokambirana zodzaza ndi machimo. Kukambirana, kuganiza zopanda pake, kusanthula mopusa, kunyoza molakwika mtsogoleri aliyense, ndi ena otero a chipani chandale, ndi zina zotero, zimapezeka paliponse. Nthawi zina, mtundu uwu wa kukambirana ukhoza kukhala chifukwa cha mantha, mphekesera, ndi chisokonezo pakati pa anthu. Nafs (umunthu wamkati) imakhala ndi chidwi chachikulu chofotokozera ndi kumvetsera milandu ya nkhani



www.dawateislami.net

zauchigawenga. Nthawi zina munthu amapempha koma pamakhalanso chidwi chobisika komanso chochokera pansi pamtima chosangalala ndi kukondwera pofotokozera ndi kumvetsera nkhani zosangalatsa muzochitika zoterezi. Ndikulakalaka tinakamazindikira kuyipa kwa Nafs ndikusiya chidwi chokambirana za uchigawenga komanso nkhani yake imene yafala. Komabe, sitiyenera kusiya kupanga Du'a yowapemphera chikhululuko amene amwalira, kukhala ndi chifundo kwa Asilamu ovulala ndi okhudzidwa, ndikupempherera mtendere ndi thandizo, chifukwa izi ndi ntchito za malipiro. Choncho, nthawi iliyonse pakakhala nkhani yokambirana kapena kumvetsera mtundu uwu wa kukambirana, tiyenera kulingalira mumtima mwathu kuti cholinga chathu chiyani. Ngati cholinga chili chabwino, ndi zabwino. Komabe, zotsatira za mtundu uwu wa kukambirana nthawi zambiri zimapezeka kuti ndi gwero la chisangalalo.

## Mtima wa munthu woyankhulitsa umakhala wouma

Zinafotokozedwa ndi Sayyiduna 'Isa عَلَيْهِ السَّلَام kuti: "Kungopatula Zikr ya Allah Wamphamvu zonse, musakambirane chilichonse mopambanitsa; apo ayi mitima yanu idzauma, ndipo mtima wouma umakhala kutali ndi Allah Wamphamvu zonse, koma inu simukudziwa zimenezi." *(Tanbeeh Al-Ghafileen, tsamba. 118)*

## Sayyiduna Imam Malik amkamunyengelera munthu amene amakonda kupanga miseche

Kalanga! Ngati wina 'aponya zinthu zopanda pake' masiku ano, anthu ena amamutsatira ndikumulimbikitsa kwinaku ndikumaseka. Kumbukirani! Anthu athu ochita zabwino akale رَحِمَهُمُ اللّٰه anali oona mu mtima ndi lilime.



www.dawateislami.net

Pamene mtsogoleri wamkulu wa anthu mamiliyoni achi Maliki, Sayyiduna Imam Malik رَحۡمَۃُ اللّٰہِ عَلَیۡہِ, akaona munthu akuyankhula kwambiri, amkamuuza kuti, "Sungani zokambirana zanu zina nokha (kutanthauza, yankhulani pang'ono)." *(Tanmbeeh Al-Mughtareen, tsamba. 190)*

## Munthu wophwanya malamulo anasanduka kukhala wodekha

O ofunafuna chisangalalo cha Allah Wamphamvu zonse! Amene akufunadi kusintha abwere ku malo a zochitika za chipembedzo a Dawat-e-Islami. 'Nkhani ya Madani' yabwino kwambiri yaperekedwa pano. Imvetsereni ndi kusangalala. Asanayambe kutenga nawo mbali m'malo a zochitika za chipembedzo a Dawat-e-Islami, m'nyamata wina wochokera ku Karachi anali kugwirizana ndi zigawenga. Kucheza ndi gulu la anthu oipa kunabweretsa chidwi ndipo iye analowa mu 'gulu la osamvera malamulo.' Chinali chizolowezi chawo kumenya anthu, kutukwana, ndi kulimbana mwadaladala. Iye amkayenda ndi zida. Palibe amene amkafuna kuyankhula naye chifukwa cha zochita zake zaupandu. Akubanja, achibale, ndi anansi onse anali atatopa naye kwambiri. Anadzuka ku tulo la kunyalanyalaza m'njira yoti m'dera lomwelo munali m'bale wina wachisilamu wokalamba yemwe anali kugwirizana ndi gulu lachipembedzo la okonda Rasool la 'Dawat-e-Islami'. Chikondi chake pa Madani Markaz Faizan-e-Madinah chikhoza kuganiziridwa kuchokera pa mfundo yakuti iye ankayenda kuchokera ku Liaquatabad (dera lapafupi ndi Madani Markaz Faizan-e-Madinah Karachi) kupita ku Faizan-e-Madinah kukapemphera Salah Fajr. Pamene m'bale wokalamba wachisilamu anayesetsa payekha pa iye ndikumulangiza kuti asiye machimo ndikuyamba kumapemphera Salah, iye anasangalala ndi malangizo amenewo mwakuti anayamba kupemphera Salah. Tsiku lina anakumana ndi m'bale wina wachisilamu wodalirika wa Dawat-e-Islami



www.dawateislami.net

mu Mzikiti. Chifukwa cha khama lake lapayekha, iye anabwera ku msonkhano wapasabata wolimbikitsa Sunnah wa Dawat-e-Islami. Kumeneko kunali madalitso a Sunnah. Ulaliki omwe unaperekedwa pa msonkhano wachipembedzo unagwedeza dziko lake kuchokera mkati. Pamene aliyense anapanga Zikr ya Allah pamodzi pa msonkhano wachipembedzo, iye anapeza mtendere wamkati. Chifukwa cha m'dalitso wa msonkhano wachipembedzo, chidwi chotere cha ntchito zabwino chinakula mumtima mwake moti iye anayamba kutenga nawo mu zochitika za Dawat-e-Islami. Iye analapa zoyipa ndi machimo ena. Anayamba kupereka ma Dars a Faizan-e-Sunnat. Kusintha kumene kunabwera m'moyo wake kunadabwitsa anthu ena. Anthu ena ankayankhula ndikumamuswa mtima pomunyoza za chilakolako chosakhalitsa cha masiku ena ake, koma ankamvetsera modekha, ndipo anazilonjeza yekha kuti chilichonse chimene chingachitike, sadzasiya malo a zochitika za chipembedzo. Atasiya machimo, chakudya chake chinayamba kuwonjezereka chifukwa cha madalitso a kuchita 'ntchito zabwino'. اَلْحَمْدُ لِلّٰه anapezanso mwayi wochita zinthu zachipembedzo monga Nigran wa 'Alaqai Mushawarat.

*Sanwar ja`ay gi akhirat اِنْ شَآءَاللّٰه*

*Tum apna`ay rakhon sada madani mahol*

*Buht sakht pachta`o gay yad rakho*

*Nah Attar tum chorna madani mahol*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 646)*



www.dawateislami.net

# Machiritso 7 a machimo

اَلْحَمْدُ لِلّٰه chifukwa cha madalitso okhala malo a zochitika za chipembedzo cha Dawat-e-Islami, anthu osawerengeka omwe sanali opemphera-Salah anakhala opemphera-Salah ndipo ochimwa anakhala otsatira Shari'ah ndi Sunnah. Munthu aliyense ayenera kutengera chikhalidwe chachipembedzo chodalachi. Kudzera m'madalitso a Allah Wamphamvu zonse, palinso mapemphero amene amawerengedwa ambiri omwe amakhala gwero la kupewa machimo. Mapemphero asanu ndi awiri aperekedwa pamenepa:

1. "يَا عَفُوُّ": Kudana ndi machimo kumayamba mumtima powerenga mawu amenewa mochuluka.

2. "يَا مُحْصِيُ": Ikani dzanja pachifuwa ndikuwerenga mawu amenewa kokwana kasanu ndi kawiri mukamagona. اِنْ شَآءَاللّٰه mudzakhala okonda kupembedza.

3. "يَابَاعِثُ": Ikani dzanja pachifuwa ndipo muwerenge izi kokwana zana limodzi (100) mukamagona kuti muzisangalala ndi kulambira. اِنْ شَآءَاللّٰه kudana ndi machimo kudzayamba.

4. "يَا قَهَّارُ": Kukonda dziko lapansi kumatha ndipo kukonda Allah Wamphamvu zonse ndi Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم umayamba powerenga mawu amenewa mukuyenda.

5. "اَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْم": Werengani izi kokwana ka khumi tsiku lililonse kuti mukhale otetezedwa kuchokera kwa Satana.

6. "يَا مُحْيِيْ، يَا مُمِيْتُ": Kuti mukalowe ku Paradiso popanda kuwerengedwa, ikani dzanja pachifuwa, werengani kokwana kasanu ndi kawiri, ndikupemerera mpweya pachifuwa pambuyo pa Salah iliyonse. اِنْ شَآءَاللّٰه zizolowezi zoyipa zidzatha ndipo mudzakhala osangalala ndi kulambira.

7. "يَا بَاطِنُ": Werengani izi kokwana zana pambuyo pa Salah iliyonse. اِنْ شَآءَاللّٰه mudzachotsa manong'onong'o oyipa ndi malingaliro oyipa.

**Chidziwitso**: Werengani Salat kamodzi kumayambiriro ndi kumapeto kwa ntchito iliyonse. Musanayambe kuwerenga, mupangeni katswiri wina wophunzira wachi Sunni kapena Qari kuti amvetsere kaye, ndipo werengani ndi mawu olondola.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Ntchito iliyonse yabwino imene ndiyovuta kuyichita imakhala ndi malipiro ochuluka

Okondedwa abale achisilamu! Kuchotsa chizolowezi cha kukambirana zopanda pake ndi ntchito yovuta kwambiri. Komabe, izi ndi zoperekanso chilimbikitso kwambiri kuti aliyense amene akuvutika kwambiri kusiya chizolowezi cha kukambirana zopanda pake, amapezanso malipiro ambiri. Monga momwe Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananenera zokhudza kupanga Wudu m'nyengo yozizira kwambiri: "Aliyense angapange Wuzu

m'nyengo yozizira kwambiri, adzapatsidwa mphotho kawiri." *(Jami' al-Sagheer, tsamba. 512, Hadith, 8398)* Chimodzimodzinso ngati momwe, Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananenera zokhudza kuwerenga Quran yopatulika ndi kuvuta kwake: "Aliyense amene angawerenga Qur'an yopatulika modekha, ndipo zimamuvuta, kutanthauza kuti lilime lake silimatchula mosavuta ndipo amatchula movutikira, amalandira mphotho kawiri." *(Muslim, tsamba. 312, Hadith, 1862)* Komanso, Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananena zokhudza munthu amene amatsogoza munthu wina kusiya chikhumbo chake: "Aliyense amene ali ndi chikhumbo chofuna china chake koma amatsogoza munthu wina kusiya chikhumbo chake, Allah Wamphamvu zonse amumukhululukira." *(Ittihaf Al-sadat, buku. 9, tsamba. 779)* Choncho, inu otsatira a Rasool! Ngakhale timafuna kupitiriza kulankhula, komabe ngati tipanga chizolowezi cholankhula pang'ono, tidzapeza malipiro, اِنْ شَآءَاللّٰه.

Sayyiduna Ibrahim Bin Adham رَحْمَةُاللّٰهِعَلَيْه anati, "Ntchito iliyonse yabwino yovuta kwambiri kuyichita padziko lapansi, idzakhala yolemera kwambiri pa Sikelo ya Ntchito pa Tsiku la Chiweruzo." *(Tazkirah Al-Awliya, buku. 1, tsamba. 95, Mwachidule)*

## Pewani mkambirano opanda pake

Zanenedwa kuchokera kwa Sayyiduna Rakb Misri رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ kuti Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Nkhani yabwino ndi ya munthu amene amakhala wodzichepetsa ngakhale alibe vuto lililonse, amadziona ngati wonyozeka ngakhale popanda umphawi, amagwiritsa ntchito chuma chake chimene wapeza pa ntchito zabwino, amachitira chifundo anthu



www.dawateislami.net

osauka, amadziwana ndi anthu akuzindikira komanso anzeru; ndipo mwayi ndi wa munthu amene ndalama zake ndi za Halal, Baatin (mkati) ndi mokongola, maonekedwe ake ndi achipembedzo, amawateteza anthu ena kuchokera ku zoyipa zake; ndipo nkhani yabwino ndi ya munthu amene amagwiritsa ntchito maphunziro ake, amagwiritsa ntchito chuma chake mu njira ya Allah kuposa mu zofuna zake, ndipo amadziletsa kuchokera ku mkambirano opanda pake."

*(Mu'jim al-Kabeer, buku. 5, tsamba. 71, Hadith 4616)*

## Iye sadzanong'oneza bondo ku Paradaiso

Okondedwa abale achisilamu! Ndikofunikira kuti tizindikire kufunika kwa nthawi yathu. Kuwononga nthawi ndi kuluza kwakukulu. Mvetsetsani izi kuchokera ku Hadith yotsatirayi yodalitsika: Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Okhala ku Paradiso sadzadandaula kwambiri kuposa nthawi iliyonse imene samachita Dhikr ya Allah Wamphamvu zonse." *(Mu'jim Kabeer, buku. 20, tsamba. 93, Hadith 182)*

**Kufotokozera Hadith:** Sayyiduna Allamah Ali Qari رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba pofotokozera gawo la 'Okhala ku Paradiso' la Hadith yodalayi: Okhala ku Paradiso adzanong'oneza bondo pa Tsiku la Chiweruzo asanalowe ku Paradiso, chifukwa sipadzakhala kunyozeka ndi chisoni ku Paradiso. *(Harz Sameen Sharah Hasn Haseen, tsamba. 209)*

عُمْر را ضائع مَکُنْ دَر گفتگو　　　یادِ اُوکُن یادِ اُوکُن یادِ اُو

*Ndiko kuti, musawononge nthawi yanu pa zokambirana zopanda pake, Pitirizani kumukumbukira Allah Wamphamvu zonse*

## Nsonga ya cholembera

Pamene cholembera cha Sayyiduna Sulaim Razi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه (anamwalira mu 447 Hijri) chinawonongeka akulemba, (ngakhale kuti nayonso ndi ntchito yopatsa mphotho pakulemba zolemba zachipembedzo ndi zolinga zabwino, komano pofuna 'kupha mbalame ziwiri ndi mwala umodzi') anayamba kupanga Zikr ya Allah Wamphamvu zonse kwinaku akusongola nsonga ya cholembera kuti nthawi isangodutsa posongola nsonga ya cholembera basi. *(Ibn-e-'Asakir, buku. 72, tsamba. 260)*

## Kudzala mtengo ku Paradaiso

Ndithudi, nthawi ndi yamtengo wapatali kwambiri. Ganizirani izi kuchokera ku mfundo iyi yakuti, ngati mukufuna, mutha kubzala mtengo ku Paradiso mu sekondi imodzi pamene mukukhala m'dziko lapansi, ndipo njira yobzalira mtengo ku Paradiso ndi yosavuta kwambiri. Malinga ndi Hadith yodalitsika, pakati pa ma Kalimaat anayi awa, Kalimah iliyonse imene mungawerenge, mtengo udzadzalidwa ku Paradiso. Ma kalimaat anayi amenewa ndi:

(1) سُبْحٰنَ الله (2) اَلْحَمْدُ لِلّٰه (3) لَآ اِلٰهَ اِلَّا الله (4) اَللهُ اَكْبَر

*(Ibn-e-Majah, buku. 4, tsamba. 252, Hadith, 3807)*

## Ubwino omufunira zabwino Mtumiki Womaliza صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَسَلَّم

Okondedwa abale achisilamu! Kodi mwaona kuti! Kupeza mtengo wobzalidwa ku Paradiso nkosavuta bwanji! Ngati mungawerenge amodzi mwa ma Kalimat anayi omwe atchulidwa, ndiye kuti mtengo umodzi udzadzalidwa; ndipo ngati muwerenga ma Kalimat onse anayi, mitengo inayi idzadzalidwa ku Paradiso. Tsopano ganizirani kuti nthawi ndi



www.dawateislami.net

yamtengo wapatali motani kuti mitengo imabzalidwa pongoyendetsa lilime pang'ono. Choncho ndikukhumba kuti tibzale mitengo yambiri powerenga "سُبۡحٰنَ اللّٰـه" "سُبۡحٰنَ اللّٰـه" m'malo mokambirana zopanda pake, kapenanso ndi zotheka kuti kaya tayimirira, tikuyenda, takhala pansi kapena tikugwira ntchito kapena kugona, tiyenera kuwerenga Salat pa Mtumiki Womaliza صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم titapinda miyendo, chifukwa nayonso ndi ntchito yopatsa mphotho kwambiri. Mtumiki Woyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati," Aliyense amene amawerengera ine Salat kamodzi, Allah Wamphamvu zonse amapereka madalitso khumi pa iye, amamuchotsera machimo khumi, ndikumuwonjezera ulemerero kokwana ka khumi." *(Nisa`ee, tsamba. 222, Hadith, 1294)*

*Baythtay uthtay, jagtay sotay*

*Ho Ilahi! Mayra shi'aar Durood*

*(Zouq-e-Na't, tsamba. 74)*

صَلُّوا عَلَی الۡحَبِیۡب!　　　صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Phindu la pa dziko kapena la muyaya la mkambirano

O inu omukonda Mtumiki! Ndi zabwino motani kuti tikhale ndi chizolowezi choganizira kaye tisanayankhule m'njira yoti kukambirana komwe mukufuna kuchita kuli ndi phindu lililonse padziko lapansi kapena Kumwamba kapena ayi. Ngati zimenezi zikuwoneka kuti ndi zopanda pake, m'malo moyankhula, ndikukhumba kuti tikanakhala ndi mwayi wowerenga 'اللہ اللہ' kapena kuwerenga Salat pa Mtumiki Wotsiriza صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuti tipeze mphotho zambiri kapena tikanakhala ndi mwayi



www.dawateislami.net

wobzala mtengo ku Paradiso powerenga "سُبۡحٰنَ اللّٰه" kapena "اَلۡحَمۡدُ لِلّٰه" kapena "لَآ اِلٰهَ اِلَّا اللّٰه" kapena "اَللّٰهُ اَكۡبَر".

## Chitsimikizo chowerengera mawu oti 'سُبۡحٰنَ اللّٰه' kapena kuwapanga iwo kuwerengedwa

Kumbukirani! Munthu amalandiranso mphotho powerenga "اَللّٰهُ اَكۡبَر" kapena "اَللّٰهُ اَكۡبَر" ngati kudabwa kapena kuyamikira. Komabe, ngati cholinga chochitira Zikri Allah Wamphamvu zonse yaphatikizidwa, munthu adzalandira mphotho zambiri. Nthawi zina alaliki ndi owerenga Na'at amapempha anthu opezekapo kuti awerenge "سُبۡحٰنَ اللّٰه". Kuchititsa kuti zimenezi ziwerengedwe kumabweretsanso mphotho, ndipo aliyense amene amawerenga zimenezi amayeneranso kupeza mphotho. Komabe, ngati wina amene akufuna kuti zimenezi ziwerengedwe ayenera kunena motere, ndi zabwino kwambiri: Nenani ndi chitsimikizo chopanga Zikr ya Allah Wamphamvu zonse mawu oti: "سُبۡحٰنَ اللّٰه". Pa zimenezi, aliyense amene anganene "سُبۡحٰنَ اللّٰه" ndi chitsimikizo chopanga Zikr ya Allah Wamphamvu zonse, mphotho yake idzawonjezereka.

Sayyiduna 'Allamah 'Aini رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه (anamwalira mu 855 H) anati: "Ndi Mustahab kunena mawu oti "اَللّٰهُ اَكۡبَر" "سُبۡحٰنَ اللّٰه" panthawi yodabwa pa chinthu china chake." *('Umdah Al-Qari, buku. 15, tsamba. 335)* Sayyiduna Mufti Ahmad Yar Khan رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه ananena mu 'Mirat' kuti: "Aliyense

amene anganene "سُبۡحٰنَ اللهِ" kapena "اَللهُ اَكۡبَرُ" kapena "اَلۡحَمۡدُ لِلّٰه" kapena "لَآ اِلٰهَ اِلَّا الله" mwanjira iliyonse, adzalandira malipiro a Nafl Sadaqah. Kaya akunena ndi chitsimikizo chopanga Zikr ya Allah Wamphamvu zonse kapena amawerenga mawu amenewa ngati Wazifah pazosowa zilizonse kapena amanena mawu oti "سُبۡحٰنَ اللهِ" akamva nkhani iliyonse yodabwitsa kapena amanena kuti "اَلۡحَمۡدُ لِلّٰه" akalandira nkhani iliyonse yabwino, adzalandira mphotho mwanjira iliyonse popeza kutchula dzina la Allah Wamphamvu zonse ndi kulambira mu nyengo zonse. *(Mir`aat, buku. 3, tsamba. 98)*

Mwachidule, ngakhale mulibe cholinga chapadera cha malipiro chifukwa cha kuwerenga Zikr-o-Azkar ndi Awrad-o-Wazaif, kuwerenga Qur'an Yopatulika ndi Durood-o-Salam, ndikuchita ntchito zolambira zoyera, komabe mudzalandira malipiro; ndipo ngati mutapanga zolinga za malipiro, malipiro adzawonjezereka.

*Zikr-o-Durood har ghari wird-e-zaban rahay*

*Mayri fuzol goyi ki 'aadat nikal do*

صَلُّوا عَلَى الۡحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Zabwino kuposa za zokwana 60 za kupembedza

Ngati mukumva ngati mukufuna kukhala chete m'malo momawerenga chinachake, palinso zinthu zomwe zimakupatsani mwayi wopeza mphotho, zomwe zikutanthauza kuti m'malo mongoganizira zinthu



www.dawateislami.net

zosiyanasiyana, muyenera kudzipereka kwambiri pomukumbukira Allah Wamphamvu zonse, Madinah kapena Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kapena kuyamba kulingalira za maphunziro achipembedzo kapena kuganizira za imfa, kusungulumwa ndi mantha a manda, ndi zoopsa za Tsiku la Chiweruzo, mwanjira imeneyi sipadzakhala kuwonongeka kwa nthawi, koma m'malo mwake, nthawi iliyonse idzaphatikizidwa mu kulambira, اِنْ شَآءَاللّٰه. Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, (Pa nkhani za tsiku lomaliza) kulingalira ngakhale kwa kanthawi ndi kopambana kuposa kulambira kwa zaka makumi asanu ndi limodzi (60)." *(Jami'-us-Sagheer, tsamba. 365, Hadith, 5897)*

*Unki yadon mayn kho ja`iye*

*Mustafa Mustafa kiji`ay*

## Kufunikira kwa nthawi ya mtengo wapatali

Okondedwa abale achisilamu! Masiku a moyo amatanthauza maola ndipo maola amatanthauza mphindi. Mpweya uliwonse wa moyo ndi mwala wamtengo wapatali. Ndikukhumba kuti tinakakhala ndi mwayi wozindikira kufunika kwa mpweya uliwonse, kuti pasapezeke mpweya uliwonse umene ungakhale wopanda pake ndipo tisadzapeze chuma cha moyo chopanda ntchito zabwino pa Tsiku la Chiweruzo ndikukhetsa misozi yamanyazi. Ndikukhumba kuti tinakakhala ndi chizolowezi chowunika sekondi iliyonse ya moyo wathu ndipo tinakakhala titagwiritsa ntchito nthawi iliyonse ya moyo wathu pazinthu zothandiza, kuti tisadzanong'oneze bondo pa Tsiku la Chiweruzo pambuyo popeza kuti nthawi yathu inatha ndi kugwiritsidwa ntchito pamacheza.



www.dawateislami.net

## Chifukwa chachikulu choyambitsa kunyozeka

Wotsatira (Sahabi) wodala wa Mtumiki Woyera, Sayyiduna Abdullah Ibn-e-Mas'ood رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anati," Sindimachita manyazi tsiku lililonse la moyo wanga limene ladutsa kuposa tsiku lililonse la moyo wanga limene limakhala lopanda ntchito zabwino."

## Nthawi ili ngati lupanga

Sayyiduna Imam Shafa'i رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "**Nthawi ili ngati lupanga**, iduleni poyigwiritsira ntchito (ndi ntchito zabwino); apo ayi, idzakudulani (pokulowetsani mu zinthu zopanda pake)." *(Lawaqih Al-Anwaar Al-Qudsiyah, tsamba. 83)*

## Kuwerenga mu Sakrat

Sayyiduna Junaid Baghdadi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه amkawerenga Quran Yopaulika pa nthawi ya Naza'. Iye anafunsidwa kuti: "Kuwerenga pa nthawi ino?" Iye anati: "Buku langa la ntchito likupindidwa (likutsekedwa) choncho ndikuwonjezera ntchito zabwino m'menemo mwachangu." *(Sayd Al-Khatir, tsamba. 227)*

Allah Wamphamvu zonse amuchitire chifundo ndipo atikhululukire popanda chiwerengero chifukwa cha iye!

اٰمِیْن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِیّٖن صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم

## Nthawi imene Faizan-e-Sunnat yalowa m'nyumba

اَللّٰہُ اَکْبَر! Chidwi chowerenga ngakhale panthawi yochoka padziko lapansi!



www.dawateislami.net

Allah Wamphamvu zonse atipatsenso chidwi chowerenga Qur'an Yopatulika! Ameen! Kuti tipeze chidwi chowerenga komanso kuchotsa chizolowezi cha machimo, pitirizani kutenga nawo mbali m'malo a zochitika za chipembedzo cha Dawat-e-Islami nthawi zonse ndikuphunzira mabuku achisilamu a Maktaba-tul-Madinah. Nkhani yaperekedwa kuti mukopeke: Asanayambe kutenga nawo mbali mu zochitika za chipembedzo za Dawat-e-Islami, m'bale wina wachisilamu wochokera ku Sahiwal (Punjab) anali kuyendayenda mu mitundu ya dziko lapansi ndi zigwa za machimo. Anapitiriza kusiya Salah, kunama, kupanga miseche, kunena nkhani za anthu ena, ndi kuchita machimo ena ambiri akuluakulu. Moyo wake unasinthika m'njira yoti msuweni wake ochokera mbali ya mayi amene anali otenga nawo mbali mu zochitika za chipembedzo za Dawat-e-Islami anabwera kunyumba kwake. Anthu a pakhomo anachita chidwi poona zovala zake zosavuta koma zachipembedzo. Iye anafotokoza nkhani za Madani za Dawat-e-Islami kwa anthu a pakhomo, ndi chifukwa chimenechi chikondi cha Dawat-e-Islami chinakula m'mitima mwawo. Komanso, iye anapereka ngati ngati mphatso buku lotchedwa 'Faizan-e-Sunnat'. Pamene m'bale wachisilamuyo ndi anthu a pakhomo pake anaphunzira bukulo, kusintha kwabwino kunayamba kubwera m'nyumba mwawo, ndipo nthawi inafika pamene khomo limeneli linakhala logwirizana ndi zochitika za chipembedzo za Dawat-e-Islami. Pambuyo pa masiku angapo, pamene m'bale wachisilamuyo anayenda ndi Madani Qafilah kuti akaphunzire ndi kuphunzitsa Sunnah, kenako اَلْحَمْدُ لِلّٰه chifukwa cha madalitso ake, anasunga ndevu zokwana mlingo wa chibakera pankhope pake ndipo anayambA kuvala Imamah m'mutu mogwirizana ndi Sunnah. Iye nalandira madalitso ambiri moti sanangoyamba Dars-e-Nizami ku Jamia-tul-Madinah, komanso alongo ake awiri nawonso anayamba kuphuzira Dars-e-Nizami ku Jamia-tul-Madinah (ya aakazi).



www.dawateislami.net

O okonda Sunnah za Mustafa! Kupereka ndi kulandira mphatso ndi Sunnah. Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "تَهَادَوْا تَحَابُّوْا" Kutanthauza kuti, patsanani mphatso. Chikondi chidzaonjezereka. *(Mauta, buku. 2, tsambs. 407, Hadith 1731)* Tikuphunzira kuchokera ku Hadith yodalitsikayi kuti chikondi chimawonjezereka popereka mphatso, ndipo ngati mphatsoyi ndi buku lachipembedzo, ndi kutheka kuti maphunziro amawonjezerekanso kuwonjezera pa chikondi. Choncho, ngati ndi kotheka, gulani mabuku achisilamu kuchokera ku Maktaba-tul-Madinah ya Dawat-e-Islami ndipo perekani kwa achibale anu ndi abwenzi ngati mphatso. Gawani m'misonkhano yaimfa ndi maukwati komanso pazochitika za Isal-e-Sawab ya achibale anu omwe anamwalira. Osangogawa ayi koma muzichipanga kukhala chizolowezi chanu chophunzira mabuku amenewa nokha. اِنْ شَآءَاللّٰه mudzapeza maphunziro ochuluka achipembedzo.

*'Amal ka ho jazbah 'ata Ya Ilahi* *Gunahon say mujh ko bacha Ya Ilahi*

*Sa'adat milay Dars-e-Faizan-e-Sunnat"* *Ki rouzana do martaba Ya Ilahi*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 102-103)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

O, Ambuye wa Mustafa! Tipatseni Taufeeq yopewa kukambirana zopanda pake.

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد



www.dawateislami.net

# Nkhani-25 za kupewa mkambirano opanda pake

## 1. Osayankhula motero mwakuti mudzafunika kupepesa nthawi ina

Munthu amene anamulandira Mtumiki Woyera, Sayyiduna Abu Ayyub Ansari رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anati munthu wina anabwera ku bwalo la Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo modzichepetsa anati: "Chonde ndipatseni uphungu waufupi." Mtumiki Woyera." Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Mukamapemphera pa Salah yanu, ndiyeno mudziyitenga ngati Salah yomaliza ya m'moyo wanu; ndipo musanene chilichonse chomwe chingakupangitseni kupepesa m'mawa; ndipo musataye mtima pa chilichonse chimene ena ali nacho." *(Musnad Imam Ahmad Bin Hanmbal, buku. 9, tsamba. 130, Hadith 23557)*

## Kufotokozera kwa magawo awiri a Hadith

Pakufotokozera gawo ili la Hadith yodalitsika 'musayankhule mwakuti mpakana mudzayenera kupepesa pambuyo pake', Sayyiduna Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه alemba kuti: "Uwu ndi uphungu wokwanira kwambiri. Ndiye kuti, nthawi zambiri khalani chete. Ngati muyenera kuyankhula, yankhulani zabwino. Musayankhule ngati mukupweteka munthu wina, chifukwa mudzayenera kupepesa pambuyo pake. Kukhala chete kumakupulumutsani ku machimo mazana ambiri, kapena tanthauzo lake ndi loti musanene chiganizo chilichonse chochimwa chomwe muyenera kulapa chifukwa cha icho." Ponena za gawo ili la Hadith 'khalani womvetsa chisoni kwambiri za zinthu zimene anthu ali

nazo m'manja mwawo', Sayyiduna Mufti Ahmad Yar Khan analemba kuti: "Osasunga chiyembekezo ndi dyera pa chuma cha wina aliyense; mtima wanu udzakhala wokhutira; simudzafunika kusangalatsa aliyense." *(Mir`aat, buku. 7, tsamba. 54)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 2. Okondedwa bambo! N'chifukwa chiyani simuyankhula?

Zananenedwa kuchokera kwa Sahabi Ibn-e-Sahabi, Sayyiduna 'Abdullah Bin 'Abbas رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُمَا kuti pamene Sayyiduna Adam عَلَیۡہِ السَّلَام anatumizidwa pa dziko, iye anadalitsidwa ndi ana ambiri. Tsiku lina ana ake onse, zidzukulu zake, komanso zidzukulu za zidzukulu zake anasonkhana mozungulira iye ndipo anayamba kuyankhula, koma iye عَلَیۡہِ السَّلَام anakhala chete ndipo sanayankhule. Anawo modzichepetsa anati, "Abambo okondedwa!

Chavuta ndi chiyani? Tikuyankhula ndipo inu mwango-khala chete." Sayyiduna Adam عَلَیۡہِ السَّلَام anati, "O ana anga! Pamene Allah Wamphamvu zonse ananditumiza kudziko lapansi kuchokera pafupi pake (Paradaiso), Iye anatenga lonjezo ili kwa ine, 'O Adam! Lankhula pang'ono mpaka pamene udzabwerere pafupi ndi ine (Paradaiso).'" *(Ayk chup so sukh (Urdu), tsamba. 5; Husn Al-simt fi Al-Samt, tsamba. 11)*

O omukonda Rasool! Tadziwano kuti Allah Wamphamvu zonse amakonda kuti kapolo azikhala chete. Choncho, m'nkhaniyi, muli chenjezo lalikulu kwa iwo amene amangoyankhula mopanda chifukwa. Allah Wamphamvu zonse atipatse gawo la 'kukhala chete' kuchokera kwa atate wathu wodala, Abul Bashar Sayyiduna Adam!



www.dawateislami.net

اٰمِيۡن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

صَلُّوۡا عَلَى الۡحَبِيۡب ! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 3. Njira yopezera kumuopa Allah Wamphamvu zonse

Sayyiduna Malik Bin Dinar رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه anati: "Sayyiduna Dawood عَلَيۡهِ السَّلَام ananena kuti, 'O anthu olungama! Bwerani! Ndikupatsani maphunziro a kuopa Allah Wamphamvu zonse. Aliyense wa inu amene amakonda kuti akhalebe ndi moyo ndi kuona ntchito zabwino, ayenera kuteteza diso lake ndi lilime lake. Sayenera kuyang'ana zoyipa kapena kunena mawu aliwonse oyipa, chifukwa Allah Wamphamvu zonse amadalitsa ma Siddiqeen (anthu a chilungamo) ndi Chifundo ndipo amawamvera nthawi yomweyo." *(Allah walon ki baatayn, buku. 2, tsamba. 547; Hilyat Al-Awliya, buku. 2, tsamba. 408, Hadith 2750)*

Abale achisilamu okondedwa! Taphunzira kuchokera munkhaniyi kuti kuti tikhale omuopa Allah Wamphamvu zonse ndikukhala olungama, tiyenera kuteteza maso athu ndi malilime athu kuchokera ku machimo komanso kuzinthu zopanda pake. Komanso, tiyenera kudziteteza ku bodza, ndi zina zotero, ndikuvomereza choonadi mpakana kalekale. Mtumiki wokondedwa wa Allah Wamphamvu zonse صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Ndithudi, Sidq [choonadi] chimatsogolera ku ntchito yabwino, ndipo ntchito yabwino imatsogolera ku Paradiso, ndipo ndithu munthu amapitiriza kuyankhula zoona mpaka kufika poti amalembedwa kuti ndi Siddiq (wokhulupirika kwambiri) pamaso pa Allah Wamphamvu zonse, ndipo ndithu Kizb (bodza) limatsogolera ku tchimo, ndipo tchimo limatsogolera ku Gahena, ndipo ndithu munthu amapitiriza kunama

mpaka kufika poti alembedwa kuti ndi Kazzaab (wabodza kwambiri) pamaso pa Allah Wamphamvu zonse.” *(Bukhari, buku. 4, tsamba. 165, Hadith 6094)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 4. Malangizo kwa lilime ali chiyimire pa Phiri la Safa

Pamene anali pa phiri la Safa, sahaba wa Mtumiki Woyera, Sayyiduna ‘Abdullah Bin Mas’ood رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ, nthawi ina anali akunena Talbiyah (لَبَّيْك اَللّٰهُمَّ لَبَّيْك) ndipo ankanena kuti: “O lilime! Yankhula zabwino, chifukwa zidzapindulitsa; ndipo khala chete pa zokambirana zoyipa, chifukwa udzapeza mtendere. (Tsata malangizo awiriwa) musanavutike ndi manyazi.” *(Ihya-ul-‘Uloom, buku. 3, tsamba. 135)*

## 5. Tsoka kwa inu!

Sahabi Ibn-e-Sahabi Sayyiduna ‘Abdullah Bin ‘Abbas رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ anati, “Iwe lilime! Tsoka kwa iwe! Yankhula zabwino, chifukwa zili ndi ubwino; ndipo leka kuyankhula zoyipa, chifukwa zili ndi mtendere." Pamene anthu anamuzungulira iye anafunsa chifukwa chake, iye anati, "Ndalandira nkhani yakuti munthu adzakhala ndi kuluza kwakukulu chifukwa cha lilime lake pa Tsiku Lachiweruzo.” *(Allah walon ki baatayn, buku. 1, tsamba. 574)*

Abale achisilamu okondedwa! Ichi ndi chowonadi kuti chisangalalo cha Allah Wamphamvu zonse chimapezeka poyankhula zabwino, ndipo aliyense amene Allah Wamphamvu zonse amakondwera naye adzapeza



www.dawateislami.net

Paradiso; ndipo Allah Wamphamvu zonse amakwiya poyankhula zoyipa, ndipo aliyense amene Allah Wamphamvu zonse amamkwiyira adzapeza chilango cha ku Gahena.

*Jahannam say hum ko bacha Ya Ilahi*

*To Jannat mayn hum ko basa Ya Ilahi*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 6. Ndimakonda kukhala chete kuposa m'mene ndimakondera kuyankhula

Sayyiduna Ibrahim Bin Basshaar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "Pamene tonse tinasonkhana nthawi ina yake, aliyense wa ife anayankhulapo china chake, koma Sayyiduna Ibrahim Bin Adham رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anakhala chete. Iye sananene chilichonse. Pamene anthu anachoka, ine ndinamuuza nkhawa yanga. Iye kenako ananena kuti, 'Kuyankhula kumawulula kupusa kwa munthu wopusa ndi nzeru za munthu wanzeru.' Ine ndinati, '(Ndiwe wanzeru) nanga bwanji sunayankhule?' Iye anati, 'Ndimakonda kukhala chete ndi kukhala ndi chisoni kuposa momwe ndimakondera kuyankhula kenako ndi kuchitsidwa manyazi.'" *(Ayk chup so sukh (Urdu), tsamba. 18; Husn Al-simt fi Al-Samt, tsamba. 31)*

سُبْحٰنَ اللّٰه! Malingaliro a anthu athu akale olungama anali okongola motani! Ndithudi, nzeru za munthu zimadziwika poyankhula. Nthawi zina zimawonekera kwa anthu kuti munthuyu alibe nzeru podziwa kuti ayenera kuyankhula malo ati, nthawi yanji, ndi chiyani. 'Kukhala chete kenako ndi kukhala odandaula' kumatanthauza kuti ndizotheka kuti



www.dawateislami.net

pokhala chete, pangakhalenso kudandaula kotero pambuyo pake kuti ngati mukanayankhula chiganizo ichi pokambirana pa nthawi inayake, zikanakhala bwino; ndipo ngati mukanayankhula zimenezo, mukanasangalala, ndi zina zotero. Mulimonse momwe zingakhalire, kudandaula pambuyo poyankhula ndi kwabwino kuposa kudandaula pokhala chete, ndipo kudandaula pambuyo pakudya ndi kwabwino kuposa kudandaula pambuyo posadya.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 7. Amuna atatu ochita zabwino a Allah Wamphamvu zonse amene anayenda pa madzi ndipo anayandama

Taba'i woyera, Sayyiduna Wahb Bin Munabbih رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, "anati, "Mu mtundu wa Bani Israel, anthu awiri olungama a Allah Wamphamvu zonse anali pa mlingo wa kupembedza moti ankayenda pamadzi. Pamene ankayenda panyanja, anaona munthu woyera amene ankayenda mumlengalenga. Anthu olungama a Allah Wamphamvu zonse amene ankayenda pamadzi anafunsa munthu woyera wa Allah Wamphamvu zonse amene ankayenda mumlengalenga kuti, 'O kapolo wa Allah! Mwafika bwanji pa mlingo umenewu?' Iye anati, 'Pamene kwinaku ndikukondwera pang'ono ndi 'dziko', ndinasunga Nafs (umunthu wamkati) kuchokera ku zilakolako ndi lilime kuchokera ku zokambirana zopanda pake, ndipo ndinakhala wotanganidwa ndi zinthu zimene Allah Wamphamvu zonse wandilamulira, ndipo ndimakhala chete nthawi zonse. Ngati ndikulumbira chilichonse mwa Allah Wamphamvu zonse, (ndikuyembekeza mu Rahmah yake kuti) Adzakwaniritsa lumbiro langa,



www.dawateislami.net

ndipo ngati ndikumupempha (chilichonse), Iye adzandidalitsa.'" *(Ayk chup so sukh (Urdu), tsamba. 22; Husn Al-simt fi Al-Samt, tsamba. 34)*

## Mtengo ku Paradaiso –Chitetezo kuchokera ku zoyipa

"اَللّٰهُ اَكْبَر"! Munthu woyera wa Allah Wamphamvu zonse amene ankayenda mumlengalenga anali ndi ubwino wa kupembedza ngakhale atakhala chete chifukwa amasunga nthawi imene ikanagwiritsidwa ntchito pokambirana zopanda pake ndipo anali ndi mwayi wopembedza Allah Wamphamvu zonse panthawi imeneyo. Ndikulakalaka kuti ifenso tinakanizira kuti chilichonse chimene titayankhule chidzakhala chothandiza pa Deen kapena dziko. Ngati sichoncho, nanga bwanji sitikuyamba kunena mawu akuti "سُبْحٰنَ اللّٰـه" "سُبْحٰنَ اللّٰـه" ndi cholinga chofuna kukondweretsa Allah Wamphamvu zonse, chifukwa nthawi iliyonse imene tikunena "سُبْحٰنَ اللّٰـه", mtengo umadzabzalidwa ku Paradiso mwa chifundo cha Allah Wamphamvu zonse. Ndipo palinso phindu lambiri ponena mawu akuti سُبْحٰنَ اللّٰـه mochuluka padziko lapansi. Mtsogoleri wa mamiliyoni achi Shafa'i, Sayyiduna Imam Shaafi'i رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, anati, "Sindinaonepo chilichonse chothandiza kuposa Tasbih kuti ndikhale otetezeka ku matenda." *(Hilyat Al-Awliya, buku. 9, tsamba. 145, mawu nambala. 1344)*

**Dziwani kuti:** Tasbih imatanthauza kumutamanda Allah Wamphamvu zonse, monga ponena mawu akuti "سُبْحٰنَ الله".

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 8. Ngati china chake chayikidwa mkamwa

Sayyiduna Ibrahim Bin Bashar رَحْمَةُاللّٰهِعَلَيْه anati, "Ndinakhala ndi Sayyiduna Ibrahim Bin Adham رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه kwa zaka zoposa zisanu ndi chimodzi. Iye رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه nthawi zambiri ankakhala chete ndipo sanatifunsepo chilichonse, koma m'malo mwake ife tinkayankhulana naye. Tinkaona ngati chinachake chinayikidwa m'kamwa mwake ndipo analetsedwa kuchokera ku kuyankhula." *('Uyoon Al-Hikayaat (Urdu), buku. 1, tsamba. 204; 'Uyoon Al-Hikayaat, tsamba. 129)*

## Ndikulakalaka panakakhala chitseko cha chitsulo

"سُبْحٰنَ اللّٰه"! Malingaliro a anthu athu akale olungama anali odabwitsa kwambiri! Ndithudi, iwo anali chitsanzo cha makhalidwe abwino, koma ife ndi odzazidwa ndi zolakwa. Ndi kofunikanso kwambiri kudziteteza ku misonkhano yosafunikira kuti lilime litetezeke. Sahaba wa Mtumiki Woyera, Sayyiduna Sa'd Bin Abi Waqqas رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ ankanena kuti: "Ndikulumbira mwa Allah Wamphamvu zonse! Ndinakakonda kuti pakhale chitseko chachitsulo pakati pa anthu ndi ine. Palibe amene ayenera kuyankhula nane ndipo inenso sindiyenera kuyankhula ndi aliyense mpaka nditakumana ndi Allah Wamphamvu zonse." *(Kitab Al-'Uzlah li ibn-e-Abi Al-dunya ma' Mousu'ah, buku. 6, tsamba. 511, mawu nambala. 57)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 9. Kulamulira lilime lake

Anafunsidwa munthu wina woyera wa Allah Wamphamvu zonse kuti Sayyiduna Ahnaf رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anakhala bwanji mtsogoleri wanu ngakhale kuti sanali wamkulu pakati panu kapena wolemera kwambiri. Munthu



www.dawateislami.net

woyera wa Allah Wamphamvu zonse anati, "Iye anadalitsidwa ndi utsogoleri umenewu chifukwa chotha kulamulira lilime lake." *(Al-Mustatraf, buku. 1, tsamba. 147)*

## Allah Wamphamvu zonse ndi yemwe amapereka chipambano

O omukonda Rasool! Ndithudi, aliyense amene amalamulira lilime lake ndi mfumu ya 'lilime lake ngati mkaidi', koma adzafunika kugonjetsa asilikali a Nafs ndi Satana kuti apeze ufumu umenewu, ndipo ngakhale kuti ndi ntchito yovuta, komabe ngati chidwi chili chenicheni, kupambana ndi kotheka mwa chifundo cha Allah Wamphamvu zonse ndi kupereka kwa Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Khama liyenera kupitirira. Mwambi wokongola kwambiri wachiarabu ndi uwu: "اَلسَّعْیُ مِنِّیْ وَالْاِتْمَامُ مِنَ اللہ" kutanthauza kuti, 'khama lokha ndi langa, ndipo kukwaniritsidwa kwa ntchito, kutanthauza kupambana ndi kochokera kwa Allah Wamphamvu zonse.'

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب!    صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 10. Ophunzira anayi, zoyankhula zinayi

Sayyiduna Abdullah Bin Mubarak رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: Pamene akatswiri ophunzira anayi odala anasonkhana kwa mfumu, mfumuyo inawauza kuti, 'Nonse nenani china chake chachidule koma chokwanira.' Mmodzi mwa akatswiri ophunzirawo anati, 'Ubwino wa maphunziro a munthu wophunzira ndi kukhala chete.' Winayo anati, 'Chinthu chothandiza kwambiri kwa munthu ndi chakuti ayenera kudziwa ulemerero wake ndi kuzama kwa nzeru zake, ndipo ayenera kuyankhula molingana ndi zimenezo.' Wachitatu anati, 'Munthu wosamala kwambiri ndi amene sakhutitsidwa ndi madalitso omwe alipo kapena kuwakhulupirira kapena



www.dawateislami.net

kupirira pa zovuta zilizonse za zimenezo.' Wachinayi anati, 'Palibe chinthu chomwe chimapatsa thupi mpumulo kuposa kukhala wokhutitsidwa ndi chikhonzero ndikukhala okhutira.' *(Ayk chup so such (Urdu), tsamba. 16)*

مَا شَآءَ الله! Mawu anayi onsewa ndi achidule koma okwanira ndipo ali ndi mfundo za mtengo wapatali za Madani. Mwambi wachiarabu uli motere: "خَيْرُ الْكَلَامِ مَا قَلَّ وَدَلَّ" *Kutanthauza kuti, "Mawu abwino ndi amene ali achidule komanso operekedwa ndi mkangano."*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 11. Mafumu anayi, mikambirano inayi

Sayyiduna Abu Bakr Bin 'Ayyash رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Mafumu anayi ochokera ku Persia, Roma, Hind, ndi China anasonkhana pamalo ena, ndipo anayiwo anayankhula zinthu zinayi zomwe zinali ngati mivi inayi yotuluka mu uta umodzi. Mmodzi anati, 'Ine ndimatha kudziletsa pa zoyankhulidwa kuposa zosayankhulidwa.' Wachiwiri anati, 'Zomwe ndayankhula kuchokera pakamwa panga ndi zomwe zimandilamulira, ndipo ine ndine wolamulira pa zomwe sindinayankhule.' Wachitatu anati, 'Sindinachititsidwepo manyazi ndi zomwe sindinayankhule, koma ndimachititsidwadi manyazi ndi zomwe ndayankhula.' Wachinayi anati, 'Ndimadabwa ndi woyankhula kuti ngati zomwezo zibwerera kwa iye, zidzamuvulaza; ndipo ngati sizingabwerera, sizidzamupindulitsa iye.' *(Ayk chup so sukh (Urdu), tsamba. 18; Husn Al-simt fi Al-Samt, tsamba. 30)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد



www.dawateislami.net

## 12. Iye sanaseke kwa zaka 40

Taba'i woyera, Sayyiduna Hasan Basri sanaseke kwa zaka makumi anayi (40). Ngati ankaoneka atakhala pansi, zinkaoneka ngati kuti anali mkaidi amene wabweretsedwa kuti adulidwe mutu. Ndipo pamene ankayankhula, njira yake inali ngati kuti akufotokoza za Tsiku Lachimaliziro kwinaku akuona zonse. Ndipo pamene ankakhala chete, zinkaoneka ngati moto unali kuyaka m'maso mwake. Pamene anafunsidwa chifukwa chokhala wachisoni kwambiri ndi woopa, iye anati: "Ndimakhala ndi mantha kuti ngati Allah Wamphamvu zonse ayang'ana zina mwa ntchito zanga zosakondedwa, kutsitsa mkwiyo pa ine, ndipo ndikunena kuti, 'Pita! Sindikukhulul ukira iwe,' ndiye kuti zidzakhala bwanji kwa ine?" *(Ihya-ul-'Uloom (Urdu), buku. 4, tsamba. 555-556; Ihya-ul-'Uloom, buku. 4, 231)*

## Ubwino omuopa Allah Wamphamvu zonse

"اَللّٰهُ اَكْبَر"! Mu nkhaniyi mmene khalifah wa Sayyiduna Maula Ali Sher-e-Khuda رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ, Taba'i wolemekezeka ndi munthu woyera wa Allah Wamphamvu zonse, Sayyiduna Hasan Basri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَیْه amkakhala ndi mantha chifukwa choopa Allah Wamphamvu zonse, muli mfundo za Madani zambiri zophunzitsa kwa ife ochimwa. Pali ubwino wambiri womuopa Allah Wamphamvu zonse. Allah Wamphamvu zonse wanena mu vesi 12, Surah Mulk, Gawo 29:

اِنَّ الَّذِیْنَ یَخْشَوْنَ رَبَّهُمْ بِالْغَیْبِ لَهُمْ مَّغْفِرَةٌ وَّ اَجْرٌ كَبِیْرٌ ﴿۱۲﴾

*Ndithudi, amene amaopa Mbuye wawo mopanda kumuona, kwa iwo kuli chikhululuko ndi mphotho yaikulu.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 29, Surah Al-Mulk, vesi 12)*



www.dawateislami.net

## Hadith Yolemekezeka yowonetsa kuti kumuopa Allah Wamphamvu zonse kumaonjezera chakudya komanso zaka

Zinanenedwa kuchokera kwa khalifah wachinayi wa Asilamu, Sayyiduna Ali رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ kuti Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Aliyense amene akufuna kuwonjezeka kwa zaka, kuwonjezeka kwa chakudya, ndi chitetezo ku imfa yoyipa, ayenera kuopa Allah Wamphamvu zonse ndi kuwachitira abale zabwino."

*(Musnad Ahmad Bin Hanmbal, buku. 1, tsamba. 302, Hadith 1212)*

## Kumuopa Allah Wamphamvu zonse kumatanthauza chiyani?

Abale achisilamu okondedwa! Kuopa Allah Wamphamvu Zonse ndi dzina la dongosolo lobisika la Allah Wamphamvu Zonse, Iye kukhala Wodziyimira payekha, kusakondwa Kwake, chilango Chake, zowawa zoperekedwa ndi Iye, mkwiyo Wake ndi kukhala ndi mantha a chiwonongeko cha Iman chifukwa cha mkwiyo umenewu. Ndikulakalaka tikanakhala odalitsika ndi kuopa Allah Wamphamvu Zonse m'njira yake yeniyeni.

*Zamanay ka dar mayray dil say mita kar*

*To kar khouf apna 'ata Ya Ilahi*

*Tayray khouf say tayray dar say hamaysha*

*Mayn thar thar rahon kanpta Ya Ilahi*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب ! صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد



www.dawateislami.net

## 13. Anthu amene amayankhula kenako ndikukhala chete

Sayyiduna Abu Hatim رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, “Amuna awiri anapeza maphunziro. Mmodzi anakhala chete ndipo winayo anayankhula. Choncho, yemwe anayankhula analembera yemwe anakhala chete, ‘Wapindura chiyani kuchokera ku maphunziro ako popeza palibe chida chabwino kuposa lilime kuti upeze chakudya.’ Yemwe anakhala chete analembera yemwe anayankhula kuti, ‘Ubwino wanji wapeza kuchokera ku maphunziro ako popeza ndikukhulupirira kuti lilime liyenera kumangidwa.’” *(Husn Al-Simt, tsamba. 44)*

Ndithudi, pokhala mkati mwa malamulo a Shariah, palibe vuto poyankhula zabwino. Ndikofunikira kupewa zokambirana zoyipa, ndipo tiyeneranso kudzitchinjiriza ku zokambirana zopanda pake komanso zosapindulitsa. Kunama pamene mukupeza zofunika pa moyo ndi tchimo, ndipo zokambirana zopanda pake sizabwinso.

## 14. Lingaliro la kukhala chete cholinga chofuna kubisa zimene waluza

Wochita malonda analuza ndalama zokwana madinar 1,000. Anamuuza mwana wake kuti, “Taona, usauze aliyense za kuluza kumeneku.” Mwanayo anati, “Atate okondedwa! Ili ndi lamulo lanu, choncho sindidzauza aliyense za zimenezo. Komabe, ndikufuna kuti mundiuze ubwino (wa kukhala chete kumeneku) chifukwa chachinsinsi cha kubisa kuluza kumeneku.” Atate anati, “Kukhala chete n’kofunika, chifukwa sitiyenera kukumana ndi mavuto awiri (nthawi imodzi). Ndiko kuti, limodzi ndi kuluza kwa ndalama ndipo lina ndi lakuti anansi (otsutsana

nafe) amasangalala ndi kuluza kwathu ndipo amatinyoza.” *(Gulistan-e-Sa’di, tsamba. 115)*

## Kusangalala pa kuluza kwa Msilamu

O omukonda Rasool! Taphunzira kuchokera mu nkhaniyi kuti ngati taluza chilichonse, mu kukhala chete muli mtendere m’malo mowululira aliyense mopanda cholinga. Ndizotheka kuti tikamawulula, munthu amadziwa ndipo mosadziwa amalowetsedwa mu zoyipa za kukondwera ndi kuluza kwathu. Kumbukirani! Kukondwera ndi matenda a Msilamu wina kapena vuto kapena kuluza kwake kumatchedwa Shamatat, ndipo Shamatat ndi yoletsedwa mu Shari’ah. Zafotokozedwa kuchokera kwa Sayyiduna Wasilah رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ kuti Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, “Usamachite Shamatat pa m’bale wako. Ndiye kuti, usakondwere ndi vuto lake, chifukwa Allah Wamphamvu zonse adzamuchitira chifundo ndipo adzakulowetsa iwe mu zimenezi.”

*(Tirmizi, buku. 4, tsamba. 227, Hadith 2514)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب!　　صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 15. Kukhala chete ndi chizolowezi cha anthu anzeru

Mnyamata wanzeru, amene anali ndi makhalidwe ambiri, ankatenga nawo mbali m’misonkhano ya anthu ophunzira ndipo ankadziletsa kuyankhula. Atate ake tsiku lina anati kwa iye, “Mwanawe! Chilichonse chimene ukudziwa, chinene.” Kenako mnyamatayo anati, “Ndimakhala ndi mantha kuti mwina anthu angandifunse chinthu chimene sindikudziwa



www.dawateislami.net

ndipo mwanjira imeneyi ndidzayenera kuchita manyazi.” *(Gulistan-e-Sa’di, tsamba. 116)*

## Kunena lamulo lolakwika

O omukonda Rasool! Taphunzira kuchokera m'nkhaniyi kuti tikakhala ndi anthu ophunzira, tiyenera kukhala chete, اِنْ شَآءَاللّٰه chifukwa tidzatha kumvetsera ndi kumvetsetsa zokambirana zawo zabwino. Choyamba, ndi zotheka kuti tilibe kuthekera kophunzira maphunziro ndi kumvetsetsa polankhula nthawi zonse, ndipo chachiwiri ndi zotheka kuti tafunsidwa funso ndipo sitingathe kuyankha. Kumbukirani kuti pamene sitikudziwa yankho lolondola la funso lililonse, sitiyenera kupereka yankho lolakwika mwadala, makamaka mayankho a malamulo a Shar'i sayenera kuperekedwa pokhapokha ngati pali chidziwitso chokwanira. Kunena lamulo lililonse la Shar'i chifukwa cha kusamvera kwanu ndi kungochita juga ndi moyo wanu wa tsiku lachimaliziro. Allah Wamphamvu zonse wanena mu vesi 68, Surah Yunus, Gawo 11 kuti:

اَتَقُوْلُوْنَ عَلَى اللّٰهِ مَا لَا تَعْلَمُوْنَ ﴿۶۸﴾

*Kodi mukunena zinthu zoterezi zotsutsana ndi Allah zomwe simukuzidziwa?'*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 11, Surah Younus, vesi 68)*

